2025
EPU - JUN

Vol. 101, No. 2

Maphunziro AmBaibulo Apa Sabata

Chigawo cha akulu



GAWO LACHIWIRI

# *Uthenga Wabwino* Malinga ndi Yohane

Mbusa wabwino amateteza ndi kutsogolera nkhosa zimene ziri pansi paubusa wake mosamalitsa

Ziri mkati

1. Yesu, Mkate Wa Moyo………………………................................................................ 5
2. Chibvuto Ku Galileya……...…………………………………………….. …10
3. Yesu Pa Phwando La Misasa……………………………………………… 15
4. Palibe Amene Anayankhula Monga Munthu Uyu………………….............. 20
5. "Ngakhale Inenso Sindikutsutsa Iwe"………………..................................26
6. Yesu, Kuunika Kwa Dziko Lapansi…………………………………….. ….31
7. Kuunika Kokanidwa – Kapena Kowunikiridwa?………………………..........36
8. Yesu Ndi Abrahamu……………………………………………………... ….41
9. Yesu Ndi Munthu Wakhungu……………………………………………… 47
10. Kukumana Ndi Khungu Lauzimu…………………………………………….. 52
11. Yesu, Mbusa Wabwino……………………………………………………. …..57
12. Yesu Ndi Lazalo………………………….................................................. 62
13. Kuuka Ndi Moyo……………………………………………………………. 67

Maphunziro a Baibulo apa Sabata, phunziro la tsiku ndi tsiku, lazikidwa pa Baibulo ndi Mzimu wachinenero basi popanda ndemanga zowonjezera. Mawu andemanga ndi achidule momwe mungathere kupereka malingaliro achidule, achindunji. Dzikutiro [ ] zamaperekedwa nthawi zina kuti atsimikizire kumveka bwino, nkhani yoyenera, ndi kuwerenga kosalala. Kuphunzira kopitilira kupyolera m`mene mwachokera ndemanda kumalimbikitsidwa kwambiri

Zitsanzo: Adobe Stock pa p. 25, 72; Map Resources on pp. 4, 51, 72; Sermonview pachikhutiro cha patsogolo

Copyright © 2025 by the Seventh Day Adventist Reform General Conference, Chigawo cha Sabata Sukulu, 5240 Hollins Road, Roanoke, Virginia 24019, USA.

Telefoni: 1-540-362-1800 • Webusaiti: www.sdarm.org • Imelo: info@sdarm.org

Kumalawi: SDARM Malawi Mission P.O. Box 200069 Lilongwe 2.

Foni: +265 999 701 423, +265 884 288 535

Maphunziro a Baibulo pa Sabata (USPS 005-118), Vol. 101, No. 2, Apulo – Juni 2025. Lofalitsidwa pa kotala ndi Seventh Day Adventist Reform General Conference, chigawo cha Sabata Sukulu Kusindikizidwa, ndi kugawidwa ndi Reformation Herald Publishing Association, 5240 Hollins Road, Roanoke, Virginia 24019–5048, U.S.A. Malipiro anthawi ndi nthawi ku Roanoke, Virginia 24022-9993.

**U.S.A. ndi Canada**

Lumikizanani: Telefoni 1-540-366-9400 • Webusaiti: www.reformationherald. com • Imelo: info@reformationherald.org

Kulembetsa pachaka ku U.S.A.: U.S. $22.00. Kusindikiza kwakukulu $33.00. Mayiko $21.00 kuphatikiza kutumiza. Kusindikiza kwakukulu kwapadziko lonse $31.00 kuphatikiza kutumiza. Kope limodzi $6.00. Kusindikiza kwakukulu $9.00. Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira (mu ndalama zaku U.S. zokha) pa keyala ali pansipa. Mitengo zitha kusintha popanda chidziwitso. POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata,

**South Africa**

Lumikizanani: Telefoni & Fax 27-011-336-7064 • Webusaiti: www.sdarm sa.org.

za •Imelo: admin@sdarm sa.org.za Kulembetsa kwapachaka mu South Africa: R120-00 (kope limodzi R35-00).

Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira ku adilesi ili pansipa.

POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata, P. O. Box 7950, Johannesburg 2000, South Africa

**Malawi**

Lumikizanani: Telefoni +26 999 701 423, +265 884 288 535

za•Imelo: sdarmmalawi@yahoo.com Kulembetsa kwapachaka Malawi: MK 2000 (kope limodzi MK 500).

Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira ku adilesi ili pansipa.

POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata, P. O. Box 20069, Lilongwe 2. Malawi

**MAWU OTSOGOLERA**

Zolembela za uthenga wabwino molingana ndi Yohane zinalembedwa patsogolo pa mabuku ena atatu authenga wabwino (wochedwa ndandanda wa mauthenga abwino), koma mkatikati mwa dzaka 100 zoyambilira. Muzaka za mma 1900, otsutsa Baibulo anayesela kuti akane kuti bukhuli linalembedwa isanafike AD 150, chotelo kuyetsera kuchosa choona choti mtumwi Yohane ndiye amene analemba bukuli. Otsutsawa amanena kutinso mubuku limeneli mumaonekela mzeru za otumbatumba a Gnostic Filosofe ndipo chotelo sizingatheke kuti lilembedwe isanafike nthawi imene mzeru zimenezi zinakhala chiopsezo chachikulu kuchikhulupiriro. (Gnosticism ndi mzeru za filosofe ndi dongosolo la chipembezo lakagulu kochepa kakalekale kamene kamanena kuti chiziwitso osati chikhulupiliro ndiye mfundo yofunikila kuchipulumutso.)Lingaliro losokoneza limeneli kwanthawi yaitali lakhala likukanidwa.

Mosiyana ndi zimenezi, maumboni a ponseponse akuchitira umboni za kukhalapo kwa bukhu lachinayi la uthenga wabwino ndi kulemekezedwa kwakukulu komwe anthu akhala alinako ku bukhuli ngakhale muzaka za mma A.D. 115. Umodzi mwa maumboni amenewo anabwera kudzera mu kupedzeka kwa chidutswa cha papyrusi, kokhala ndi mavesi ochepa a Yohane (chaputala 16, vesi 31-33, 37, 38), amene amadziwika ndi dzina lotiRylands Papyrus amene amachedwa P52, amene analembedwa A.D 125. Kachiduswa kameneka, kamene kanapezeka ku dziko la Egupto kumayambiriro kwa zaka za mma 200, amatengedwa ngati umboni wogwirika wa kufalikira ndi ukalekale wa bukhu lachinayi la uthenga wabwino. Ophunzira ochuka wa chipangano chatsopano Adolph Deissmann akutsimikizira kuti:

“Misuso yambiri yokhuzana ndi kupezeka kochedwa kwa bukhu la uthenga wabwino wa Yohane mwachangu zizafota ndi kuuma monga mtengo munyumba yotentha kwambiri. Ife kuno ku Rylands Papyrus tili ndi zolembera zina zimene ndi umboni kuti Uthenga wabwino wa Yohane sunayambe mu zaka za mma 200, koma kuti zolembera zimenezi zinafika kale ku Egypto. Kulembedwa kwa Uthenga wabwino chotero kukuyenera kuikidwa muzaka zoyambirira zambuyo.” – Deutsche Allgemeine Zeitung, Dec. 3, 1935.

Zolembela za Yohane sizinangotumikila kokha kucholinga chapadela pakati pa akhristu oyambilira; zakhala zikubweletsa chitsogozo cha uzimu, thandizo, ndichilimbikitso kwa otsatila a Khristu, okhala pansi pazochitika zosiyanasiyana kupyola mumibadomibado.

Ambuye “ali ndi kuunika kumene kuli kwatsopano kwa ife, komabe ndikwamtengo wapatali kwambili, kuunika kwakalekale koti kuwalire kuchokela kumawu achoonadi. Tili ndi milezo chabe yakuunika kumene kuyenela kubwela pa ife. Ife sitikugwiritsa ntchito kwambiri kuunika kumene Ambuye anatipatsa ife kale, ndipo pakutelo ife tikulephera kulandira kuunika koonjezera; ife sitikuyenda muukunika kumene kunapelekedwa kale kwa ife.

“Timazichula ife tokha kuti ndiife anthu osunga malamulo, koma sitikuzindikila kuya ndikukula kwa mfundo za lamulo la Mulungu; Ife sitimazindikila khalidwe lake lopatulika. Ambiri amene amazinena kukhala aphuzintsi achoonadi, alibe chiziwitso chenicheni cha zimene iwo akuchita Mukuphuzitsa lamulo laMulungu, chifuka choti iwo alibe chiziwitso cha moyo

cha Ambuye Yesu Khristu.”-Selected messages,BK. 1, pp. 401,402.

Tilole kuti kuphunzira kopitilira kwa uthenga uwu wabwino zitithandize ife kumuziwa Yesu bwino!

**Agawo la sabata sukulu aku General Comference**




## Zomangira Tcharichi ku Prokhorovka, Russia

Russia, potengela malo, ndi dziko lalikulu kwambili padziko lonse lapansi, liri ndi malo okwanila 6,612,073.2 sikweya mailosi (17,125,191km) lili ndi chiwelengelo cha anthu okwana 147,000,000. Anthu ochokela mumaiko oposa 180 amakhala mudziko lalikulu limeneli. Chifukwa cha ichi, Iwo amasatila zikhulupiliro za zipembezo zosiyanasiyana. Chimene chilli ndi anthu kwambili ndi chipembezo chochedwa Russsian Orthodox (41.1%), kutsatidwa ndi zikhulupiliro zina zachikhristu (6.3%),Chisilamu(6.5%), Neopagans ndi Tengrist (1.2%), Buddhism(1.22%),Osakhulupilira(25.2%),Anthu osakhulupilira kuti kuli Mulungu(13%),ndi ena osala oti Sali pa mpingo wina ulionse.

Chiyambileni SDARM, uthenga wabwino wosatha wakhala ukukula kuno pansi pa zochitikachitika zovuta kwambili. Ambili mwa okhulupilira akhala akusautsika ndi zitsautso zazikulu kwambiri-ndipo ena alalikila za mombolo opachikidwa ndikuukitsidwa ndikutaya miyoyo yawo.

Kumamaliziro kwa 1990 mlaliki wauthenga wabwino ndi mkadzi wake anasamukila mudela lapakati ladziko la Russia ndicholinga chopititsa patsogolo ntchito ya Uthenga wabwino. Monga chotsatila cha kuyetsetsa kwawo ndi mapemphero awo, gulu la okhulupilira linakonzedwa. Koma iwo analibe malo okomanilana ndi kupemphera. Mapeto ake, muchaka cha 2006 iwo anapeza nyumba yaing'ono pamalo ena mudela la Prokhorovka, dela lapatikati lotukuka lantchito za utsogoleri laboma la Prokhorovsky mu Belgorod Oblast-dela la zaulimi limene limalima zambewu, mizimbe, mpendazuwa, ndizipatso mmbali mwa msinje wochedwa PSYOL kummawa kwa mzinda wa Kursk, mmene uli ndi migodi yaikulu kwambili ya Iron.

Ife tikuona mwachindunji zanja la Mulungu likugwira ntchito pamene Iye mozizwizwitsa anachotsa zochinga zambiri ndikudalitsa kugula kwa nyumba imeneyi.Ntchito mudela limeneli yakhala ikupitilira kukula, Ndipo sipanatenge nthawi kuti nyumba ikhale yochepa kwambiri kuti ikwanire kukhalamo anthu onse opembeza Mulungu. Zaka zochepa zapitazo, tinalandila chilolezo chochokela kwa atsogoleri aboma ndikuyamba kumanga nyumba yopempherera. Abale anapeleka thandizo ndikugwira ntchito mwakhama, Koma kuti timalidze ntchitoyi tikusowa thandizo loolowa manja laanthu kudziko lonse lapansi amene amamukonda Ambuye. Kumalidza kwa ntchito imeneyi kudzapeleka mwayi wakupititsa patsogolo ntchito ya uthenga wabwino mmadela odzungulira, monga chidzindikilo chakuunika mukufalitsa uthenga womalidza wachipulumutso. Tilole Ambuye kuti adalitse wina aliyense amene mtima wake ndiokonzeka kuthandiza kupita patsogolo kwa choonadi chalero!

**Abale ndi Alongo anu kuchokela kumpingo wa Prokhorovka ndi Unioni ya Russia**

**SABATA, EPULO 5, 2025**

**PHUNZIRO 1**

# YESU, MKATE WA MOYO

**VESI LOLOWEZA: "Yesu anati kwa iwo, Ine ndine mkate wa moyo; iye amene adza kwa Ine sadzamva njala, ndi iye amene akhulupilira Ine sadzamva ludzu nthawi zonse" (Yohane 6:35).**

**Zowelenga zoonjezera: Thoughts From the Mount of Blessing, pp. 18-21.**

**"Timadya thupi la Khristu . . . pamene tigwira zolimba pa Iye mwa chikhulupiliro monga mpulumutsi wathu."—The SDA Bible Commentary [E. G. White Comments], vol. 5, p. 1135.**

## 1. CANGU CHOFUNA KUTCHUKA

**Loyamba, Marichi 30**

**a. Chitatha kuchitika chozizwitsa cha mikate, kodi anthu ambiri anakhala ndichikhulupiliro chotani? Yohane 6:14. Kodi amkafunitsitsa kuchita chiyani? Yohane 6:15 (gawo loyamba).**

---

"Tsiku lonse chikhulupiliro chinalimbikitsika. Mchitidwe womalizira umenewo unali chitsimikizo choti Mpulumutsi woyemebekezeredwa kwa nthawi yayitali ali pakati pawo. Ziyembekezo zonse za anthu zinakwera pamwamba kwambiri. Uyu ndiye amene azamupanga Yudeya kukhala paradizo wapadziko lapansi, dziko loyenda mkaka ndi uchi. Iye akhonza kukukhutiritsa khumbo lilironse. Iye angathe kthyola mphamvu za Aroma odanidwa. Iye angathe kupulumutsa Yuda ndi Yerusalemu. Iye angathe kuchiritsa Asilikali ovulazidwa mu nkhondo. Iye akhonza kupereka chakudya kwa khamu lonse la nkhondo. Iye akhonza kugonjetsa amitundu, ndi kupereka kwa Irayeli ulamuliro omwe wakhala ukufunidwa kwa nthawi yayitali.

"Mwa changu chawo, anthu anali okonzeka nthawi yomweyo kumuveka Iye ufumu. Iwo anawona kuti Iye sachita kuyesetsa kulikonse kuti akope chidwi kapena ulemu wa kwa Iye mwini. Mwa ichi Iye anali wosiyana kwambiri ndi Ansembe ndi Olamulira, ndipo amaopa kuti Iye sadzaumiliza konse ndi kunena kuti atenge mpando wachifumu wa Davide. Atatha kufunsana pamodzi, adagwirizana kuti amugwire Iye mwa mphamvu, ndi kumutchula Iye kuti ndi Mfumu ya Israeli. Ophunzira adagwirizana ndi khamu la anthu ponena za mbuye wao kukhala wolowa woyenera kukhalapo pa mpando wa chifumu wa Davide. Iwo amati, chifukwa cha kudzichepetsa kwa Khristu, kudamupangitsa Iye kukana ulemu oterewo. Bola anthu akweze mpulumutsi wawo. Kuti Ansembe odzikuza ndi Olamilira akakamizidwe kumulemekeza Iye amene wabwera atabvekedwa ndi ulamuliro wa Mulungu."—*The Desire of Ages*, pp. 377, 378.

## 2. KUZIZILITSA CHANGU CHOLAKWIKA

**Lachiwiri, Marichi 31**

**a. Kodi Yesu anachita chiyani kuti alepheretse anthuwa ndi ophunzira kuti akwaniritse zolinga zawo kuti amuike Iye pampando wachifumu wapadziko lapansi? Yohane 6:15.**

---

---

"[Ophunzirawo ndi khamulo] mwakhama anakonza zakuti akwaniritse cholinga chawo; koma Yesu akuwona zomwe zikuyendayenda. Ngakhale tsopano ansembe ndi olamulira akusaka moyo wake.Iwo akumuneneza Iye za kuchotsa anthu kwa iwo.Chipolowe ndi kuukira kutha kuchitika potsatira lingaliro la kumuika Iye pa mpando wa chifumu, ndipo nchito ya ufumu wauzimu isokonezedwa. Popanda kuchedwachedwa lingaliroli likuyenera kuimitsidwa. Anaitana ophunzira Ake, nawalamulira kuti atenge bwato ndikubwerera nthawi yomweyo kupita ku Kapernao, ndikumusiya kuti abalalitse anthu.

"Mbuyo monsemu sanakhalepo ndi lamulo lochokera kwa Khristu lomwe limawoneka losatheka kulikwaniritsa. Ophunzirawo anali atayembekezera kwa nthawi yaitali mgwirizano wamphamvu wotere kuti ayike Yesu pampando wachifumu; Iwo sanathe kupirira lingaliro loti khumbo lonseli lithetsedwa. Ambiri omwe anali kusonkhana kuti asunge paska anali ndi nkhawa kuti awone mneneri watsopanoyo. Kwa otsatira ake izi zidawoneka ngati mwayi waukulu wakukhazikitsa Mbuye wawo wokondedwa pa mpando wachifumu wa Israeli. Mukukula kwa khumbo latsopanoli chinali chovuta kuti achoke paokha, ndikusiya Yesu yekha pagombe lopanda malo okhala lija. Iwo adatsutsana ndi chikonzerochi; Koma tsopano Yesu analankhula ndi ulamuliro womwe mbuyo monse sanayambe waugwiritsa nchito kwa iwo. Iwo anadziwa kuti kutsutsa kopitirira mbali yawo kukhala kopanda phindu, ndipo mwa kachetechete iwo anatembenuka ndikumapita kunyanja." —***The Desire of Ages, p. 378***

**b. Tsiku lotsatira chitatha kuchitika chozizwitsa, kodi ndi chiyani chimene anthu anachita? Yohane 6: 22-25.**

---

---

"Chozizwa cha mikate chinafalitsidwa pafupi ndi patali, ndipo mmamawa kwambiri wa tsiku lotsatira anthu ambiri anabwera ku Betsaida kuti azawone Yesu. Iwo adabwera mwa unyinji, kudzera pa ntunda ndi pa nyanja. Iwo amene anali atamusiya usiku wapitawo, akuyembekezera kuti akamupezabe ali pomwepo; popeza padalibe bwato lomwe angagwiritse nchito kuti apite tsidya linalo. Koma kufunafuna kwawo kunali kopanda phindu, ndipo ambiri anabwerera ku Kapernao, napitiriza kumufunafuna Iye.

"Munthawi imeneyi Iye anali atafika ku Genessarete, pambuyo pa tsiku limodzi chabe. Mwachangu pamene zinangodziwika kuti wafika, anthuwa 'adathamangira dera lonselo nayamba kunyamula anthu odwala pa akama ao, kufika nao kumene anamva kuti analiko Iye.' Maliko 6:55."—***Ibid., pp.383, 384***

**a. Kodi ndi uthenga wachindunji komabe ozusa malingaliro otani umene Yesu anaupereka ku khamu la anthu? Yohane 6:26, 27.**

"Yesu sanakhutitse khumbo lawo. Iye mokhumudwa anati, 'Mundifuna Ine, si chifukwa munaona zizindikiro, koma chifukwa munadya mkate, nimunakhuta.'

Iwo samamufunafuna iye ndi zolinga zoyenera; koma chifukwa choti anadyetsedwa, iwo amayembekezerabe kulandira zinthu zakanthawi kudzera mukulumikizana ndi Iye. Mpulumutsi anawapempha iwo kuti, 'Gwirani nchito si chifukwa chacakudya chimene chitayika koma cha chakudya chimene chitsalira ku moyo wosatha.' Musamangofunafuna kungokhala ndi mwayi woti mupindule zinthu zakuthupi. Chisakhale cholinga chanu chachikulu kupedza zinthu za moyo uno womwe tikukhalawu basi, koma funafunani chakudya cha uzimu, inde nzeru zimene zingapirire kufikira ku moyo wosatha."—***The Desire of Ages, p. 384***

**b. Kodi ndi funso lanji limene Ayuda anamufunsa Yesu lokhudzana ndi ntchito za Mulungu? Yohane 6:28. Fotokozani yankho limene Ambuye adapereka. Yohane 6:29.**

"Kwa kamphindi chidwi cha omvetsera chinazutsidwa. Iwo anati, 'Tichite chiyani, kuti tichite ntchito za Mulungu?' Iwo anali akugwira ntchito zambiri komanso zolemetsa kuti azidziyamikira iwo okha kwa Mulungu; Ndipo anali okonzeka kumva mwambo watsopano womwe kudzera mu iwo iwo atha kupedza kuyenera kwakukulu. Funso lawo limatanthauza kuti, kodi ife tidzatani kuti tikhale oyenera kumwamba? Kodi ndi mtengo wanji womwe ife tikufunikira kulipira ndi cholinga choti tidzapeze moyo umene ukubwerawo?

"'Yesu adayankha nati kwa iwo, ntchito ya Mulungu ndi iyi, kuti mukhulupirire Iyeyo amene Iye adamutuma.' Mtengo wa kumwamba ndi Yesu. Njira yopita kumwamba ndiyo kudzera mwa chikhulupiriro mwa 'Mwanawankhosa wa Mulungu, amene achotsa tchimo la dziko lapansi.' Yohane 1:29." — ***Ibid., p. 385***

"Kulapa ndiko kutembenuka kuchoka ku undekha kupita kwa Khristu; Ndipo pamene Ife tamulandira Khristu kuti kudzera mu chikhulupiriro Iye akhoza kukhala moyo wake mwa ife, ntchito zabwino zidzawonekera." —***Thoughts From the Mount of Blessings,* p. 87.**

"Ambuye athandize anthu ake kuti azindikire kuti pali ntchito yofunika kuti ichitidwe. . .. Mnyumba, mu mpingo, komanso mdziko lapansi iwo akuyenera kugwira ntchito ntchito za Khristu. Iwo sanasiyidwe kuti agwire ntchitozi okha. Angelo ndi owathandiza awo. Ndipo Kristu ndiye mthandizi wawo."— ***Testimonies for the Church,* vol. 8, p. 18.**

**a. Kodi ndi chizindikiro chanji chimene Ayuda amafuna nanga kodi ndi choona chanji cha mumbiri chimene iwo anachinena? Yohane 6:30, 31. Kodi Yesu anati chiyani za mkate wochokera kumwamba? Yohane. 6:32, 33.**

"Ayudawo amalemekeza Mose monga wopereka manna, Kupereka matamando ku chida, osamamuwona Iye amene kudzera mwa Iye ntchitoyi idakwaniritsidwa. Makolo awo anali atang'ung'udza motsutsa Mose, ndipo anali kukaikira ndi kumakana utumiki wake wa Umulungu. Tsopano mu Mzimu womwewo anaawo akana Yemwe akufotokoza uthenga wa Mulungu kwa iwo eni. 'Chifukwa chake Yesu adati kwa iwo, indetu, indetu, ndinena kwa inu, si Mose amene anakupatseni inu mkate wa kumwamba.' Wopatsa manna anali atayimirira pakati pawo. Anali Khristu Mwini Yemwe adatsogolera Ahebri kudutsa m'chipululu, ndipo tsiku lililonse anali kuwadyetsa iwo ndi mkate wochokera kumwamba. Chakudya chimene chija chinali choyimirira cha mkate weniweni wochokera kumwamba. Mzimu wopatsa moyo, woyenda kuchokera ku chizalo cha umulungu, ndiye Manna weniweni." —***The Desire of Ages*, pp. 385, 386.**

**b. Pokhala ndi malingaliro awo ogokhazikika pa mkate wachilengedwe, wakuthupi, kodi ndi pempho lanji limene iwo adalipereka- nanga kodi ndi chiyani chimene Ambuye anafotokoza? Yohane 6: 34-36.**

"Chisanzo chomwe Khristu adagwiritsa ntchito chinali chodziwika kwa Ayuda. Mose, kuzera mukuuzira kwa Mzimu Woyera, ananena kuti, 'munthu sakhala wamoyo ndi mkate wokha, koma munthu akhala wa moyo ndi zonse zakutuluka m'kamwa mwa Yehova.' Ndipo mneneri Yeremiya analemba kuti, 'Mau anu anapezeka, ndipo ndinawadya; mau anu anakhala mwa ine chikondwerero ndi chisangalaro ca mtima wanga.' Deuteronomo 8:3; Yeremiya 15:16. Arabi iwo eni anali ndi muyambi woti, kudya kwa Mkate, mu tanthauzo lake la uzimu, kunali kuwerenga kwa malamulo; ndi kuchita nchito zabwino; ndipo kawirikawiri zimanenedwa kuti pa kubwera kwa Mesiya a Israyeli onse azadyesedwa. Ziphunzitso za aneneri zimamvekesa bwino phunziro lokuya la uzimu la chozizwitsa cha mikate. Phunziro limeneli Khristu amafunisisa kuti atsegule kwa omvetsera ake mu sunagoge. Ngati iwo akanamvesesa malemba, Iwo akanatha kuzindikira mawu ake pamene Iye anati, 'Ine ndine mkate wa moyo.' Tsiku limodzi lapitalo, unyinji waukulu, utafooka ndi kutopa, udadyetsedwa mkate womwe Iye adapereka. Monga momwe kuchokera ku mkate uja iwo adalandira mphamvu zakuthupi ndi kusisimutsidwa, choteronso kuchokera kwa Khristu iwo akhoza kulandira mphamvu zauzimu kufikira ku Moyo Wamuyaya."—***Ibid.*, p. 386**

## 5. KUUKITSIDWA NDI MOYO WAMUYAYA — Lachisanu, Epulo 3

**a.** Kodi ndi malonjezo awiri anji ogwirizana amene akuperekedwa kwa iwo amene azilumikiza okha ndi Khristu – nanga ndi motani mmene izi zimabweretsera chiyembekezo kwa wochimwa aliyense? Yohane 6: 37-40.

---

---

"Onse amene adamlandira Iye mwa chikhulupiriro, [Yesu] adati, azakhala ndi moyo wamuyaya. Palibe ndi mmodzi yense amene azatayika."—***The Desire of Ages*, p. 387**

"Musamvere lingaliro la mdani kuti mukhale kutali ndi Khristu mpaka mutadzipanga nokha kukhala wabwino; kufikira mutakhala wabwino mokwanira kubwera kwa Mulungu. Ngati inu mungayembekezere kufikira nthawi imeneyo, simuzabwera konse. Pamene Satana aloza kuzobvala zanu zokuda, bwerezani lonjezo la Yesu loti, 'Ndipo iye wakudza kwa ine sindizamutaya iye kunja.' Yohane 6:37. Muuzeni mdani kuti mwazi wa Yesu Khristu umayeretsa kuchoka ku uchimo wonse. Pangani pemphero la Davide kukhala lanu, 'Mundiyeretse ndi hisope ndipo ndizayera; Munditsuke ndipo ndizakhala wa mbu woposa matalala.' Masalimo 51: 7.

"Nyamukani nimupite kwa abambo anu. Adzakumana nanu mudakali patali. Ngati inu mungatenge khwerero ngakhale limodzi chabe kupita kwa Iye molapa. Iye azathamanga kuzakukhumbatirani inu mumanja a chikondi chopanda malire. Khutu Lake ndi loseguka ku kulira kwa mtima wolapa. Kupempha koyambirira komweko kwa mumtima kwa Mulungu kumaziwika kwa Iye. Palibe pemphero limene linapempheredwapo, ngakhale monon'gona motani, palibe msozi umene unagwetsedwa, ngakhale mtseri motani, palibe khumbo loona mtima lofuna Mulungu limene limakhalapo, ngakhale mofooka, muzonse Mzimu wa Mulungu umapita kukakumana ndi zonsezi. Ngakhale lisanaperekedwa pemphero kapena

kukhumba kwa mtima kusanaziwike, chisomo cha Khristu chimapita kuti chikakumane ndi chisomo chimene chikugwira nchito pa mzimu wa munthu." ***– Christ's Object Lessons, pp. 205, 206.***

**b. Kodi Ayuda osakhulupirira anang'ung'udza chiyani nanga kodi Yesu analonjeza chiyani kwa amene akhulupirira mwa Iye? Yohane 6: 41-51.**

---

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu ndi chimodzi, Epulo 4

1. Patsogolo pa chozizwitsa cha mikate, kodi otsatira a Khristu adafuna kuchita chiyani?
2. Fotokozani cholinga chachikulu cha khamu lomwe limamutsatira Yesu.
3. Fotokozani mawu a Yesu mu Yohane 6:29.
4. Kodi ndi chisanzo chanji chomwe Khristu anagwiritsa ntchito kuwonetsera gwero la moyo wa uzimu?
5. Kodi atsogoleri achiyuda anaonetsa bwanji kuweruziraru koipa kolimbana ndi Khristu?

**SABATA, EPULO 12, 2025** **PHUNZIRO 2**

# CHIBVUTO KU GALILEYA

**VESI LOLOWEZA: “Chifukwa chake Yesu anati kwa iwo, Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Ngati simukudya thupi la Mwana wamunthu ndi kumwa mwazi wake, mulibe moyo mwa inu nokha” (Yohane 6:53).**

**Zowelenga Zoonjezera:** ***Testimonies for the Church*, vol. 5, *pp.* 573-580.**

**“Chikhulupiriro chofunikira kwambiri chokha ndicho chikhulupiriro chimene chimalandira choonadi ndi kuchiphatikiza icho kukhala gawo la munthu ndi mphamvu zotsogolera moyo ndi machitachita.”—*Testimonies for the Church, vol. 5, p. 576.***

## 1. MOYO MU THUPI NDI MU MWAZI WA KHRISTU — Loyamba, Epulo 6

**a. Kodi ndi zotsatira zanji zimene mawu a Khirstu analinazo pa atsogoleri a chipembedzo? Yohane 6:52. Kodi Iye analongosola chiyani za thupi Lake ndi mwazi Wake? Yohane 6:53-55.**

---

---

“Tsopano arabi anafuula mokwiya, ‘Kodi munthu uyu angakhoze bwanji kutipatsa ife kudya thupi lake? Iwo anakhudzidwa pomvetsetsa mawu Ake mu lingaliro lawamba lofanana monga anachitira Nikodemo pamene anafunsa kuti, ‘Kodi munthu angabadweso bwanji atakalamba? Yohane 3:4. Pamlingo wina, iwo anamvetsesa tanthauzo la Yesu, koma sanali ofuna kuvomereza tanthauzolo. Pakupotoza mawu Ake, iwo ankayembekeza kuutsa tsankho mwa anthu lotsutsana ndi Iye.”— ***The Desire of Ages, p. 389*.**

**b. Kodi kudya thupi ndi kumwa mwazi wa Mwana wa Mulungu kumatanthauza chiyani kwenikweni? Yohane 6:56, 57; 1 Yohane 3:24; 5:12.**

---

---

“Kudya thupi ndi kumwa mwazi wa Khristu ndiko kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wa iwe mwini, kukhulupirira kuti Iye amatikhululukira machimo athu, ndikuti ndife anthunthu mwa Iye. Ndi kudzera mu kuona chikondi chake, kudzera mukukhazikika pa icho, ndi kuchimwa icho, ndi mmene ife timakhalira otenga nawo gawo akhalidwe lake. Chomwe chakudya chili kuthupi, Khristu ayenera kukhala chomwecho kumoyo.”—***Ibid., p. 389*.**

## 2. MAWU A MULUNGU

**Lachiwiri, Epulo 7**

**a. Ndi pamodzi ndi kufotokozera koonjezera kwanji kumene Yesu anamveketsa bwino tanthauzo la mawu Ake? Yohane 6:63.**

---

---

"Chakudya sichingatipindulire ife kanthu pokhapokha titachidya icho, pokhapokha chitakhala mbali yamoyo wathu.Choncho Khristu alibe phindu kwa ife ngati sitimudziwa Iye ngati Mpulumutsi wa ife eni. Chidziwitso cha mmalemba chabe sichidzatichitira chabwino chilichonse. Tiyenera kudya pa Iye, kumulandira Iye mu mtima, kotero kuti moyo wake ukhale moyo wathu. Chikondi Chake, chisomo Chake, chiyenera kuphatikizidwa kuthupi. . . .

"Moyo wa Khristu umene umapereka moyo kudziko lapansi uli m'mawu ake. Ndi kudzera mu mawu ake mmene Yesu anachiritsira matenda ndi kutulutsa ziwanda; Ndi mawu Ake anatontholetsa nyanja, ndi kuukitsa akufa; ndipo anthu adachitira umboni kuti mawu ake adali ndi mphamvu. Iye analankhula mawu a Mulungu, monga analankhulira kudzera mwa aneneri ndi aphunzitsi onse a m'Chipangano Chakale. Baibulo lonse ndi chionetsero cha Khristu, ndipo Mpulumutsi anafuna kukhazikitsa chikhulupiriro cha otsatira ake pa mawu. Pamene kukhalapo Kwake kowoneka kuyenera kuchotsedwa, mawu ayenera kukhala gwero la mphamvu zawo. Mofanana ndi Mbuye wawo, iwo anafunika kukhala ndi moyo 'ndi mawu onse akutuluka m'kamwa mwa Mulungu.' Mateyu 4:4.

"Monga momwe moyo wathu wakuthupi umachirikizidwa ndi chakudya, momwemonso moyo wathu wauzimu umachirikizidwa ndi mawu a Mulungu. Ndipo munthu wina ali yense akuyenera kulandira moyo kuchokera m'mawu a Mulungu kwa iye yekha. Monga momwe tiyenera kudzidyera tokha kuti tilandire thandzi, chomwecho tiyeneranso kulandiranso mawu kwa ife tokha. Sitiyenera kuwalandira iwo kudzera mu malingaliro a wina kokha. Tiyenera kuphunzira Baibulo mosamalitsa, kupempha Mulungu kuti atithandize ndi mzimu woyera, kuti timvetse mawu ake. Tiyenera kutenga ndime imodzi, ndi kuyika maganizo athu pa ntchito yofufuza ganizo limene Mulungu watiikira ife mu ndimeyi. Tiyenera kukhazikika pa ganizolo mpaka litakhala lathulathu, ndipo tidziwa 'chomwe ateroYehova.' "— ***The Desire of Ages, pp. 389, 390.***

**b. Kodi mneneri Yeremiya akulongosola motani za chochitika chimenechi? Yeremiya 15:16.**

---

---

---

"Ngati tizatenga Mulungu pa mawu ake, ife tidzaona chipulumutso chake. . . .Tiyenera kulandira mawu a Mulungu. Tiyenera kudya mawu, kukhala mu mawu; ndiwo thupi ndi mwazi wa Mwana wa Mulungu. Tiyenera kudya thupi Lake ndi kumwa mwazi Wake—kulandira mwa chikhulupiriro makhalidwe Ake auzimu."**— Testimonies *for the Church,* vol. 6, pp. 51, 52**

**a. Kodi ndi vuto lotani limene mawu a Khristu anayambitsa pakati pa ophunzira ake omwe—nanga kodi ndi motani momwe ili lili chenjezo kwa ife lero lino? Yohane 6:60, 61, 65, 66.**

---

---

"Yesolo linali lalikulu kwambiri. Changu cha anthu amene ankafuna kumugwira ndi kumulonga ufumu chinazirala. Iwo ananena kuti ulaliki umenewu m'sunagoge unatsegula maso awo. Tsopano iwo anali osanyengedwa. M'maganizo mwawo mawu Ake anali kuvomereza kwa chindunji kuti Iye sanali Mesiya, ndi kuti palibe mphotho ya padziko lapansi imene inayenera kupezedwa kudzera mukugwirizana ndi Iye. Iwo analandira mphamvu Yake yochita zozizwitsa; iwo anali ofunitsitsa kumasulidwa kumatenda ndi kuzunzika; koma sangathe kubwera mukumvera chifundom moyo Wake wodzipereka Yekha nsembe. Iwo samasamala za ufumu wodabwitsa wa uzimu umene Iye analankhula. Osaona mtima, odzikonda, amene adamufuna Iye, sanamufunenso Iye.Ngati Iye sangapereke mphamvu Zake ndi chikoka chake kuti apeze ufulu wawo kwa Aroma, iwo sagakhale ndikanthu kochita ndi Iye. . . .

"Kudzera mu mawu a choonadi, mankhusu anali kulekanitsidwa ndi tirigu. Chifukwa cha kuti iwo anali achabechabe ndi odzilungamitsa okha kwambiri mwakuti sakadalandira chidzudzulo, okonda kwambiri dziko mwakuti sangabvomere moyo wodzichepetsa, ambiri anapatuka mkuchoka kwa Yesu. Ambiri akuchitabe zomwezi. Miyoyo ikuyesedwanso masiku ano monga momwe anachitira ophunzira aja m'sunagoge ku Kapernao. Pamene chowonadi chabweretsedwa ndi kukhuza mumtima, iwo amawona kuti mmoyo yawo siili yogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu. Iwo amaona kufunika kwa kusintha kotheratu mwa iwo okha; koma Sali okonzeka kutenga ntchito yodzikaniza wekha. Chotero iwo amakwiya pamene machimo awo adziwika. Iwo amachoka ali okhumudwa, monganso momwe ophunzira aja anamsiya Yesu, akung'ung'udza, kuti, "Mawu awa ndi ovuta; ndani angawamve?*"*— ***The Desire of Ages*, pp. 391, 392 .**

**b. Atatha ophunzira aja kumuchokera Iye, kodi Khristu anawafunsa chiyani ophunzira khumi ndi awiri aja? Yohane 6:67. Kodi masiku ano tingabwerenze bwanji mawu anzeru a Petro? Yohane 6:68, 69.**

---

---

---

Kupyora mu mbiri ya bwino ndi yoipa, kupyora mu mdima, kupyora m'zidani zonse za amithenga a Satana, Dzuwa la Chilungamo limawalira modekha, kusanthula zoipa, kuubwenza uchimo, ndi kutsitsimutsa mzimu wa odzichepetsa ndi olapadi. 'Ambuye, tidzamuka kwayani? Inu mulinawo mawu a moyo wosatha.' "—***Testimonies to Ministers*, p. 285.**

## 4. KUCHOKERA KU WOPHUNZIRA KUPITA KWA ADANI — Lachinayi, Epulo 9

**a. Kodi tinganene chiyani kwenikweni za iwo amene atembenuka kuchoka kwa Khristu? 1 Yohane 2:19. Kodi ndimbali yanji yokhumudwitsa imene ophunzira omwe sanakhudzike anatenga?**

---

"Pamene ophunzira amene sanakhudzike anatembenuka mkuchoka kwa Khristu, mzimu wina wachilendo unayamba kuwalamulira iwo. Iwo sanathe kuona kalikonse kokopa mwa Iye amene poyamba anampeza kukhala wokondweretsa. Iwo anafunafuna adani ake, chifukwa anali ogwirizana ndi mzimu wawo ndi ntchito zawo. Iwo anatanthauzira molakwika mawu Ake, kutembenuza zonena Zake, ndi kutsutsa zolinga Zake. Iwo adalimbikitsa machitidwe awo kudzera mu kusonkhanitsa chilli chonse chimene chingatembenuzidwe mkumutsutsa Iye; ndipo mkwiyo woterowo unasonkhezeredwa ndi malipoti onama amene amati moyo Wake unali pangozi."— **The *Desire of Ages*, pp. 392, 393 .**

**b. Kodi chimachitika ndi chiyani kwa omvetsera malingaliro akuthupi? Aroma 16:17, 18.**

---

"Kutamanda ndi kuyamikira mokokomeza kungakhale kokondweretsa . . . koma chowonadi nchosalandilika; iwo sangathe kuchimva icho. Pamene makamu a anthu akutsatira, ndipo makamuwo akudyetsedwa, ndipo kufuula kwa chipambano kukumveka, mawu awo amveka mokwera m'chiyamikiro; koma pamene kufufuza kwa Mzimu wa Mulungu kuwulula tchimo lawo, ndikuwawuza iwo kuti alisiye ilo, iwo atembenuzira mbuyo zawo osafuna choonadi, ndipo samayendanso ndi Yesu."—***Ibid., p. 392.***

**c. Kupatula aja amene anamusiya Yesu, ndi ndaninso wina amene anagwirizana mumtima mwake ndi adani Ake—ndipo kodi kugwirizana kwa mtima watheka kumeneku kunasonyezedwa motani? Yohane 6:70, 71.**

---

Ulaliki wa Kristu m'sunagoge wonena za mkate wamoyo unali pa chiyambi pa kusintha kwa mbiri ya Yudasi. . . .Iye anaona kuti Khristu anali kupereka zinthu za uzimu osati za dziko. Iye ankadziona yekha ngati wopenya patali, ndipo ankaganiza kuti iye akutha kuona kuti Yesu sadzakhala ndi ulemu, ndipo sadzapereka udindo wapamwamba kwa otsatira ake. Iye anatsimikiza mtima kuti asadziphatike kwambiri kwa Khristu koma kuti achoke. Iye akhoza kumayang'ana. Ndipo iyedi amayang'anisitsa.

"Kuyambira nthawiyo iye amafotokoza zoonetsera kukayikira komwe kumasokoneza ophunzira. Iye amayambitsa mitsutso ndi nkhani zosocheretsa, kumabwereza mitsutso yomwe imanenedwa ndi alembi ndi Afarisi zotsutsa zonena za Kristu. Mavuto onse a ang'ono ndi a akulu ndi zobechera, zobvuta ndi zopinga zowonekera kukupititsa patsogolo uthenga wabwino, Yudasi amazimasulira monga maumboni wotsutsa kulondola kwake kwa uthengawo."—***Ibid.*, p. 719.**

## 5. KUMZINDIKIRA WOMPELEKAYO — Lachisanu, Epulo 10

**a. Fotokozani khalidwe limene Yudasi anayamba kukhala nalo. Yohane 12:4-6; Miyambo 3:32.**

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

"[Yudasi] amatha kubweretsa mawu a m'Malemba amene sanali kugwirizana ndi choonadi chimene Kristu analikufotokoza. Malemba amenewa, olekanitsidwa ndi malembo ogwirizana nawo, amadodometsa ophunzira, ndipo amawonjezera kugwetsedwa mphwayi kumene kunali kuwavutitsa mosalekeza. Komabe zonsezi zinachitidwa ndi Yudasi m'njira yoti ziwonekere kuti anali wowafunira zabwino."— ***The Desire of Ages, p. 719.***

**b. Kodi ndi lonjezo lotani lomwe nthawi zambiri limatsimikiziridwa muzochitika zathu zachipembedzo– ingakhale mu zochitika zonga za mavuto a ku Galileya? Aroma 8:28.**

____________________________________________________________

____________________________________________________________

"Pamene Yesu anapereka chowonadi choyesa chimene chinapangitsa ophunzira Ake ambiri kubwerera m'mbuyo, Iye ankadziwa chimene chidzakhala chotulukapo cha mawu Ake; koma Iye adali ndi cholinga cha chifundo choti akwaniritse. Iye anaoneratu kuti pa nthawi yakuyesedwa ali yense wa ophunzira Ake okondedwa adzayesedwa koopsa. Zowawa zake mu Getsemane, kuperekedwa kwake ndi kupachikidwa kwake, kukanakhala kwa iwo chiyeso choyesa kwambiri. Zikanakhala kuti sipadapelekedwe chiyeso amenewa, pakutula pansi kukhulupirika kwawo kwa Yesu, akanabweretsa chisoni chowawa kwa ophunzirawo, kuwonjezera pa chisoni chawo ndi kukhumudwa chifukwa cha kuwonongeka kwaziyembekezo zawo zokondedwa koposa. Mu nthawi ya mdima ija, chitsanzo cha amene adamusiya chikadawatengera ena kwa iwo. Koma Yesu anabweretsa vuto limeneli pamene kudzera mukukhalapo Kwake kwa kuthupi Iye akanakhoza kulimbikitsabe chikhulupiriro cha otsatira Ake owona."— ***Ibid., p. 394.***

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu ndi chimodzi, Epulo 11

1. Kodi ndi motani mmene ife 'tingadye thupi la Mwana wamunthu ndipo kumwa mwazi wake'?
2. Kodi kuyang'ana kwa Yesu kumatanthauza chiyani?
3. N'chifukwa chiyani ena anakhumudwa ndimawu a Khristu?
4. Kodi patsogolo pake anachita chiyani—ndipo kodi ili ndi chenjezo lotani kwaife?
5. Fotokozani mkhalidwe wauzimu wa Yudasi zitachitika izi, ndi zotsatira zake.

SABATA, EPULO 19, 2025

PHUNZIRO 3

# YESU PA PHWANDO LA MISASA

**VESI LOLOWEZA: "Ndipo anadabwa ndi chiphunzitso chake; chifukwa mau ace anali ndi ulamuliro" (Luka 4:32).**

**Zowelenga zoonjezera**: *Thoughts From the Mount of Blessing*, pp. 31–35.

"Yesu amadziwa zofuna za moyo. Kudzikweza, chuma, ndi ulemu sizingakhutiritse mtima. 'Ngati munthu aliyense amva ludzu, muloleni iye abwere kwa Ine.' Olemera, osauka, apamwamba, otsika, amalandiridwa mofanana. Iye amalonjeza kuti apeputsa malingaliro olemedwa, kutonthoza omva chisoni, ndikupereka chiyembekezo kwa otaya mtima."— **The *Desire of Ages*, p. 454.**

## 1. MOYO WA PAKHOMO WA YESU

**Loyamba, Epulo 13**

**a. Kodi Yesu anakumana ndi bvuto lanji lalikulu kunyumba kwake komwe? Yohane 7:5.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

"Adakali wamng'ono kwambiri, Yesu anayamba kuchita zinthu mwa Iye yekha mukupanga khalidwe Lake, ndipo ingakhale ulemu ndi chikondi kwamakolo ake sizinamulepheretse kumvera mawu a Mulungu. 'Kwalembedwa' chinali chifukwa Chake cha mchitidwe uli wonse wosiyana ndi miyambo yam'banja mwawo. Koma chikoka cha arabi chinapangitsa moyo Wake kukhala wowawa. Ingakhale mu unyamata Wake anayenera kuphunzira phunziro lovuta la kukhala chete ndi kupirira moleza mtima.

"Abale ake, omwe amatchedwa ana a Yosefe, anali kumbali ya arabi. Iwo amakakamira kuti miyambo iyenera kumatsatiridwa, monga ngati inali zofuna za Mulungu. Iwo amaonanso kuti malamulo a anthu ndi apamwamba kuposa mawu a Mulungu, ndipo amakwiya kwambiri ndi kufotokoza momveka bwino kwa Yesu posiyanitsa pakati pa bodza ndi choonadi. Kumvera kwake mosamalitsa ku malamulo a Mulungu iwo amakutsutsa kuti ndi kuuma mtima. Iwo amadabwa ndi chidziwitso ndi nzeru zimene Iye amasonyeza poyankha arabi. Iwo ankadziwa kuti Iye sanalandire maphunziro kuchokera kwa anzeru, komabe iwo samalephera kuona kuti Iye anali mphunzitsi kwa iwo. Iwo anazindikira kuti maphunziro Ake anali amtundu wa pamwamba kuposa awo. Koma iwo sanazindikire kuti Iye anali ndi mwayi wofika kumtengo wamoyo, gwero lachidziwitso chimene iwo anali mbuli."— ***The Desire of Ages, p. 86.***

**a. Kodi ndi ganizo lotani lomwe abale a Khristu adapereka kwa Iye poyembekezera Phwando la Misasa la pachaka? Yohane 7:3, 4.**

---

---

"Abale [ake a Kristu] amaganiza kuti n'kulakwa kuti iye akhale ndi udani ndi anthu a akulu ndi ophunzira a dziko lawo. Iwo ankaona kuti amuna amenewa ayenera kukhala olondola, ndiponso kuti Yesu anali wolakwa podziika yekha m'chidani ndi iwo. Koma iwo anali ataona moyo wake wopanda chilema, ndipo ngakhale iwo sanali kudziika pa mdandanda wa ophunzira Ake, iwo anali atachita chidwi kwambiri ndi ntchito zake. Kutchuka kwake mu Galileya kunali kokhutiritsa ku chikhumbo chawo; iwo ankayembekezerabe kuti Iye adzapereka umboni wamphamvu zake zimene zikanatsogolera Afarisi kuona kuti Iye anali chimene Iye ankadzinenera kukhala. Bwanji ngati Iye akanakhala Mesiya, Kalonga wa Israeli! Iwo ankakondwelera ndi lingaliro limeneli ndi chikhutiro chodzikweza.

"Iwo amkakhumba ichi kwambiri mwa kuti anakakamiza Khristu kupita ku Yerusalemu. 'Chokani kuno," iwo anati, 'ndipo mupite ku Yudeya, kuti ophunzira anunso akapenye ntchito zimene Inu mukuchita. Pakuti palibe munthu wa kuchita kanthu kalikonse mobisa, nafuna iye yekha kudziwika poyera. Ngati muchita izi, dziwonetseni nokha kudziko.' 'Ngati'adawonetsa kukayikira ndi kusakhulupirira. Iwo amamuika Iye kukhala wamantha ndi wofooka. Ngati Iye mwini amkadziwa kuti Iye anali Mesiya, nchifukwa ninji akudzisunga mwa chilendo kumeneku ndikusachitapo kanthu? Ngati Iye analidi ndi mphamvu yotere, bwanji osapita ku Yerusalemu molimba mtima, ndikukadziika molingana ndi kudzinenera kwake? Bwanji osachita mu Yerusalemu ntchito zodabwitsa zosimbidwa za Iye ku Galileya? Iwo adati, musabisale mmadera obisika, ndi kumachita ntchito zanu zamphamvu kukupindulirira anthu wamba ndi asodzi osaphunzira. Dziwonetsereni nokha kulikulu, pindulani ndi chithandizo cha ansembe ndi olamulira, ndikugwirizanitsa mtunduwu pakukhazikitsa ufumu watsopano."—***The Desire of Ages, p. 450.***

**b. Fotokozani vuto limene nthawi zonse anthu ofatsa akhala akukumana nalo. Masalmo 86:14.**

---

"Abale a Yesu amenewa analingalira mwazolinga zadyera zopezeka kawirikawiri m'mitima ya anthu ofunitsitsa kudzionetsera. Mzimu umenewu unali mzimu womwe umalamulira dziko lapansi. Iwo anakhumudwitsidwa chifukwa, m'malo mofunafuna mpando wachifumu wosakhalitsa, Kristu anadzitcha yekha kukhala mkate wamoyo. Iwo anakhumudwa kwambiri pamene ophunzira ake ambiri anamusiya. Iwo eni adachoka kwa Iye kuthawa mtanda wakuvomereza zomwe ntchito Zake zidawululira—kuti Iye anali Wotumidwa wa Mulungu."—***Ibid., p. 451***.

**a. Kodi ndi malingaliro otsutsana otani amene anadzutsidwa okhuzana ndi za Yesu? Yohane 7:11, 12.**

“Kuchokera ku Yerusalemu mbiri yazozizwitsa za Kristu inafalikira kuli konse kumene Ayuda anamwazikana; ndipo ngakhale miyezi ingapo sanakhale nawo m’maphwando, chidwi cha Iye sichinazilale. Anthu ambiri ochokera kumadera onse a dziko lapansi anabwera ku Phwando la Misasa ndi chiyembekezo choti adzamuone. Kumayambiriro kwa phwando anthu ambiri anamfunsa za Iye. Afarisi ndi olamulira anali kuyembekezera kuti Iye abwera, ndi kuyembekezera mwayi woti amutsutse Iye. Iwo adafunsa mwankhawa kuti, ‘Ali kuti Iyeyo?’ koma palibe amene amkadziwa. Lingaliro la Iye linali la pamwamba kwambiri mu malingaliro a onse. Chifukwa cha mantha kuwopa ansembe ndi olamulira, palibe amene adalimba mtima kumuvomereza kuti Iye ndi Mesiya, koma paliponse panali kukambirana mwakachetechete koma mozama za Iye. Ambiri ankamumuikira kumbuyo kuti ndi munthu wotumidwa kuchokera kwa Mulungu, pamene ena ankamunyoza Iye kuti ndi wonyenga wa anthu.*”— The Desire of Ages, pp.451, 452.***

**b.** Kodi motani mmene Yesu anakhazikitsira chete maganizo otsutsana okhudza Iye mwini? Yohane 7:14-18; Luka 4:32.

“Pakati pa phwando, pamene chiyembekezo chokhuzana ndi Iye chinali pa chimake, Iye analowa m’bwalo la Kachisi pamaso pa khamu la anthu. Chifukwa cha kusakhalapo kwake pa phwandolo, anthu amafotokoza kuti akuopa kudziika yekha mu mphamvu ya ansembe ndi olamulira. Onse anadabwa ndi kupezeka kwake. Mawu onse anatonthola. Onse anadabwa ndi kulemekezeka ndi kulimba mtima kwakupirira Kwake pakati pa adani amphamvu amene anali ndi ludzu lofuna moyo Wake.

“Ataimirira motere, phata la chikoka chakhamu lalikululo, Yesu analankhula kwa iwo mwakuti palibe munthu wina ali yense analankhulapo motere. Mawu ake anasonyeza chidziwitso cha malamulo ndi zikhazikitso za Israyeli, za utumiki wa nsembe ndi ziphunzitso za aneneri, choposatu chija cha ansembe ndi arabi. Iye anagamula nadutsa zochinga za myambo ndizikhazikitso zawo. Zochitika za moyo wa mtsogolo zinkawoneka ngati zatambasulika pamaso Pake. Monga munthu wopenya Wosaoneka, Iye analankhula za pa dziko lapansi ndi zakumwamba, munthu ndi Mulungu, ndi ulamuliro wotsimikizika. Mawu ake anali omveka bwino ndi okhuza kwambiri; ndipo kawirinso, monga ku Kapernawo, anthu anazizwa ndi chiphunzitso cace; 'pakuti mawu ake anali ndi mphamvu.' Luka 4:32. Onse anazizwa ndi chidziwitso chake cha malamulo ndi mauneneri.”—***Ibid., pp. 452, 453.***

**a. Kodi Yesu anazindikira chiyani mwa arabi ndipo Iye anawafunsa iwo funso lotani? Yohane 7:19.**

---

---

Yesu anapatsa arabi umboni wa umulungu Wake kudzera mukuwaonetsera kuti amawerenga mitima yawo. Kuyambira pa machiritso a ku Betesda iwo anali akumkonzekera Iye imfa. Motero iwo eniwo analikuswa lamulo limene ankati anali kuliteteza. 'Kodi Mose sanakupatseni inu chilamulo,' Iye anatero, 'ndipo palibe mmodzi wainu amene amasunga chilamulo? M'chifukwa chiyani mufuna kundipha Ine? *"*— ***The Desire of Ages,*** **p. 456.**

**b. Mu kuyankha kwawo kwa Khristu, kodi ndi za chiyani zimene arabi anamuneneza Iye—ndipo ndimotani momwe Iye anayankhira? Yohane 7:20-23.**

---

---

"Kubodza la [kuti ntchito Zake zodabwitsa zinali kusonkhezeredwa ndi mzimu woipa] Kristu sanalabadire. Iye anapitiriza kuwasonyeza kuti ntchito Yake yochiritsa pa Betsaida kuti inali yogwirizana ndi lamulo la Sabata, ndipo inalungamitsidwa ndi kumasulira kumene Ayudawo anaika pa chilamulo. Iye anati, 'Mose anakupatsani inu mdulidwe; . . . ndipo mudula munthu tsiku la Sabata.' Malinga ndi lamulo, mwana aliyense ayenera kudulidwa patsiku la chisanu ndi chitatu. Ngati nthawi yoikidwiratu ifika pa Sabata, mwambowo uyenera kuchitidwa. Koposa kotani nanga kukuyenera kukhala kogwirizana ndi mzimu walamulo kumupanga munthu kukhala 'wangiro kwanthunthu pa Sabata.' "— ***Ibid., pp. 456, 457.***

**c. Fotokozani tanthauzo lalikulu la chenjezo lotsatira la Kristu. Yohane 7:24.**

---

---

"Olamulira anakhala chete; ndipo ambiri a anthuwo adati, "Si uyu kodi afuna kumupha uja? Koma tawonani, Iye alankhula molimbika mtima, ndipo iwo sakunena kanthu kwa Iye. Kodi olamulira akudziwa mwandithu kuti ameneyi ndiye Kristu? "—***Ibid., p. 457.***

"[Khristu] sayang'ana maonekedwe akunja; Saweruza monga momwe munthu amaweluzira. Iye salemekeza munthu kutengera udindo, luso, maphunziro, kapena ntchito yomwe munthu amagwira. 'Ndidzayang'ana kwa munthuuyu,' akutero, 'ingakhale kwa munthu wosauka, ndi wa mzimu wosweka, nanthunthumira ndi mawu anga. *"*— ***The Signs of the Times,*** **October 21, 1897.**

## 5. CHIWELUZO CHA MUNTHU *KUSIYANITSA NDI* CHA MULUNGU — Lachisanu, Epulo 17

**a. Kodi ndi motani mmene Malemba amaonetsera m'khalidwe wa maganizo a anthu m'dziko lino— kawirikawiri monga momwe zimaonekera m'nthawi zakale, koma makamaka lero lino? Yesaya 59:14, 15.**

________________________________________________

________________________________________________

________________________________________________

"Mabungwe a zoyipa akuphatikizana mphamvu zawo ndi kugwirizana. Iwo akudzilimbitsa kukonzekera mkangano waukulu wotsiriza. Kusintha kwakukulu kudzachitika posachedwapa pa dziko lapansi, ndipo migwirizano womaliza udzakhala ofulumira kwambiri. . . ..

"Mdani wapambana popotoza chilungamo, ndikudzaza mitima ya anthu ndi chikhumbo cha phundu lakudzikonda. . . .. Kulira kwa anthu ovutika ndi anjala kukubwera pamaso pa Mulungu, pamene kudzera mumtundu uli wonse wakuponderezana ndi kulanda anthu uunjika *chuma chambiri."*— ***Testimonies for the Church*, vol. 9, pp. 11, 12.**

**b. M'kati mwa chipwirikiti, n'chifukwa chiyani tingadalire njira za Mulungu? Yesaya 55:8, 9.**

________________________________________________

________________________________________________

"Ngakhale malingaliro okhala ndi malire a anthu ali osakwanira kulowa mu uphungu wa Wopanda malire, kapena kumvetsetsa bwino momwe zifuno Zake zimagwirira ntchito, komabe nthawi zambiri ndi chifukwa cha zolakwika zina kapena kunyalanyaza kwawo komwe kumawapatsa kusamvetsetsa mauthenga a Kumwamba. Kawirikawiri malingaliro aanthu, ngakhalenso a atumiki a Mulungu, amachititsidwa khungu ndi malingaliro a anthu, miyambo ndi ziphunzitso zonyenga za anthu, kotero kuti amatha kuzindikira pang'ono zinthu zazikulu zimene Iye wavumbulutsa m'mawu Ake."— *The Great Controversy, p. 344, 345.*

"Cholinga cha Mulungu kwa ana ake ndi chapamwamba kuposa momwe malingaliro amunthu angafikire. Iye wapereka m'chilamulo Chake chopatulika kukhala chithunzithunzi cha khalidwe Lake."— *Testimonies for the Church, vol. 8, p. 63.*

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu ndi chimodzi, Epulo 18

1. Fotokozani khalidwe la pakhomo pamene Yesu analeledwa.
2. Kodi ndi motani momwe chidwi cha abale ake a Khristu chimabwerezedwera masiku ano?
3. Kodi ndi malingaliro otsutsana otani amene anafalitsidwa ponena za Yesu?
4. Fotokozani mzimu umene arabi anaonetsa kwa Yesu.
5. Fotokozani kusiyana kwakukulu pakati pa njira za anthu ndi za Mulungu.

**SABATA, EPULO 26, 2025**

**PHUNZIRO 4**

# PALIBE AMENE ANAYANKHULA MONGA MUNTHU UYU

**VESI LOLOWEZA: "Anyamatawo anayankha, Nthawi yonse palibe munthu analankhula cotero." (Yohane 7:46).**

**Zowelenga Zoonjezera: *Testimonies to Ministers,* pp. 506–512.**

**"Kuzindikira ndi kuyamikira kwa chowonadi, Iye anati, kumadalira pang'ono pamalingaliro koposa pamtima. Choonadi chiyenera kulandiridwa mu moyo; icho chimaitanitsa chigonjero cha chifuniro."— The *Desire of Ages,* p. 455.**

## 1. ZOKHUMBA ZA ANTHU MWA YESU

**Loyamba, Epulo 20**

**a. Pakumva ndi kuona Yesu akulalikira poyera, Kodi ndi chiyani chomwe a Yuda ena anafunsa? Yohane 7:25, 26.**

---

"Ambiri mwa omvetsera Kristu anali anthu amene analikukhala kuYerusalemu, amene anali asakudziwa za ziwembu za olamulira pa Iye, anadzimva kukhala okokeredwa kwa Iye ndi mphamvu yosakanizika. Kukhudzika kunasindikiza pa iwo kuti Iye anali Mwana wa Mulungu."— **The *Desire of Ages,* p. 457.**

**b. Kodi Satana anachita chiyani pa olamulirawo kuti alimbikitse kukayikira? Yohane 7:27.**

---

"Satana anali wokonzeka kubweretsa kukayikira; ndipo chifukwa cha ichi njira inakonzedwa kudzera malingaliro awo olakwika okhudza Mesiya ndi kudza kwake. Anthu ambiri amakhulupirira kuti Khristu adzabadwira ku Betelehemu, koma kuti pakapita nthawi adzasowa, ndipo pakuwonekera Kwake kachiwiri palibe amene adzadziwe kumene achokera. Si ochepa okha amene ankakhulupirira kuti Mesiya sadzakhala ndi unansi wachibadwa ndi anthu. Ndipo chifukwa chakuti lingaliro lotchuka la ulemerero wa Mesiya silinakwaniritsidwe ndi Yesu wa ku Nazarete, ambiri analimbikira kulingaliro lakuti, 'Koma ife tikudziwa Munthu uyu kumene Iye achokera: koma pamene Khristu akadzadza, palibe mmodzi adzadziwa uko achokera. "—***Ibid.***

**a. Powerenga maganizo a anthu omumvetsera omwe anali kukaika, kodi Yesu anawauza chiyani iwo? Yohane 7:28.**

---

---

"Pamene iwo anali kugwederagwedera pakati pa chikaiko ndi chikhulupiriro, Yesu anatenga malingaliro awo, nati kwa iwo: 'Mundidziwa Ine, ndiponso mudziwa kumene ndi chokera; ndipo sindinaza Ine ndekha, koma Iye wondituma Ine amene inu simumudziwa, ali woona.' Iwo amazinena kuti amadziwa mmene chiyambi cha Khristu chidzakhalire, koma iwo anali osadziwa kotheratu.Ngati akanakhala moyo wogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu, akanadziwa Mwana wake pamene anaonekera kwa iwo."— ***The Desire of Ages,* p. 457.**

**b. Posowa zifukwa zomutsutsa Yesu, kodi ndi kudzera mu njira yanji imene atsogoleri achiyuda anafuna kumukhalitsa chete Iye? Yohane 7:30 (gawo loyamba). M'chenicheni, n'chifukwa chiyani sanathe kum'manga Iye? Yohane 7:30 (gawo lomaliza).**

---

---

"Omvera sakanatha kumvetsa mawu a Kristu. Mwa chionekere iwo anali kubwereza zonena zimene Iye ananena pamaso pa Khoti Lalikulu la Ayuda miyezi yambiri m'mbuyomo, pamene anadzilengeza yekha kuti ndi Mwana wa Mulungu. Monga olamulira pamenepo anayesera kuzinga Iye kuti amuphe, koterotso pano anafuna kumgwira Iye; koma anatsekeredwa ndi mphamvu yosaoneka, imene inaika malire kuukali wawo, ndikunena kwa iwo, mlingo uwu ndi umene mungathe kufikira, ndipo simupitirira apa." — ***Ibid.***

**c. Kodi ambiri anasonyeza bwanji chikhulupiriro chawo mwa Yesu—ndipo kodi olamulirawo analinganiza kuchita chiyani atazindikira kuti anthu anali kumumvera chisoni? Yohane 7:31, 32.**

---

---

---

"Atsogoleri a Afarisi, amene anali kuyang'ana mwa chidwi zochitikazo, anaona nkhope zoonetsa kumumvera chisoni pakati pa khamulo. Ndipo anafulumira kunka kwa ansembe a akulu, nakonza dongosolo loti amgwire Iye. Koma adapangana kuti amgwire Iye ali yekha; pakuti sanalimbika mtima kumgwira Iye pamaso pa anthu."—***Ibid., pp. 457, 458.***

## 3. KUITANIRA



**a. Pa tsiku lomaliza la phwandolo, kodi ndi fanizo lochititsa chidwi lotani limene Yesu anagwiritsa ntchito popereka chitonthozo kwa miyoyo yotopa ndi uchimo? Yohane 7:37, 38.**

---

"Mtima umene umalandira mawu a Mulungu sulingati thamanda lomwe madzi ake amangouma, sulingati chitsime chong'ambika chimene chitaya chuma chake. Uli ngati mtsinje wam'phiri, wodyetsedwa ndi akasupe osatha, amene madzi ake ozizira, othwanima amatumpha kuchokera kuthanthwe kupita kuthanthwe, kutsitsimula otopa, aludzu, olemedwa. Uli ngati mtsinje woyenda mosalekeza, ndipo pamene ukuyenda, umaya kwambiri ndi kukulirakulirabe, kufikira madzi ake opatsa moyo atafalikira padziko lonse lapansi. Mtsinje umene umayimba munjira yake pamene ukuyenda umasiya m'mbuyo mphatso yake yamaluwa ndi zipatso. Udzu womwe uli m'mphepete mwake ndi wobiriwira bwino, mitengo imakhala yobiriwira, maluwa ake amakhala ochuluka kwambiri. Pamene dziko likakhala lopanda kanthu ndi lofiirira chifukwa cha kutentha kwa m'chilimwe, mzere wamaluwa umalemba m'njira ya mtsinjewu.

"Zimakhalaso chomcho ndi mwana weniweni wa Mulungu. Chipembedzo cha Khristu chimadziwonetsera chokha ngati mfundo yofunikira kwambiri ndiyofalikira, mphamvu ya uzimu ya moyo, yogwira ntchito. Pamene mtima utsegukira kuchikoka cha kumwamba cha choonadi ndi chikondi, mfundo zimenezi zidzasefukiranso ngati mitsinje ya m'chipululu, kuchititsa kuti zipatso ziwonekere kumene tsopano kuli chilala ndi ng'amba."—***Prophets and Kings, p. 233, 234 .***

"'Ngati wina akumva ludzu' la chiyembekezo chopumulitsa, cha kumasulidwa ku zilakolako za uchimo, Khristu akuti, 'abwere kwa Ine, namwe.' Yohane 7:37."— ***The Ministry of Healing, p. 179.***

**b. Kodi ndi motani mmene kuitanira kumeneku kuyenera kumvetsetsedwanso? Yohane 7:39**.

---

"Khristu anapereka mfundo za choonadi mu uthenga wabwino. Muchiphunzitso Chake tikhoza kumwa mitsinje yoyera yomwe ikuyenda kuchokera kumpando wachifumu wa *Mulungu."*— ***Testimonies for the Church,* vol. 8, p. 309.**

"Chomwe timafunikira ndi chipembedzo chamoyo. Munthu mmodzi amene ali ndimalingaliro owonjezereka a udindo, amene moyo wake uli m'chiyanjano ndi Mulungu ndiponso amene ali wokangalika kaamba ka Kristu, adzakhala ndi chikoka cha mphamvu cha kuchita za bwino. Iye samamwa pa mtsinje wochepa, wakuda, woipitsidwa, koma wamadzi oyera, ochokera pa akasakupe a m'mwamba; ndipo iye akhoza kofotokozera mphamvu ndi mzimu watsopano ku mpingo. Pamene chitsenderezo chochokera kunja chikuchulukirachulukira, Mulungu akufuna kuti mpingo wake ukhale wopatsidwa moyo ndi choonadi chopatulika chimene iwo amakhulupirira. MzimuWoyera wochokera Kumwamba, wogwira ntchito limodzi ndi ana a amuna ndi a akazi a Mulungu, adzagonjetsa zopinga ndikukhala ndi chipambano mukulimbana ndi mdaniyo. Mulungu ali ndi zigonjetso zazikulu zosungira anthu Ake okonda chowonadi, osunga malamulo."—***Ibid., vol. 5, p. 581.***

**a. Monga chotsatira cha mawu a Khristu okamba za madzi a moyo, kodi ambiri ananena chiyani— ndipo chifukwa chiyani? Yohane 7:40 (fananisani ndi Deuteronomo 18:15).**

**b. Pamene ena analimbikitsidwa ndi chiyembekezo kudzera mu chochitika chimenechi, kodi ena anatani? Yohane 7:41-44.**

**c. Kodi ndi ulamuliro otani omwe anyamata analandira kuchokera kwa olamulira awo? Yohane 7:45. N'cifukwa chiyani sanathe kugwilaYesu? Yohane 7:46.**

"Pa tsiku lomaliza la phwando, anyamata amene anatumidwa ndi ansembe ndi olamulira kuti akamugwire Yesu, anabwerera opanda Iye. Iwo adafunsidwa mokwiya, Chifukwa chiyani simunabwere naye? Ndi nkhope zaulemu iwo anayankha, 'Palibe munthu analankhula monga Munthu uyu analankhulira.'

"Owumitsidwa monga momwe inaliri mitima yawo, iwo anasungunulidwa ndi mawu Ake. Pamene Iye anali kulankhula m'bwalo la kachisi, iwo anayandikira pafupi kuti apeze china chake chimene chingam'tembenukire Iye. Koma pamene iwo amamvetsera, cholinga chimene iwo anatumizidwira chinaiwalika. Iwo anaima ngati anthu opepetulidwa. Khristu adadzibvumbulutsa yekha ku miyoyo yawo. Iwo anaona izo zimene ansembe ndi olamulira samatha kuziona— umunthu osefukiridwa ndi ulemerero wa umulungu."— ***The Desire of Ages, p. 459.***

"[Khristu] amagwiritsa ntchito zinthu za m'chilengedwe zimene iwo ankazidziwa bwino pofotokoza choonadi cha Mulungu. Motero nthaka ya mu mtima imakonzetseredwa kuti ilandire mbewu ya bwino. Iye anapangitsa omvera Ake kumva kuti zokhumba Zake zimagwirizana ndi zawo, kuti mtima Wake umagunda molingana ndi chimwemwe ndi chisoni chawo. Pa nthawi yomweyo iwo amawona mwa Iye mawonetseredwe a mphamvu ndi ubwino waukulu kwambiri kuposa zomwe analinazo arabi olemekezeka kwambiri. Ziphunzitso za Kristu zinali zodziwika ndi zophweka, ulemu, ndi mphamvu zimene sizinali zodziwika m'kale kwa iwo, ndipo mfuwu yawo yokakamizika inali ya kuti: 'Nthawi zonse palibe munthu analankhula monga Munthu uyu analankhulira.' Anthu anamvera Iye mokondwera; koma ansembe ndi olamulira—iwo eni onyenga ku udindo omwe anadalilidwa nawo monga alonda a chowonadi—anadana ndi Khristu chifukwa cha chisomo chomwe chinavumbulutsidwa, chimene chinakokera makamu kutali ndi iwo kuti atsatire kuunika kwa moyo. Kupyolera mu chikoka chawo mtundu wa Chiyuda, polephera kuzindikira Umulungu wa Khalidwe lake, unamukana mombolo."— ***Testimonies for the Church,* vol. 5, p. 747.**

## 5. WOFUNAFUNA WOONA AKULIRATU

**Lachisanu, Epulo 24**

**a. Kodi ndi motani momwe ansembe a akulu ndi Afarisi anadzudzulira anyamatawo? Yohane 7:47-49.**

**b. Fotokozani zokambirana zomwe zinatsatirapo ndi Nikodemo—kuwulula kukula kwake kuyambira pa zokambirana zake ndi Khristu usiku mu Yohane chaptala 3. Yohane 7:50–52.**

"[Nikodemo] anabisa chowonadi mu mtima mwake, ndipo kwazaka zitatu panalibe zipatso zowonekera. Koma ngakhale Nikodemo anali asanavomereze Khristu poyera, mu Khonsolo Lalikulu la Asaduki mobwerezabwereza amalepheretsa machenjerero a ansembe oti amuwononge Khristu."— **The *Acts of the Apostles,* p. 104.**

"Phunziro limene Kristu anapereka kwa Nikodemo [pa ulendo wake wausiku mu Yohane chaputala 3] silinapite pa chabe. Kutsimikiza kudakhazikika pamalingaliro ake, ndipo mu mtima mwake adalandira Yesu. Kuchokera pakuyankhulana kwake ndi Mpulumutsi, iye adasanthula mowona mtima Malemba a Chipangano Chakale, ndipo adawona chowonadi chikuyikidwa m'malo enieni a uthenga wa bwino.

"Funso limene iye anafunsa linali la nzeru, ndipo likanadziyamikiritsa lokha kwa amene anali kutsogorera pa khonsoloyo akanapanda kunyengedwa ndi mdani. Koma iwo anali odzala ndi tsankho moti palibe umboni uli wonse wokomera Yesu wa ku Nazarete, ngakhale unali wokhutiritsa bwanji, umene unali ndi kukhuza kwa iwo. Yankho limene Nikodemo analandira, linali lakuti, 'Kodi iwenso uli woturuka m' Galileya? santhula, nuwone kuti palibe mneneri anachokera ku Galileya.'

Ansembe ndi olamulira ananyengedwa, monga momwe Satana anafunira, kuti akhulupirire kuti Kristu anachokera ku Galileya. Ena amene anadziwa kuti iye anabadwira ku Betelehemu, anangokhala chete, kuti mabodza woasala ndidwe mphamvu zake."— ***The SDA Bible Commentary [EG White Comments], vol. 5, p. 1136.***

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

**Lachisanu ndi chimodzi, Epulo 25**

1. Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anakopa chidwi ndi ulemu wa anthu?
2. Kodi ndi motani mmene olamulira achiyuda analimbikirira mukuyesesa kumuimitsa Yesu?
3. Kodi ndi pempho lanji la poyera limene Yesu analipanga pa tsiku lomaliza la phwando?
4. Fotokozani mkangano waukulu umene unatsatirapo.
5. Poganiza za anthu amene ndimawadziwa, kodi ndiyenera kukumbukira chiyani za Nikodemo?



**Zopeleka za Sabata Loyamba**

**SABATA, MEYI 3, 2025**



**Za Mauthumiki a pa dziko Lonse**

**Lero, uthenga wa panthawi yake ukumvekanso:**

"Mzimu wa umishonale uyenera kudzutsidwanso m'mipingo yathu. Membala aliyense wa mpingo ayenera kuphunzira momwe angathandizire kupititsa patsogolo ntchito ya Mulungu, mu ma mission a kunyumba ndi am'maiko akunja. Pafupifupi gawo limodzi mwamagawo 1,000 la ntchito imenei ikuyenera kuchitidwa m'magawo a amishonale ikuchitika mochepa kwambiri. Mulungu akuitana antchito Ake kuti amuwonjezere malo atsopano. Pali minda ya chonde kwambiri yomwe ikuyembekezera wantchito wokhulupirika. Ndipo angelo otumikira adzagwirizana ndi membala aliyense wamumpingo amene adzagwira ntchito mopanda undekha chifukwa cha Ambuye.

"Mpingo waKhristu pa dziko lapansi unakhazikitsidwa ndi cholinga cha utumiki, ndipo Ambuye akufuna kuona mpingo wonse ukukonza njira zomwe anthu apamwamba ndi otsika, olemera ndi osauka, angamvere uthenga wa choonadi. Si onse amene amaitanidwa kukagwira ntchito eni okha m'maiko akunja, koma onse angachite china chake mwamapemphero awo ndimphatso zawo kuthandiza ntchito ya umishonale.

"Wamalonda wina wa ku Amereka amene anali Mkristu wolimbikira, pocheza ndi wantchito mnzake ananena kuti iye mwiniyo amagwirira ntchito Khristu maola makumi awiri ndi anayi a tsiku. 'Muzamalonda zanga zonse,' iye anatero, 'ndimayesetsa kuimira Mbuye wanga. Pamene ndili ndi mwayi, ndimayesetsa kukopa ena kwa Iye. Tsiku lonse ndi kugwirira ntchito Khristu. Ndipo usiku, pamene ndilikugona, ndili ndi munthu womugwirira ntchito Khristu ku China.'

"Pofotokoza iye anawonjezera kuti: 'Mu ubwana wanga ndinatsimikiza mtima kupita monga mmishonale kwa anthu akunja. Koma bamboo anga atamwalira ndinatenga bizinezi yawo kuti ndizipeza zofunikira za pabanja langa. Tsopano, m'malo moti ndizipita ndekha, ndimathandiza mumishonale. M'tauni yotere yachigawo chotere cha China, wantchito wanga amaima. Ndipo kotero, pokhala ine m'tulo, ndikhala ndikumugwirira ntchito Kristu kudzera mwa wondiimira. "— ***Testimonies for the Church, vol. 6, pp. 29, 30 .***

Tsopano kuposa kale ndi nthawi yoti muyike ndalama mu banki ya Kumwamba kudzera mu mamishoni a padziko lonse lapansi. Sizidzakhala zosavuta, ndipo m'tsogolo mutha kukhala mochedwa kwambiri. Miyoyo ikuwonongeka wopanda Khristu ndi choonadi chamunthawi ino, ndipo Ambuye watipatsa kuwala kwa mtengo wapatali kuti tifalitse dziko lonse lapansi.

Chonde perekani mowolowa manja, ndipo Ambuye akudalitseni kwambiri ndi mphatso yanu. Zikomo!

***A Dipatimenti ya Sabata sukulu ya General Conference***

**SABATA, MEYI 3, 2025**

**PHUNZIRO 5**

# "NGAKHALE INENSO SINDIKUTSUTSA IWE"

**VESI LOLOWEZA: "Inenso sindikutsutsa iwe; pita; kuyambira tsopano usachimwenso" (Yohane 8:11, mbali yomalidza).**

**Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, vol 2, pp. 73-77.**

**"Chikondi chachikhristu chimakhala chochedwa kutsutsa, chimakhala chachangu kuzindikira kugonja, chokonzeka kukhululukira, kulimbikitsa, kukhazikitsa osochera munjira ya chiyero, ndikuwakhazikitsa mapazi awo mmenemo"-** ***The Desire of Ages, p. 462.***

## 1. MSAMPHA WA YESU

**Loyamba, Epulo 27**

**a. Pamene Yesu anali kuphuzitsa mkachisi, kodi ndi chiyani chimene Alembi ndi Afalisi anachita? Yohane 8:2-3.**

---

---

"(Khristu) mwachangu anasokonezedwa. Gulu la Afalisi ndi Alembi linaza kwa iye, likukoka mzimayi wogwidwa ndi mantha, amene ndimawu okuwa komanso olimba iwo amamuneneza iye zakuphwanya lamulo lachisanu ndi chiwiri."- ***The Desire of Ages, p. 460.***

**b. Ponetsera ulemu wooneka waukulu wa malamulo, kodi ndi funso lanji limene Afalisi analipeleka kwa Khristu-nanga kodi cholinga chawo chenicheni chinali chiyani? Yohane 8:4- 6(Mbali yoyamba**).

---

---

"Kulemekeza kwawo kwachinyengo kunaphimba dongosolo lawo lakuya limene anakhazikitsa kuchionongeko chake. Iwo anatenga mwayi umenewu kuti akhazikitse chiweludzo chakumutsutsa iye, poganiza kuti yankho lililonse limene iye angathe kulipereka, iwo adzapeza mwayi wakumuneneza iye. Ngati iye angamukhululukire mzimayiyo, ndiye kuti iye atha kuimbidwa mulandu wakupeputsa lamulo la Mose. Ngati iye angamuweludze iye kuti ndiwoyenera kuphedwa, iye adzanenezedwa kwa Aroma monga mmodzi amene akuzipatsa ulamuliro umene ndi waiwo okha basi."- ***Ibid., pp. 460,461.***

**a. Kodi ndimotani mmene Yesu anayankhira kuchinyengo cha Afalisi? Yohane 8:6(mbali yomaliza).**

---

"Yesu anayang'ana kwakamphindi pazochitikazi- pa olakwa onjenjemera mumanyazi ake, pankhope zopanda chisoni za olemekezeka, zopandilatu ingakhale chisoni chaumunthu. Mzimu wake wachiyero chopanda banga unakhuzika pakuona zotelezi. Iye bwinobwino amadziwa cholinga chimene mlanduwu wabweletsedwa kwa Iye. Iye amawerenga mtima, ndikuziwa khalidwe ndi mbili ya moyo wawina aliyense amene anali pamaso pake. Awawa ozinena kukhala oteteza chilungamo akhala akutsogolera olakwayi kuuchimo, kotelo kuti iwo akathe kuchela msampha Yesu. Popanda kuonetsa chizindikiro china chilichonse cha kuti iye wamva funso lawo, Iye anawelama pansi, nakhazikitsa maso ake pansi, ndipo anayamba kulemba pansi."-***The Desire of Ages, p. 461.***

**b. Kodi ndimotani mmene Yesu anaonetsera kuti onenezawo iwo eni sianthu oti alibe chimo- nanga ndichiyani chimene iwo anachita kenako? Yohane 8:7-9.**

---

"Oneneza anagonjesedwa. Tsopano, mikanjo yawo yachiyero chonamizira inang'ambidwa kuchoka kwa iwo,iwo anayima, otsutsidwa ndi ochimwa, pamaso pa olungama wamuyaya. Iwo ananjenjemera kuopa kuti zochimwa zawo zobisika zammiyoyo yawo zitha kuikidwa poyela pamaso pa khamu laanthu; ndipo mmodzimodzi wa iwo, ndinkhope zakugwa ndimaso oyang'ana pansi, anachoka pamalopa, ndikusiya munthu olakwa wawo limodzi ndi mpulumutsi wachisoni." – *Ibid.*

**c. Muchina chili chonse, Kodi ndi chiyani chimene ife tonse tikuyenera kuphunzira kuchokela kumawu a Yesu kwa oneneza? Luka 6:42.**

"Pali anthu amene ali osakhwima mukhumbo lawo lakukonzanso zinthu zimene kwa iwo zimaoneka zolakwika. Iwo amaganiza kuti iwo akuyenera kusankhidwa kuti atenge malo aiwo amene apanga zophophonya. Iwo amapeputsa zimene ogwira ntchito amenewa anachita pamene ena amangoyang'ana ndikutsutsa moweludza. Kudzera mmachitidwe awo iwo amati, 'Ndingathe ine kuchita zinthu zazikulu. Ndingathe ine kupititsa ntchito patsogolo ndichipambano.' Kwa iwo amene amaganiza kuti akuziwa bwino kwambiri mmene angapewele zolakwitsa, ine ndinalamulilidwa kuti ndinene kuti, 'musaweludze,kuti mungaweluzidwe.' Mateyu 7:1. Inu mungathe kupewa zolakwitsa muzinthu zina, koma muzinthu zina muli ndikuthekera inu kwakupanga zolakwika zazikulu kwambiri, zimene zizakhala zovuta kwambiri kuzikonza ndipo zimene zizabweretsa chisokonezo muutumiki. Zophophonya zimenezi zizatha kuononga kwambiri kupotsera izo zimene abale anu anachita."-***Testimonies for the Church, vol. 7, p. 279.***

## 3. CHOCHITIKA CHOSAYEMBEKEZELEKA

**Lachitatu, Epulo 29**

**a. Kodi ndifunso lanji limene Yesu anamufunsa Mzimayi atatha kuchoka omuneneza ake-nanga ndimotani mmene njira yake ya kuchitila ndi nkhaniyi ingakakhuzire moyo wake wa mzimayiyu? Yohane 8:10, 11.**

“Mzimayi anaima pamaso pa Yesu, odzazidwa ndimantha. Mawu ake oti, ‘iye amene mwainu ali opanda chimo, ayambe kumponya mwala,’ Anabwela kwa iye ngati chigamulo cha imfa. Iye sanayelekeze kutukula maso ake kuyang’ana nkhope ya Mpulumutsi, Koma mwakachetechete anayembekezera imfa yake. Modabwa iye anaona omuneneza ake akuchoka opanda mawu ndi okhazikitsidwa chete; kenako mau achiyembekezo anafika mmakutu ake,`inenso sindikutsutsa iwe; pita; kuyambila tsopano usachimwenso.’ Mtima wake unasukunulidwa, ndipo, ndi pozigwetsa yekha pamapazi a Yesu, iye analira ndichikondi chake chachiyamiko ndimisozi yowawidwa mtima anavomeleza machimo ake.

“Ichi kwa iye chinali chiyambi cha moyo watsopano, moyo wachiyelo ndi mtendele, wozipereka kwa Mulungu. Mukukweza kwa moyo wakugwa umenewu, Yesu anachita chozizwa chachikulu kwambiri kupotsera kuchilitsa nthenda yaikulu kwambiri yakuthupi; iye anachilitsa nthenda yauzimu imene ili yofikila kuimfa yamuyaya. Mzimayi wolapayu anakhala mmodzi waotsatira ake ozipereka kwambiri. Ndi chikondi chozipereka yekha nsembe iye anaonetsera chiyamiko chake pachifundo chake chakukhululukira. Kwa mzimayi olakwitsayu dziko linali ndi chiweluzo ndi kunyoza basi, koma Osalakwayo anamvera chisoni kufooka kwake ndipo anamuyandikira iye ndikumutambasulira dzanja la chithangato. Amene Afalisi achinyengo anatsutsa, Yesu anamulamulira iye kuti, `pita, kuyambira tsopano usakachimwenso.’”- The Ministry of Healing, p. 89.

“Mumchitidwe wake wakukhululukira mzimayiyu ndikumulimbikitsa iye kuti akhale moyo wabwino, khalidwe la Yesu linawala ponseponse mukukongola kwa chilungamo chodzadza. Pamene Iye sabvomeleza chimo, kapena kuchepetsa kuipa kwachimo, iye amafunitsitsa osati kususa, koma kupulumutsa. Kwa mzimayi wolakwayu dziko linali ndi kusutsa ndi kunyodza basi; koma Yesu akuyankhula mawu achitonthozo ndi chiyembekezo.*”- The Desire of Ages, p. 462*

**b. .Fotokozani zotsatira zachisomo chopulumutsa cha Khristu. Luka 7:37-40, 47, 48.**

“Yesu amadziwa zochitikachitika zamoyo winaulionse. Monga Kukula kwa kuipisisa kwa ochimwa momwemonso ndi momwe amafunira mpulumutsi. Mtima wake wachikondi ndi chisoni cha Umulungu ukukoka koposa wina aliyense iye amene ndiosowelatu thandizo ogwidwa mmisampha ya mdani.

Ndimwazi wa iye yekha iye anasindikiza chizindikiro pamapepala akumasula mtundu waanthu.”-***The Ministry of Healing, pp. 89-90.***

## 4. CHITONTHOZO CHIFALIKILA PONSEPONSE

**Lachinayi, Epulo 30**

**a. Kodi khalidwe lathu likuyenera kukhala lotani, makamaka pochita ndi ena-nanga kodi izizi zingatheke bwanji kokha? 2 Akolinto 1:3-5**

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

"Zochitikachitika zili ndi gawo lochepa chabe mokhuzana ndi zodusamo za moyo. Ndi mzimu umene umakondwereredwa umene umakongoletsa machitidwe athu onse. Munthu amene ali pamtendere ndi Mulungu komanso ndi anthu anzake sangakhumudwitsike. Msanje sizakhala mumtima mwake; zoneneza zoipa sizizapeza malo mmenemo; udani sungakhalepo. Mtima umene uli mumgwirizano ndi Mulungu umakwezedwa pamwamba pa zokhumudwitsa ndi mayesero a moyo uno*."-Testimonies for the Church, vol. 5, p. 488.*

"Ndikudzera mmasautso kuti Yesu anapedza utumiki wachitonthodzo. Mumasautso onse aumunthu iye amasautsika; Ndipo 'madzunzo awo onse iye anazunzidwa,pakuti popeza ananva zowawa poyesedwa yekha, akhoza kuthandiza iwo amene ayesedwa.' Yesaya 63:9; Ahebri 2:18. Muutumiki uwu moyo ulionse umene walowa muchiyanjano chamatsautso ake uli ndi mwayi wakugawana nawo." ***-Thought from the Mount of Blessings, p. 13.***

**b. Fotokozani mwayi ndi chiyembekezo chapadela chimene ife tili nacho mukusatira mapazi a Khristu. 2 Akolinto 1:6, 7.**

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

"Ngati inu simuzinva mumtima mwanu kuti anakulemekezani kuti mukhale otenga nawo gawo a masautso a Khristu; Ngati simuchinva kukhala cholemetsa chamoyo cha zaiwo amene ndiokonzeka kuonongeka; ngati inu simuli ofuna kupereka nsembe kuti mukathe kusunga chuma cha ntchito imene iyenera kuti igwiridwe, sikumuzakhala malo anu muufumu wa Mulungu. Tikufunika ife kukhala otenga nawo mbali ndi Khristu a masautso ake ndikuzikaniza wekha kwake pakhwerero lina lililonse."- ***Tetsimonies for the Church, vol. 9, pp. 103, 104.***

**c. Fotokozani khalidwe labwino limene likufunikira kwambiri pakati pa okhulupilira muuthenga wa angelo atatu. 1 Akolinto 13:13,4-8**

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

"Makhalidwe amene akufunikira kwambiri kuti azikuzidwa ndi anthu a Mulungu osunga malamulo ndi chipiliro ndi kuledza mtima, mtendere ndi chikondi. Pamene chikondi chikusowa, kuludza kwakukulu kumachitika."- ***Ibid., vol. 6, p. 398.***

## 5. KUBWEZELETSA KWA CHIFUNDO **Lachisanu, Meyi 1**

**a. Kodi ndimotani mmene okhulupirira owona amachitila ngati mkhristu wagwera muuchimo-mosiyana ndi mmene okhulupilira amitima yonyenga kawirikawiri amachitira? Agalatiya 6:1-3; Aroma 15:1-3.**

---

"Chiikeni mumtima mwanu kuti ntchito yakubwezeretsa ikuyenera kukhala cholemetsa chathu. Ntchito imeneyi siikuyenera kuchitidwa munjira yonyada, yozikweza, yaulamuliro. Musamanene inu, kudzera mmachitidwe anu kuti, 'ndili ndi mphanvu, ndipo ine ndizigwiritsa ntchito zimenezo,' ndikumafotokoza zoneneza zambirimbiri kwa munthu wolakwitsayo. Gwirani ntchito yanu yakubwezeretsa `Muuzimu wachifatso; ndikuzipenyerera wekha, ungayesedwe nawenso.' Ntchito imene tapatsidwa ife kuti tiigwire kwa abale athu sikuwachotsa iwo ndikuwaika pambali, osati kuwapanikizira iwo kupita kukugwetsedwa mphwayi kapena kukukhumudwa kudzera mukumanena kuti.. 'Inu mwandikhumudwitsa ine, ndipo sindiyetsa kukuthandizani inu' Iye amene amazikweza yekha pamwamba ngati ozaza ndi mzeru ndi mphanvu, ndikumapepusa iye amene waphinjika ndikukhala ndi nkhawa ndikumafunitsitsa thandizo, akuonetsera mzimu wa mfalisi, ndipo wazitsokera yekha mwinjiro wakulemekezeka kozipangira yekha. Muuzimu wake iye amathokoza Mulungu kuti sali ngati anthu ena, ndipo amaganiza kuti machitidwe ake ndioyamikilidwa kwambiri ndikuti iye ndiwamphanvu kwambiri kuti angayetsedwe. Koma `Ngati wina ayesa ali kanthu pokhala ali chabe, azinyenga yekha.' vesi 3."-***Testimonies for the Church, vol. 6, pp. 398,399.***

"Siotsatira Khristu amene, ndimaso otseka mwadala, amatembenuka kuchoka kwa olakwitsa, kuwatsiya iwo osawatsokonedza kuti atsatire njira yawo yopita pansi kuchionongeko. Iwo amene amakhala patsogolo mukuneneza ena, ndikukhala achangu mukuwabweretsa iwo muchiweludzo, kawirikawiri mmiyoyo yawo amakhala olakwa kwambiri koposa iwo aja. Anthu amadana ndi ochimwa, pamene iwo akukonda uchimo. Khristu amadana ndi uchimo, koma amakonda ochimwa. Uwu udzakhala mzimu waonse amene amamutsatira iye. Chikondi cha chikhristu ndichochedwa kutsutsa, chachangu kuzindikira kulapa, chokonzeka kukhululukira, kulimbikitsa, kukhazikitsa osochera munjira yachiyero, ndikukhazikitsa mapazi ake mmenemo." - ***The Desire of Ages, p. 462.***

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA **Lachisanu ndi chimodzi, Meyi 2**

1. Fotokozani msampha umene Alembi ndi Afalisi anamukonzera khristu.
2. Kodi ndimotani mmene Ayuda achinyengo anaonetsera kulemekedza kwabodza lamulo?
3. Kodi ndichiyani chimene Ayuda oneneza anakakamizidwa kuti avomeleze zokhuza iwo eni?
4. Fotokozani chiyembekezo chimene chinaperekedwa kwa mzimayi olakwa amene amachitidwa moyipa.
5. Kodi ndimotani mmene ine ndingakhalire monga Yesu pamene ndikuchita ndi moyo wolakwa?

**SABATA MEYI 10, 2025**

**PHUNZIRO 6**

# YESU, KUUNIKA KWA DZIKO LAPANSI

**VESI LOLOWEZA: "Pamenepo Yesu analankhulanso nao, nanena, Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; iye wonditsata Ine sazayenda mumdima, koma adzakhala nako kuunika kwa moyo" (Yohane 8:12).**

**Zowelenga Zoonjezera: Testimonies for the Church, vol. 1, pp. 405-409.**

**"Monga momwe mwedzi ndi nyenyezi zomwe zili mauniko athu zimawalira kudzera mu kuwala kochokera ku dzuwa, choteronso, ngati chiphunzitso chao chili choonadi, ndi momwe anthu anzeru zakuya a kudziko lapansi amawalitsira milezo ya Dzuwa la Chilungamo. Lingaliro lina lililonse, kutwanima kwa nzeru, ndi zochokera ku Kuunika kwa Dziko Lapansi." – Education, p. 14.**

## 1. KUBWEZERETSA CHILENGEDWE

**Loyamba, Meyi 4**

**a. Kodi ndi chiyani chimene Mulungu analenga pa tsiku loyamba la kulenga? Genesis 1:3-5.**

---

"Pa liwu lakulenga pachiyambi, kuunika kunawalira kuchoka mundima." – *The Desire of Ages, p. 464.*

**b. Kodi ndi ndani amene analipo pakulengedwa kwa dziko lapansi- osati monga ongoonerera chabe, koma monga otenga nawo gawo mukulenga? Genesis 1:1, 2; Yohane 1:1, 2; Akolose 1:16.**

---

"Pachiyambi, Mulungu amabvumbulutsidwa mu nchito zonse za kulenga. Ndi Khristu amene anayala thambo, ndi kuika madziko a dziko lapansi…Ndi Iyeyo amene anazaza dziko lapansi ndi zokongoletsa, ndi kuzaza mlenglenga ndi nyimbo. Ndipo pa zinthu zonse za padziko , ndi za mlengalenga, ndi za mu mpweya, Iye analembamo uthenga wa chikondi cha Atate."- *Ibid., p. 132.*

"Dzanja limene limagwirizitsa maiko mlengalenga, dzanja limene limagwira zinthu zonse mwadongosolo ndi mosatopa kumayendetsa zochita zonse za muchilengedwe chonse cha Mulungu, ndi dzanja lomwelo limene linakhomeledwa pa mtanda chifukwa cha ife." – *Education, p. 132*.

**a. Kodi ana a Isalayeli amasongoloreredwa motani mu chipululu? Eksodo 13:21, 22.Fotokozani amene anaphimbika mu mtambo njo ndi mmotonjo? Eksodo 13:21 (mbali yoyamba); 1 Akorinto 10:1-4.**

"Mukuonekera kwa Mulungu kwa anthu ake, kuwala kwakhala nthawi zonse kwakhala kuli chizindikiro cha kupezeka kwake. Pa mau akulenga pa chiyambi, kuunika kunawala kuchokera mundima. Kuunika kunaphimbidwa mu ntambonjo masana ndi mumoto njo usiku, kutsogolera khamu lalikulu la israyeli." – ***The Desire of Ages, p. 464.***

**b. Kodi zinalembedwa zotani zokhuza kupedzeka kwa Khristu ndi ana a Israyeli muchipululu – nanga kodi ndi chitetezo chanji chimene Mulungu anachilonjeza kwa anthu ake? Masalimo 105:39; Yesaya 4:5, 6.**

"Mu limodzi mwa malembo okongola ndi otonthoza kwambiri a uneneri wa Yesaya, akunena za mtambo njo ndi moyo njo kuimirira chisamaliro cha Mulungu kwa anthu ake mu kulimbana komaliza ndi mphamvu za zoipa." – ***Patriarchs and Prophets, p. 283.***

**c. Kodi ndi motani mmene Khristu anazionetsera yekha pa Sinai – nanga kodi ndi motani mmene Mose ndi anthu anachitira? Eksodo 19:16-18; 20:18,19; Aheberi 12:21**

"'Ulemelero wa Mulungu unali ngati moto wonyeketsa pamwamba pa phiri' pamatso pa khamu limene linasonkhana…Zionetsero za Yehova zinali zoopsa kwambiri kotelo kuti khamu la Israeli linanjenjemera ndi mantha, ndipo anagwetsa nkhope zawo pansi pamaso pa Ambuye"- ***Ibid., p. 304.***

"Ulemerero unali waukulu kwambiri wakuonekera kwa Khristu kotelo kuti sizikanatheka kuti munthu wakuthupi athe kuyang'anapo. Mose, amene anali wokondeleledwa kwambiri ndi Mulungu, anafuula kuti 'ndili ndi mantha aakulu koposa'. Koma mulungu anamulimbikitsa iye kuti apilire ulemelero waukulu umenewo, ndikubweletsa kuchokela mphiri kunyezimilira kwaulemerero pa nkhope pake kotelo kuti anthu sanathe kuyang'anitsitsa pa iwo.*"- **Sons and Daughters of God, p. 225.***

**a. Kodi ndimotani mmene Khristu amaonetsera kupedzeka kwake Muchihema? Ekisodo 40:34, 35.**

---

"Ndi chidwi chachikulu khamu lalikulu la Israeli linasonkhana kuzungulira kuti lione chomangidwa chopatulika. Pamene iwo anali kulingalira zachochitikachi ndi kukhutitsidwa kwakukulu, mtambo unatsika ndikuvindikila chihema.`Ndipo ulemerero wa Ambuye unadzadza muchihema.'Panali kubvumbulutsidwa kwa olemekezeka wa umulungu, ndipo kwakanthawi ngakhale Mose sanathe kulowamo. Ndi mantha aakulu anthu anayang'ana chizindikilo choti ntchito ya manja awo inalandilidwa. Panalibe mfuwu owonetsera chimwemwe. Bata lopatulika linakhala pa onse. Koma kusangalala kwa mmitima yawo kunaonekela mmisozi yachimwemwe ndipo iwo anang'ung'uza pansipansi, mawu otsimikizika achiyamiko oti Mulungu watsika kuti adzakhale pamodzi ndi iwo.***"- Patriachs and Prophets, pp. 349,350.***

"Pamwamba pa mpando wachisomo panali Shekina, kuonetseredwa kwa kupedzeka kwa umulungu; ndipo kuchokela pakati pa Akelubi, Mulungu amadzindikilitsa chifuniro chake. Mauthenga a Mulungu nthawi zina amapelekedwa kwa wamsembe wamkulu kudzera mmawu ochokela mumtambo. Nthawi zina kuwala kumagwa kuchokela kwa ngelo wakuzanja lamanja, kuonetsera kubvomeleza kapena kulandila, kapena mthuzi kapena mtambo umagwela paiye wakudzanja lamamzere kuonetsera kukana kapena kusabvomeleza " – ***Ibid.***

**b. Kodi ndi chiyani chimene chinachitika patadutsa nthawi, munthawi imene kachitsi amapatulidwa? 2 Mbiri 7:1.**

---

"Chihema cha ulemelero kwambiri chapangidwa, molingana ndichisanzo chimene chinaonetsedwa kwa Mose mphiri, ndipo kenako kuonetseredwa ndi Ambuye kwa Davide. Kachisi wapadziko lapansi anapangidwa mofanana ndi wakumwamba. Kuphatikiza akelubi omwe anali pamwamba palikasa, Solomoni anapanganso angelo ena awiri okulilanso, wina aliyense anaima pambali pa likasa, Kuimilira Angelo akumwamba amene nthawi zonse amateteza lamulo la Mulungu. Ndizosatheka kufotokoza kukongola ndiulemerero wa kachisi ameneyo. Mmenemu, monganso mkachisi, Likasa lopatulika linaikidwa pamalo polemekezeka kwambiri, pansi pamapiko aakelubi awili amene anaima mbali zonsezonse.

"Oimba nyimbo zopatulika analumikiza mawu awo, ndi zida zoimbila za mitundu yonse, mukuyamika Mulungu. Ndipo pamene mawu ogwirizana ndi zida zoimbila nyimbo, amanveka modzadza kachisiyu, ndikumanveka muYelusalemu monse, mtambo waulemelero wa Mulungu unasikila ndikukhala mnyumbayi, monga mmene mbuyomuja unazazira muchihema. 'ndipo chinachitika, kuti pamene ansembe anatuluka kuchoka mmalo opatulika, mtambo unadzadza mnyumba ya ambuye, kotelo kuti ansembe sanathenso kuima kuti atumikile chifukwa cha mtambo,pakuti ulemelero waambuye unadzadza mnyumba ya Yehova.'"***-Spritual Gifts, vol 4a, pp. 113,114.***

**a. Kodi ndiuthenga wanji wa Khristu mu Yohane 8:12 umene ukubweletsa chiyembekezo chachikulu kwa ife?**

---

"Siazibusa ophunzira kwambiri amene ali ndikumvetsetsa kwa choonadi chimenechi, ndikugwilitsidwa ntchito mukuchilalikira icho. Ngati awa akanakhala alonda okhulupilika kufufuza malembo mwapemphero ndi mwakhama, Iwo akanatha kuziwa nthawi yautsiku; mauneneri akanatha kusegulidwa kwa Iwo zochitikachitika zimene zinali pafupi kuti zichitike, koma iwo samagwira ntchito imeneyi, ndipo uthenga unapelekedwa kudzera mwa anthu ozichepetsa… Iwo amene atembenuka kuchoka kukuniika kumene Mulungu wakupeleka, kapena amene anyozera kufunafuna kuunikako pamene kuli pafupi ndiiwo, amasiidwa mumdima." ***– The Great Controvesy, p. 312.***

"Ambuye anapanga chikonzero chinachilichonse kotelo kuti ife tikathe kukhala ndichiziwitso chachimwemwe, chichikulu ndi chozaza.Yohane akulemba zokhuzana ndi Khristu, kuti, 'mwa iye munali moyo; ndipo moyowo unali kuunika kwaanthu.' Moyo ukulumikizana ndi kuunika, ndipo ife ngati tilibe kuunika kochokela ku Dzuwa la Chilungamo, sitingathe kukhala ndi moyo mwa iye. Koma kuunikaku kunapelekedwa kuti kukakhale kwa moyo wina ulionse, ndipo ndipokhapokha pamene ife tikupatuka kuchoka kukuniika kuti mdima umabwela kwa ife. Yesu anati, 'Iye amene akundisatila ine sazayenda mumdima, koma azakhala nako kuunika kwamoyo.' Motizungulira ife mudziko lapansi simungakhale moyo popanda kuunika. Ngati dzuwa lingachotse kuwala kwake, mbewu zonse, moyo wa nyama zonse uthera pomwepo. Ichi chikuonetsera choona choti ife tingathe kukhala nawo moyo wauzimu pokhapokha ife titaziika tokha pansi pamiledzo la Zuwa la Chilungamo. Ngati ife tingaike mtengo wamaluwa muchipinda cha mdima, iwo mwachangu unyala ndikufa; ndipo chotelo ife tingathe kukhala nawo kamoyo ka uzimu, komabe kuutaya kudzera mukukhala mmalo odzungulilidwa ndi kukaika ndi kukhumudwa."***- Sons and Daughters of God, p. 281.***

**b. Kodi ndi chitsimikizo chanji chimene chikubwela pamene ife tikutembenukira kwa Khristu? 2 Akolinto 3:18.**

---

"Monga momwe duwa limatembenukila kudzuwa kotelo kuti miledzo yake yowala ikathe kuthandizira mukukongoletsa kukongola kwake ndimaonekedwe ake, Chotelo otsatila Akhristu akuyenera kutembenukira ku Dzuwa la Chilungamo, kotelo kuti kuunika kwa kumwamba kukathe kuwalira pa iwo kuyeretsa makhalidwe awo, ndikuwapatsa iwo chiziwitso cha kuya ndichokhazikika muzinthu za Mulungu. Ndichoposa mphanvu zathu kuzindikila madalitso amene abweletsedwa chifupi ndiife kudzera mw a Khristu, koma pokhapokha ngati ife tingalumikize kuyetsetsa kwathu kwa umunthu ndi chisomo cha umulungu."***-Ibid p. 26***

"Wina aliyense amene ali ndi cholinga chimodzi chokha chakufunafuna kuchita chifunilo cha Mulungu, moona mtima kumasatila kuunika kumene kwapelekedwa, adzalandira kuunika kwakukulu; kumoyo umenewu nyenyezi inayake ya kuwala kwakumwamba izatumizidwa kuti izimutsogolera iye muchoonadi chonse."***-The Great Controversy, p. 312.***

## 5. KUWALILA MITIMA YATHU

**Lachisanu, Meyi 8**

**a. Kodi ndimotani mmene ife tingakwezedwe pamwamba kuzera kukufotokoza kolimbikitsa kwa Paulo kokhuza kuunika kwadziko lapansi? 2 Akolinto 4:6.**

---

---

"Lolani kuti malingaliro a ulemerero a Mulungu adzaze mu mtima wanu. Lolani kuti moyo umangililidwe pamodzi ndi zingwe zobisika kumoyo wa Yesu. Iye amene analamulila kuti kuwala kuwalire kuchoka mumdima ndiofunitsitsa kuti awalire mmitima yanu, kuti apeleke kuunika kwa chiziwitso chaulemelero wa Mulungu pankhope pa Yesu Khristu. Mzimu woyela uzatenga zinthu za Mulungu ndikuzionetsa izo kwa inu, kuzisamutsila izo monga mphanvu za moyo kupita nazo mumtima womvela. Khristu azasogolera inu kupita nanu kumsipu wamuyaya, muzaona ulemelero kupyola chophimba, ndikumbvumbulutsa kwa anthu kukwanila kwa Iye amene ali ndi moyo chikhalire kutipembezera ife." – ***Christ's Object Lesson, p. 149.***

"Kubvumbulusidwa kwa ulemelelo wake muthupi la umunthu zizabweletsa kumwamba pafupi kwambiri ndi anthu kotelo kuti kukongola konyezimila kwa mkati mwa kachisi kuzaonekela mmoyo wina ulionse umene Khristu Mpulumutsi akukhalamo. Anthu azakopeka ndiulemelero waKhristu wokhala mkati. Ndipo mumiledzo yachiyamiko ndi kuthokoza kuchokela mumiyoyo yambili imene yapindulidwa mwa Mulungu motelemu, ulemelero uzasefukila ndikupita kwa opeleka wamkulu.

'Nyamuka, wala pakuti kuunika kwako kwafika, ndi ulemelero wa Yehova wakutulukira.' Yesaya 60:1. Kwa iwo amene akupita kukakumana ndi mkwati uthenga uwu unapelekedwa. Khristu akubwela ndi mphanvu ndiulemelero waukulu. Iye akubwela ndiulemelero wa Iye mwini komanso ndiulemelero wa atate. Iye akubwela ndi angelo onse oyela pamodzi ndi Iye. Pamene dziko lonse lapansi lazazidwa ndi mdima, padzakhala kuunika konsekonse pamene akukhala olungama. Iwo adzaona kuunika koyambilira kwakubwela kwake kwachiwili. Kuunika kosadetsedwa kuzawalira kuchokela mmaonekedwe ake aulemelero, ndipo Khristu mombolo azasililidwa ndi onse amene anamutumikila iye. Pamene oyipa azathawa kuchoka pamaso pake, otsatila a Khristu azakondwera."- ***Ibid., pp. 420,421.***

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

**Lachisanu ndi chimodzi, Meyi 9**

1. Kodi ndi motani mmene Baibulo limaphuzitsira zokhuzana ndi umulungu muntchito ya kulenga?
2. Fotokozani mmene Yesu anazionetsera mwini yekha kwa anthu ake Muchipululu.
3. Kodi ndi motani mmene kuunika kwa Yesu kunawalira muchihema ndi mukachisi?
4. Fotokozani mmene Yesu anazionetsera mwini Yekha mukupatulidwa kwa kachisi.
5. Kodi ndi motani mmene Khristu amazibvumbulutsila mwini yekha kwa ife ndikudzera mwa ife?

SABATA, MEYI 17, 2025

PHUNZIRO 7

# KUUNIKA KOKANIDWA – KAPENA KOWUNIKIRIDWA?

**VESI LOLOWEZA: "Yehova ndiye kuunika kwanga ndi chipulumutso changa; ndizaopa yani?" (Masalimo 27:1).**

**Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, vol. 7, pp. 18-28.**

**"Khristu ndi kuunika, kumene kumawalira munthu wina aliyense amene amadza mu dziko lapansi.' Yohane 1:9.Monga mmene kudzera mwa Khristu munthu wina aliyense amakhala ndi moyo, chotelonso kudzera mwa Iye moyo ulionse umalandira miledzo ina yake yakunika ya umulungu."- Education, p. 29.**

## 1. KUUNIKA KOLOSELEDWA

**Loyamba, Meyi 11**

**a. Kodi ndi motani mmene Mzimu Woyera umafotokozera za Yesu kudzera mwa Yesaya? Yesaya 49:6.**

---

**b. Kodi ndi motani mmene Simioni anamuzindikirira Yesu pa nthawi imene iye anabweretsedwa kukachisi kuti adzapatulidwe - Nanga kodi zimenezi zingatipangitse ife kulingalira chiyani? Luka 2:32.**

---

"Simioni wokalamba, analankhula za Khristu monga 'Kuunika kowalira amitundu, ndi ulemelero wa anthu anu Israeli,' mukachisi mmene khristu tsopano amaphuzitsa. (Luka2:32). Mmawu amenewa Simeoni anali akukwanilitsa kwa Iye uneneri umene unali odziwika kwa Israyeli yense. Kudzera mwa mneneri Yesaya, Mzimu Woyera unalalikira kuti, 'inde, ati, chili chinthu chopepuka ndithu kuti iwe ukhale mtumiki wanga wakuutsa mafuko a Yakobo, ndi kubwezera osungika a Israeli; ndizakupatsanso ukhale kuunika kwa amitundu, kuti ukhale chipulumutso changa mpaka ku malekezero adziko lapansi.' Yesaya 49:6. Uneneri uwu umamvetsetsedwa bwino lomwe kuti umakamba za Mesiya, ndipo pamene Yesu amati, 'Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi,' anthu sakanalephela kudzindikira kuzinena kwake kukhala wolonjezedwayo." – ***The Desire of Ages, p. 465.***

"Oh, ndi phunziro lanji ili la nkhani yodabwitsa ya ku Betelehemu! Mmene imadzuzulira kutsakhulupilira kwathu, kunyada kwathu ndi kudzimva kukwanila kwathu kwa undekha. Ndi motani mmene imatichenjezera ife kukhala otsamala, kuti mwina kudzera mu mphwayi zathu za uchimo tikhonza nafenso kulephera kudzindikira zidzindikilo za nthawi, ndi kukhalanso otsaziwa tsiku la kuyendeleledwa kwathu."-***The Great Controversy, p. 315.***

**a. Kodi ndi motani mmene azitsogoleri achiyuda anachitila ndi utumiki wa Khristu? Yohane 1:11; 8:13.**

“Moyo wake wonse wa Khristu komanso ndi kuphunzitsa kwake, zinali maphunziro opitilira akuzichepetsa, akuchita zinthu zabwino, akhalidwe lokoma, ndi odzikaniza wekha. Ichi chinali chidzudzulo chopitilira kwa Ayuda amene amaonetsa mzimu odzilungamitsa, ndi waliuma opanda chifundo. Satana anawatsogolera iwo kufikizana anayamba kuoneka kuti amazunguzika wina akangonena za ntchito zodabwitsa za Khristu, zimene zimapangitsa kuti anthu achotse chidwi chawo kwa ayudawa ndi kupita kwa Khristu. Ndipo kwanthawi yaitali anazipanga mwa iwo okha kukhulupirira kuti anali wachinyengo womanamizira kuti ndi Mesiya, ndipo njira ina iliyonse imene angaigwiriste ntchito kuti amuchotse iye izakhala nchito yabwino kwa iwo.” – ***Spiritual Gifts, vol, 4a, p. 117.***

**b. Kodi ndi kufotokozera komveka bwino kotani kumene Yesu anakupereka kwa Afalisi osakhulupilirakomabe kodi ndi motani mmene iwo anayankhira? Yohane 8:14-18.**

“(Afalisi) anali ndi umbuli okhudzana ndi khalidwe la umulungu la Khristu ndi utumiki wake chifukwa choti iwo samafufuza mauneneri okhudzana ndi Mesiya, monga mmene unalili mwayi wawo ndi udindo wawo kutelo. Ndipo iwo analibe kulumikizana kulikonse ndi Mulungu komanso kumwamba, ndipo ndichifukwa chake sanazindikile ntchito ya Mpulumutsi wa dziko lapansi, ndipo ngakhale analandira umboni otsimikizika oti Yesu ndiye Mpulumutsi, komano anakana kutsegula malingaliro awo kukumvetsetsa. Poyambilira pomwe anaika udani mmitima mwawo otsutsana ndi iye, ndi kukanitsitsa kukhulupilira umboni wa mphanvu kwambiri wa umulungu wake, ndipo zotsatira zake, mitima yawo inapitilira kuumitsitsa ndi kufikizana poti anazitsimikizira okha kuti sangamukhulupilire Iye kapena kumulandira Iye.”- ***The Spirit of Prophecy, vol. 2, pp. 334,355.***

**c. Kodi ndi kusiyana kwakukulu kotani kumene Yesu anakufotokoza kumene kulipo pakati pa Iye ndi Afalitsi otsakhulupilira aja? Yohane 8:19-23.**

**d. .kodi ndi chiyani chimene chizakhala chotsatila choopsa kwambiri cha kukana Khristu kwa azitsogoleri achiyuda? Yohane 8:24; Mateyu 23:38.**

## 3. MAGULU AWIRI OMVETSERA

**Lachitatu, Meyi 13**

**a. Atatha kuchenjezedwa kuti iwo adzafa mmachimo awo, kodi ndi chiyani chimene Afalisi analamulira Yesu kuti awachitile, nanga chifukwa chiyani? Yohane 8:25 (mbali yoyamba).**

---

---

"Pooneka ngati anyozera mawu ake ,iwo anamufunsa iye, 'Kodi ndinu yani?' Anachichita chinthuchi pofuna kumukakamiza iye kuti adzinene yekha kuti ndi Khristu. Maonekedwe ake ndi ntchito yake zinali zosiyana kwambiri ndi zimene anthu amayembekezera, ndipo izi zinapangitsa adani ake kukhulupirira kuti Kulankhula kwake poyankha funso lija mwachindunji kuti Iye ndi Mesiya zipangitsa kuti anthu amukane Iye ndi kumutenga ngati munthu wachinyengo." – ***The Desire of Ages, p. 465.***

**b. Kodi ndi motani mmene Mpulumutsi anawayankhira iwo- pobvumbulutsa kulumikizana kwake kodabwitsa ndi Atate? Yohane 8:25 (Mbali yomalidza), 26-29.**

---

---

"Khristu sanapatukepo ku kumvera ku mfundo za malamulo a Mulungu. Ndipo sanachitepo kanthu kalikonse kosemphana ndi chifuniro cha Atate wake. Pamaso pa angelo, anthu, ndi ziwanda Iye akhonza kulankhula mawu amene ngati angachokere pa kamwa pa munthu wina aliyense akhala kuchitira Mulungu mwano: 'Ndichita Ine zimene zimkondweretsa Iye nthawi zonse.' Yohane8:29. Tsiku ndi tsiku kwa dzaka zitatu adani ake anamutsatira iye, kuti ayesetse kupedza kadontho kenakake kolakwika mukhalidwe lake; Satana pamodzi ndi gulu lake lonse la zoipa, anayesesa kuti amugonjetse Iye; koma analephera kupedza kanthu ngakhale kamodzi mwa iye kuti apezerepo mwayi. Ngakhale ziwanda zinakakamizika kuti zichite umboni kuti: 'khristu analidi woyera yekhayo wa Mulungu.'"-***Testimonies for the Church, vol.8, p. 208.***

**c. Fotokozani mmene Khristu amayendela ndi Atate tsiku ndi tsiku- ndi mmene ife tingamaonetsere moyo womwewo? Yohane 15:10; Aefeso 2:4-6.**

---

"Monga mmene Yesu analili mukhalidwe la umunthu, Chotelo Mulungu amafuna kuti omutsatira ake ayenera kukhala choncho. Tikuyenera ife kumakhala kudzera mumphanvu yake moyo wa chiyero ndi wangwiro umene mpulumutsi anakhala.'-***Ibid., p. 289.***

"Moyo wa mpulumutsi pa dziko lapansi ngakhale anaukhala pakati pa mkangano, unali moyo wa mtendere. Ngakhale adani ake okwiya amamulonda Iye kosalekedza, Iye anati `Iye amene ananditumа ine ali ndi ine: Atate sanandisiye ine pandekha; popedza nthawi zonse ndimachita zinthu zimene zimamukondweretsa iye.' Yohane 8:29. Panalibe namondwe wa anthu kapena mkwiyo wa Satana umene ukanatha kusokonedza bata la kulumikizana kwake kwa ngwiro ku ndi Mulungu."-***Thoughts from the Mount of Blessings, pp. 15, 14.***

**a. Pamene khristu amalankhula choonadi chenicheni chakuthwa kwa Afalisi, kodi ndi motani mmene mawu Ake amakhudzira anthu oona mtima amene amamumvetsera-nanga ndi chifukwa chaiyani zinthu ngati izi zingatilimbikitse ife lero? Yohane 8:30.**

---

---

"Khristu amaziwa mmene anagachitile modekha, ndi mwa mzeru, ndi kulepheretsa upo wa adani ake woti amubweretse iye kuciweruzo chomutsutsira iye. Mawu a Ambuye anali ngati mivi yokuthwa imene imayenda mwachindunji kupita kumene yalodza, ndipo amavuladza mitima ya iwo amene amamuneneza iye. Nthawi zonse pamene Khristu amalankhulana ndi anthu, kaya omvetserawo akhalapo ambiri kapena pang'ono, mawu ake amakhala ndi mphamvu zopulumutsa pa miyoyo ya anthu ena amene amamumvesera. Palibe uthenga umene unatuluka pa kamwa pa Khristu umene umayenera kungotaika chabe. Mawu alionse amene Iye walankhula amaika udindo watsopano paiwo amene awanva mawuwo. Azibusa amene akupereka uthenga otsiliza wa chifundo kudziko lapansi, amene akupereka choonadi moona mtima amene amadalira kotheratu pa Mulungu kuti awapatse mphanvu, sakuyenera kuopa konse kuti kulimbika kwawo ndi kopanda ntchito. Munthu wina asanene kuti muvi wa choonadi sungathe kupyoza pofikilapo, ndi kukalasa miyoyo ya iwo amene akumvetsera . Ngakhale diso la Munthu silingathe kuona kuyenda kwa muvi wa choonadi, ngakhale khutu la munthu silingathe kumva kulira kwa moyo ovulazidwa, komano choonadi chimakhala chapyoza mumtima mwake mwakachetechete. Mulungu amalankhula ndi moyo ulionse, ndipo pa tsiku lomaliza lotseka mbiri mtumiki wa Mulungu adzaima ndi mphoto za chisomo cha chiombolo kuti zipereke ulemu ndi kulemekedza kwa Khristu, amene akuyenera ulemu. Mulungu, amene amaona mtseri, azapereka mphoto moonekera kwa onse amene analalikira choonadi mu dzina lake."-***The signs of the Times, February 6, 1896.***

**b. Pambali pa azibusa, ndi ndani wina amene akudalitsika kudzera mukuunikila ena kuwala kochokela kumwamba? Masalmo 27:1; 147:15; Yesaya 55:10, 11.**

---

"Anthu amene sanaitanidwe kuutumiki akuyenera kulimbikitsidwa kumugwirira ntchito Ambuye molingana ndi kuthekela kwawo kosiyanasiyana. Amuna ndi akazi mazana mazana amene angokhara opanda kuchitapo kanthu ku ntchito ya Ambuye, akhoza kuchitapo utumiki ovomelezeka pamaso pa Ambuye. Kudzera mukutengela choonadi mmakomo aabwenzi ndi anansi awo, akhonza kugwira ntchito yaikulu ya Ambuye. Mulungu alibe sankho. Ndipo iye adzagwiritsa ntchito anthu odzichepetsa, akhristu odzipereka, ngakhale iwo atakhala kuti sanalandile maphunziro okwanira monga amene ena analandilira. Aloleni anthu otelewo kuti alowe muutumiki mukutumikila iye kudzera mu ntchito yakhomo ndi khomo. Pokhala pambali pa moto, iwo akhonza- ngati ali ozichepesa, oganiza bwino, ndi akhalidwe la umulungu kuchita zambiri kukwanitsa kufikila zotsowa zenizeni za mabanja kupotsera mbusa odzozedwa."- ***Testimonies for the Church, vol. 7, p. 21.***

## 5. UKAPOLO KUSIYANITSA NDI UFULU

**Lachisanu, Meyi 15**

**a. Kodi ndi chiyani chimene Yesu analankhula kwa a Yuda amene anamulandira iye? Yohane 8:31, 32. Mosiyana, kodi ndi motani mmene anthu osakhulupilira amalephera kuona chinthu chofunikila chokhacho chimene chingatipangitse ife kumatsulidwa kuuchimo ndi kukhala mfulu? Yohane 8:33-36.**

---

---

"(Afalisi) anali muukapolo oyipitsitsa ndi omvetsa chisoni- omalamuliridwa ndi mzimu oyipa.

"Moyo ulionse umene umakana kuzipereka okha kwa Mulungu umakhala pansi pa ulamuliro wa mphanvu zina. Ndipo munthuyo samakhala wa iye yekha. Akhonza kumalankhula za ufulu komano iye mwini ali muukapolo wa zaoneni. Ndipo iye samaloredwa kuti awone kukongola kwa choonadi, popeza malingaliro ake ali pansi polamulilidwa ndi satana. Pamene iye angamapange matama kuti iye akutsatira chigamulo cha malingaliro ake, iye amakhala akumvera chifuniro cha karonga wa mdima. Khristu anabwera kuti adzaphwanye maunyolo amsinga za ukapolo wa uchimo kuchoka mmoyo….

"Mu ntchito ya chiombolo mulibemo kukakamizana. Palibe kukakamiza kochokela kunja kumene kumagwiritsidwa ntchito. Pansi pa chikoka cha mzimu wa Mulungu, munthu amasiidwa ndi ufulu kuti asankhe iye amene angamutumikile. Mukusintha kumene kumachitika pamene moyo wozipereka kwa Khristu, umamva ufulu weniweni mumtima. Kuthamangitsidwa kwa tchimo mumtima ndi chochitika cha moyo pachokha. Ndizoonadi, tilibe mphanvu zoti tingazimasule tokha kuulamuliro wa Satana; komano pamene ife tikukhumba kuti timasulidwe kuuchimo, ndipo mukusowa kwathu kwakukulu tikulilira thandizo la mphanvu zochokela kunja kwanthu komanso zoposa zathu, mphanvu za moyo zimapatsidwa mphanvu za umulungu za mzimu woyera, ndipo zimanvera zolamula za chifuniro mukukwaniritsa chifuniro cha Mulungu.

"Choyenereza chokhacho chimene munthu angathe kupezadi ufulu, ndiko kukhala mmodzi ndi Khristu. `Choonadi chidzakumasulani;'ndipo Khristu ndiye choonadi. Chimo likhonza kupambana pokhapokha ngati lagonjetsa ndi kufooketsa malingaliro, ndi kuononganso ufulu wa moyo. Kudzipereka mogonja kwa Mulungu ndi kudzibwezeletsa wekha ku ulemelero weniweni ndi ulemu wa munthu. Lamulo lopatulika, limene ife tonse timabweletsedwa kuti tiligonjere, 'ndi lamulo la ufulu.' Yakobo 2:12." – ***The Desire Of Ages, p. 466,***

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

**Lachisanu ndi chimodzi, Meyi 16**

1. Fotokozani kufunikila kwa mawu a Simioni okhudzana ndi Yesu.
2. Fotokozani zimene Alembi ndi Afalisi amamuchitila Khristu.
3. Kodi ndi chiyani chimene chimayenera kuzachitika ndi dziko lawo chifukwa chakukana Yesu?
4. .Kodi ndi motani mmene miyoyo yoona mtima imachitila ndi uthenga wa Khristu mu nthawi yake komanso pano?
5. Fotokozani tanthauzo la mau oti "Ufulu" mukuunika kwa uthenga wabwino wa choonadi.

**SABATA, MEYI 24, 2025** **PHUNZIRO 8**

# YESU NDI ABRAHAMU

**VESI LOLOWEZA**: "**Atate wanu Abrahamu anakondwera kuona tsiku langa; ndipo anaona, nasangalala" (Yohane 8:56).**

**Zowelenga Zoonjezera: Christ's object Lessons, pp. 269-271, 330-332; Early Writtings, pp. 149-153.**

**"(Abrahamu) anapereka pemphero loona mtima kuti imfa yake isanafike akathe kuona Mesiya. Ndipo iye anaona Khristu."-** ***The Desire of Ages, p. 468.***

## 1. ANA A ABRAHAMU — Loyamba, Meyi 18

**a. Kodi ndi chodziyeneleza chanji chimene Afalisi amachibwereza kuchilankhula? Yohane 8:33, 39 (mbali yoyamba). Komabe kodi chiyani chimene chimatsimikizira ubale umenewu? Yohane 8:39 (mbali yomaliza), 56; Aroma 9:6-8.**

---

---

"Afalisi amazinena okha kuti iwo ndiye ana a Abrahamu. Yesu anawauza kuti kuzinena koteleku kungakhazikitsidwe pokhapokha kudzera mukuchita ntchito za Abrahamu. Ana owoona a Abrahamu, adzakhala monga iye amakhalira, moyo omvera nthawi zonse Mulungu. Ndipo iwo sazayesera kufuna kupha Iye amene akulankhula nawo choonadi chimene chinapelekedwa kwa Iye kuchokera kwa Mulungu. Pochita upo otsutsana ndi Khristu, arabi aja sanali kuchita ntchito za Abrahamu. Popanda kulumikizana kwa uzimu ndi iye, kumene kungazaonetsedwe mukukhala ndi Mzimu ofanana ndi iye, ndi kumachita ntchito zofanana ndi iye,amenewo sangakhale ana ake. "Mfundo iyi imanyamula kulemera komweko kofanana ndi funso limene lakhala likufunsidwa kwa nthawi yaiktali mu dziko la chikhristuli-Funso lokhudzana ndi olowa mmalo mwa atumwi. Kukhala mwana wa Abrahamu kumatsimikizilidwa, otsati ndi dzina kapena ubale wakuthupi, komano kufanana kwa khalidwe. Chotelonso kulowa mmalo mwa atumwi sikukudalira pakungotsamutsa ulamuliro wa mpingo, komano kukukhudzana ndi ubale wa uzimu. Moyo umene unaonetseledwa ndi Mzimu wa atumwi, chikhulupiliro ndi kuphunzitsa kwa choonadi chimene iwo amaphunzitsa, uwu ndiye umboni owona wa mlowa mmalo wa atumwi. Ichi ndi chimene chimawapanga anthu kukhala olowa mmalo aaphuzitsi oyambilira a uthenga wabwino." – ***The Desire of Ages, pp. 466,467.***

**a. Ngakhale Ayuda anali mbumba yeniyeni ya Abrahamu, kodi iwowo anasanduka kukhala ana andani pamene anamukana Khristu? Yohane 8:41-44.**

---

---

"Yesu anakana kuti Ayuda anali ana a Abrahamu. Iye anati, 'Inu muchita ntchito za Atate wanu.' Mwachipongwe iwo anamuyankha, 'Ife sitinabadwe m'chigololo; tili naye Atate mmodzi, ndiye Mulungu.' Mawu awa, polumikizana ndi zochitika za kubadwa kwake, anakonzedwa kuti akhale chida chomutsusira Khristu pamaso pa onse amene anayamba kumukhulupilira iye. Yesu sanalabadire mawu oneneza amwanowa, koma anati, 'Ngati Mulungu akanakhala Atate wanu mukanandikonda ine; popeza Ine ndinatuluka ndi kuchokela kwa Mulungu.' "Ntchito zawo zimachitila umboni za ubale wawo ndi iye amene anali wabodza ndi wakupha. 'Inu atate wanu ndi mdielekezi,' Yesu anatelo, 'ndipo zolakalaka zake za atate wanu mufuna kuzichita. Iye anali wakupha kuyambila pachiyambi, ndipo samaima mu choonadi chifukwa mwa iye mulibe choonadi… koma ine chifukwa ndinena choonadi, simunkhulupilira ine.' Yohane 8:44,45. R.V. Choona choti Yesu amalankhula choonadi ndi kutsimikizika konse, ndi chifukwa chake sanalandilidwe ndi azitsogoleri achiyuda. Chinali choonadi chimene chinakhumudwitsa anthu ozilungamitsa okhawa. Choonadi chimaika poyela zolakwika zonse za chinyengo; ndipo chimatsutsa zophunzitsa zawo ndi machitidwe awo, ndipo chinakhala chotsalandilidwa. Ndipo iwo anachiona chinthu chabwino kuti atseke maso awo kuchoonadi koposera kuti angozichepetsa ndi kuvomeleza kuti ali muzolakwika. Iwo sanakonde choonadi. Ndipo iwo sanachikhumbe icho, ngakhale chinali choonadi." – ***The Desire of Ages, p. 467.***

**b. Kodi ndi chiyani chimene chimatipanga ife kukhala ana a Abrahamu- nanga ndi motani mmene adzitsogoleri a chiyuda anaonetsera kuti sanali ana oona a Abrahamu? Agalatiya 3:6-9; Yohane 8:40.**

---

---

---

"Popedza sitinalandila mzimu wa ukapolo kuti tiziopa; komano tinalandira mzimu wa umwana, 'umene tifuula nawo Abba , Atate.' Mzimu wa ukapolo umabwera kudzera mukufunafuna kukhala molingana ndi chipembezo cha mwambo, ndi kudzera mukuyestetsa kukwaniritsa lamulo mu mphanvu zathu. Pali chhiyembekezo chokhacho kwaife pokhapokha ngati tingabwere pansi papangano la Abrahamu, limene lili pangano la chisomo kudzera mwa chikhulupiliro mwa Khristu Yesu. Uthenga umene unalalikidwa kwa Abrahamu, umene unamupangitsa iye kukhala ndi chiyembekezo, ndi uthenga omwewo umene ukulalikidwa kwa ife lero lino, umene kudzera mwaiwo timakhala ndi chiyembekedzo. Abrahamu anayang'ana kwa Yesu, amene ali woyamba ndi wotsiliza wa chikhulupiliro chathu." – ***The Youth's Instructor, September 22, 1892.***

**a. Kodi ndi funso lanji limene adani ake a Yesu analephera kuliyankha lokhudzana ndi khalidwe lake losadetsedwa? Yohane 8:46 (Mbali yoyamba).**

---

---

"M'moyo wake wa pansi pano, Khristu anakudza khalidwe la ngwiro, ndipo iye anapereka kumvera kwa mbambande ku malamulo a Atate ake. Mukubwera ku dziko lapansi mukhalidwe la umunthu, mukukhala ogonjera kulamulo, mukubvumbulutsa kwa anthu kuti iye anasenza kudwala kwawo, nkhawa zawo, zolakwa zawo, Iyeyo sikuti anakhalano munthu wochimwa. Pamaso pa Afalisi iye amanena kuti, 'Ndani wainu amene anditsutsa ine za chimo?' Panalibe ngakhale kadontho ka tchimo kamene kanapezeka pa Iye. Iye anaima pamaso pa dziko monga nkhosa yopanda banga ya Mulungu." – ***Sons and Daughters of God, p. 25.***

"Yesu anakhala moyo osunga lamulo pamaso pa kumwamba, pamaso pa maiko amene sanagwepo, ndi pamaso pa anthu ochimwa. Ndipo iye amalankhula pamaso pa angelo, pamaso pa anthu ndi pamaso pa ziwanda mopanda omutsutsa, mawu amene akanakhala kuti akuchokera pa kamwa pa munthu wina akanakhala kuchitira Mulungu mwano: 'Ndimachita zinthu zimene zimamutsangalatsa iye nthawi zonse.'" – ***The Desire of Ages, pp. 467,468.***

**b. Kupatula izo zimene Yesu anazilankhula monga mwana wa munthu,kodi ndi chiyani chimene malemba anafotokodza zokhudzana ndi khalidwe la Khristu? Ahebri 4:15; 1 Petro 1:18, 19.**

---

---

"Chikhulupiliro cha anthu mwa khristu monga Mesiya sichikuyenera kukhazikika pa maumboni owoneka ndi maso, kapena kumukhulupilira iye chifukwa cha maonekedwe ake okopa, komano chifukwa cha khalidwe lake la ngwiro limene linapezeka mwa Iye, limene silinayambepo litapedzeka kapena kupedzeka mwa wina aliyense." – ***The SDA Bible Commentary (E.G.White Comments), vol.7. p. 904.***

**c. Kodi ndi motani mmene tingakhuzikile ndi moyo wa Yesu? Afilipi 2:6-8.**

---

---

"Kodi Chitsanzo chathu sichinayende munjira yolimba, yodzikaniza wekha, ndi yodzipereka nsembe, yodzichepetsa mmalo mwathu ndi cholinga chofuna kutipulumutsa ife? Iye anakumana ndi zokhoma, ndi kukumana ndi zokhumudwitsa, ndi kudzunzika ndi chitonzo komanso mazunzo muntchito yake yopulumutsa ife. Nanga kodi tidzakana kusatira kumene mfumu ya ulemerero akutitsogolera ife munjira? Kodi tidzadandaula za mabvuto ndi mayeselo mu ntchito yoti ifeyo tiyenera kugonjetsa mwakuthekela kumene kunapatsidwa kwaife, Pamene tikukumbukila mazunzo a Mombolo wathu? – ***Testimonies for the Church, vol.3, p. 371.***

**a. Kodi cholinga chenicheni cha anthu otsatira Khristu ndi chiyani? 1 Petro 1:13-16.**

---

---

"Ntchito yathu ndiyo kulimbikila kupedza ungwiro mmachitachita athu umene khristu anauonetsera mmoyo wake pa dziko lapansi mmakhalidwe ake onse amachitachita." – ***That I May Know Him, p. 130.***

**b. Kodi ndi motani mmene tingafikile cholinga chimenechi? Ahebri 12:1-4; Agalatiya 5:6 (Mbali yomaliza); Afilipi 3:12-15; 4:13.**

---

---

"Ndimotani mmene tingafikile ungwiro umene umaonetseredwa ndi ambuye komanso Mpulumutsi wathu Yesu Khristu- Mphuzitsi wathu wamkulu?Kodi tingakwanitse zofuna zake ndi kukwanitsa kufikila muyeso wapamwamba ngati otele? Tikhonza kukwanitsa, apo ayi Khristu sakanatilamulira ife kuti tiyenera kutelo. Iyeyo ndiye chilungamo chathu. Muumunthu wake iye anatitsogolera ife ndi kutionetsera ife ungwiro wa khalidwe labwino. Tikuyenera kukhala ndi chikhulupiliro mwa Iye chimene chimachititsa mwa chikondi ndi kuyeretsa moyo. Ungwiro wa khalidwe umakhazikika pa chimene Khristu ali kwa ife. Ngati tingamakhale ndi kudalira kwa nthawi zonse pa kuyenera kwa Mpulumutsi wathu, ndi kumayenda mmapadzi ake, tizakhala ngati iye, oyera ndi osadetsedwa."-***Ibid..***

**c. Ndi motani mu zenizeni zake tingakhalire oyera ndi opanda banga pamaso pa Mulungu? Aroma 5:18- 20; Ahebri 10:14.**

---

---

---

"Khristu samakhulukukira aliyense koma olapadi yekha, komano kwa munthu amene iye wamukhulukira koyambilira komwe amamupangitsa kusweka mtima." – ***Selected messages, bk.1.pp.393,394.***

"Munthu wochimwa akuyenela nthawi zonse kumayang'ana pa kavali; ndipo ndi chikhulupiliro chophweka ngati cha mwana wa ng'ono, akuyenera kumadalira mukuyenera kwa Khristu, ndi kuvomereza chilungamo chake ndi kumakhulupilira mu chifundo chake…

"Ndi chikondi chotani chotele- ndi chikondi chodabwitsa ndi chotsamvetsetseka motani- chimene chinatsogolera khristu kuti atifere ife tikadali chichimwile chomwecho! Ndi kuluza kotani ku moyo umene wanvetsetsa zofunikila za lamulo za mphanvu, komano amalephela kumvetsetsa chisomo cha Khristu chimene chinaikidwa kochuluka kwaife!" – ***Ibid., p. 384***

## 5. KHALIDWE LATHU KUKHALANGATI LA IYE

**Lachisanu, Meyi 22**

**a. Ndi motani mmene tingapangile maitanidwe athu ndi kusankhidwa kwathu kukhala kotsimikizika? 2 Petro 1:4-11; Chibvumbulutso 19:8.**

---

"Mulungu chimene amafuna lero ndi chimene iye amachifuna kwa Adamu, kumvera kwa mbambande, chilungamo chopanda chinyengo, chotsapepuka pamaso pa Mulungu. Mulungu atithandize ife kuti tikakwanirite kwa iye chimene lamulo limafuna kwa ife. Sitingakwanitse kuchita zimenezi popanda chikhulupiliro chimene chimabweletsa chilungamo cha Khristu mmachitachita athu a tsiku ndi tsiku." – ***Selected Messages, bk. 2, p. 381.***

"Ngati Satana akulamulilabe, tizakhala ndi ntchito yogonjetsa uchimo otibwezeletsa mmbuyo; ndipo nthawi zonse pamene tingakhalire ndi miyoyo, sipazakhala malo oti tipume, kapena kufika muyeso umene tinganene kuti, ndatha kufikapo modzadza ndagonjetsa. Kuyeretsedwa ndi zotsatira za kumvera kwa moyo kwa nthawi yaitali." – ***The Acts of the Apostles, pp. 560,561.***

"Tikuyenela kudzindikila kuti kudzera mwa chikhulupiliro mwa iye ndi mwayi wathu kuti tikakhale nawo mwayi otenga nawo mbali mu khalidwe la Umulungu ndi kuti chotelo tikathawe chibvundi chimene chili mdziko kudzera mu chilakolako. Pamenepo timayeletsedwa kuchoka ku machimo onse, ndi zolakwika zonse za khalidwe. Ndipo sitikuyenelanso kubwezeletsanso ngakhale mchitidwe umodzi wa chimo…

"Pamene tikutenga nawo mbali mukhalidwe la umulungu, zizolowedzi zonse zolakwika za chibadwa kapena zotengela kwa ena, zimadulidwa mu khalidwe lathu, ndipo timapangidwa kukhala ndi mphanvu zochitila zabwino. Kumphunzira kwa nthawi zonse zaMphunzitsi wa umulungu, ndi tsiku ndi tsiku kumakhala tikutenga nawo mbali mukhalidwe lake, timakhala tikulumikizana ndi Mulungu mukugonjetsa mayesero a Satana. Mulungu amagwira ntchito, ndipo munthu amagwiranso ntchito, ndi kuti munthu akhale limodzi ndi Khristu monga khristu ali amodzi ndi Mulungu..

"Ndi Mulungu amene amatipatsa phanvu zogonjetsera. Iwo amene amanvera mawu ake ndikumbvera malamulo ake amayenelezedwa kupanga makhalidwe achilungamo." – ***The SDA Bible Commentary(E.G White comments) Vol 7.p, 943.***

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

**Lachisanu ndi chimodzi, Meyi 23**

1. Kodi ndi chifukwa chiyani Afalisi sangathe kupeza moyo osatha pakungotengela pa ndanda wa chibadwa chawo chakumene anabadwira kapena wina aliyense wa ife lero kumadalira makolo kapena D.N.A monga chinthu chopezera chipulumutso?
2. Fotokozani makhalidwe enieni owona aana a Abrahamu?
3. Motengela ndi khalidwe lake, kodi ndi chiyani chimene Yesu amakwanitsa kuchifotokoza?
4. .kodi ndi cholinga chanji chimene chinayikidwa pa maso pa Mkhristu aliyense kuti achifikile?
5. Ndimotani mmene tingapezedwere kukhala angwiro ndi opanda banga pa maso pa Mulungu?

**SABATA, MEYI 31, 2025** **PHUNZIRO 9**

# YESU NDI MUNTHU WAKHUNGU

**VESI LOLOWEZA: "Ndipo Yesu anati, Kudzaweludza ndadza ine ku dziko lino lapansi, kuti iwo osapenya apenye; ndi kuti iwo akupenya akhale osaona" (Yohane9:39).**

**Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, vol.3, pp. 570-575.**

**"Mbiri ya Yobu imaonetsera kuti matsautso amabweretsedwa ndi Satana, ndipo amabvomerezedwa ndi Mulungu ndizolinga za chifundo." -** ***The Desire of Ages, p. 471*****.**

## 1. KUDZINDIKILA KOLAKWIKA — Loyamba, Meyi 25

**a. Kodi ndi funso lanji limene ophunzira anamfusa Yesu pamene iwo anaona munthu amene anabadwa wakhungu? Yohane 9:1, 2.**

---

---

**b. Kodi ndilingaliro lanji lolakwika lokhuzana ndi zotsautsa limene limakhulupiliridwa ndi Ayuda komanso ophunzira, nanga ndimotani mmene Satana amapindulira nawo lingaliroli? Yohane 9:34 (Mbali yoyamba).**

---

---

---

"Chimakhulupililidwa ponseponse pakati pa Ayuda kuti chimo chilango chake chimaperekedwa mmoyo womweuno. Bvuto lililonse limatengedwa kukhala chilango cha cholakwa chinachake, mwina kulakwa kwa odwalayo mwiniwake kapena kwa makolo ake. Ndizoona kuti kudwala konse ndizotsatila zakuphwanya kwa lamulo la Mulungu, Koma choona ichi chakhala chikupotozedwa. Satana, oyambitsa wa uchimo ndi zotsatila zake zonse, wakhala akutsogolera anthu kuti aziyang'ana pa matenda ndi imfa ngati zochokera kwa Mulungu zoperekedwa chifukwa cha chimo. Chotelo munthu amene matsautso akuulu kapena tsoka linalake lalikulu lagwera pa iye amakhalanso ndi cholemetsa choonjezera chomatengedwa ngati wochimwa wamkulu.

"Chotelo njira inakonzedwa yoti a Yuda akane Yesu. Iye amene `ananyamula zowawa zathu, ndikusenza zisoni zathu' ayuda amayang'ana pa iye monyoza monga `okanthidwa ndi Mulungu ndi ovutidwa; Ndipo iwo anabitsa nkhope zawo kwa iye." – ***The Desire of Ages, p. 471.***

**a. Kodi ndi lankho lanji la Yesu limene linapereka kuunika zokhuzana ndi kubvutika ndi chimo? Yohane 9:3-5.**

“Chikhulupiriro cha a Yuda chokhuzana ndi kugwirizana kwa chimo ndi matsautso limatengedwanso ndi ophunzira a Yesu. Pamene Yesu amakonza cholakwitsa chawo, iye sanafotokoze choyambitsa chamatsautso a Munthu, koma anawauza iwo chimene chingakhale chotsatira. Chifukwa cha ichi ntchito za Mulungu zionetsedwa. ‘Pakukhala ine padziko lapansi,’ Iye anati, ‘ine ndine kuunika kwa dziko lapansi.’ ”- ***The Desire of Ages, p. 471.***

**b. Kodi ndi chiyani chimene Yesu anachita patangodutsa nthawi pang’ono, nanga ndimotani mmene munthu wakhungu anagwirizilana ndi iye? Yohane 9:6, 7.**

“Atatha kudzoza maso a munthu wakhungu, iye anamutumiza iye kuti akasambe muthamanda la Siloamu, ndipo maso amuthuyo anachilisidwa. Mukutele Yesu anayankha funso la ophunzira kudzera muchochitika, monga mmene iye nthawi zambiri amachitira mukuyankha mafunso operekedwa kwa iye mwamkwiyo. Ophunzira sanaitanidwe kuti azikakambirana funso lokhuzana ndi kuti ndi ndani amene anachimwa kapena sanachimwe, koma kuzazindikira mphanvu ndi chisomo cha Mulungu mukupereka kupenya kwa akhungu. Chinali choziwikilatu kuti munalibe mphanvu zamachilitso muthope, kapena muthamanda limene munthu wakhungu anatumizidwa kuti akasambe koma kuti mphanvu zinali mwa Khristu. “- ***Ibid.***

**c. Fotokozani mmene azinzake ndi omuzungulira anachitira –ndipo fotokozani kulankhulana kumene kunakhalapo pakati pa iye ndi anzake. Yohane 9:8-12.**

“Anzake anyamata wachichepereyu-ndiiwo amene amamuziwa iye ali wakhungu mmbuyomu, anati, `Kodi siuyu uja wokhala ndikupemphapempha?.’ Iwo anayang’ana pa iye ndikukayika ;pakuti pamene maso ake anasegulidwa, nkhope yake inasinthika ndikuwalitsidwa, ndipo amaoneka ngati munthu wina. Pakati pa wina ndi mzake funso linafunsidwa. Ena amati, `ndiiyeyo’ Ena amati, ‘iye akufanana ndi iye.’ Koma iye amene analandira dalitso lalikulu kwambiri anathetsa funsoli kudzera mukuyankha kuti, `Ndiine amene.’” – ***Ibid., pp. 471, 472.***

## 3. FUNSO LIKULA

**Lachitatu, Meyi 27**

**a. Ndi kwa ndani kumene atsogoleri aYuda anatengela munthu amene anabadwa osaona – nanga chifukwa chiyani? Ndipatsiku lanji pamene iye anachilitsidwa? Yohane 9:13, 14.**

**b. Fotokozani mmene anachitila Afarisi pa nkhaniyi? Yohane 9:15, 16.**

"Afarisi anayembekezera kuti amuonetsere Yesu kukhala ochimwa, ndipo chotelo osati Mesiya. Iwo sanaziwe kuti ndiiyeyo amene anapanga Sabata ndikudziwa zofunikira zonse, pamene anachidza munthu wakhungu. Iwo amaoneka achangu modabwitsa za kutsunga kwa Sabata, komabe amakonza zakupha patsiku lomwelo." – ***The Desire of Ages, p. 472.***

**c. Kodi ndindani amene Afarisi anawaitana kuzachita umboni zokhuzana ndi munthu amene anachilitsidwa? Yohane 9:18, 19.**

"(Afarisi) anaitanitsa makolo ake, ndikuwafunsa iwo kuti,` kodi uyu ndi mwana wanu, amene inu mumati anabadwa osaona?.'

"Munthuyu anali pamenepa mwini wake, kumafotokoza kuti iye anali osaona, ndikuti kuona kwake kunabwezeretsedwa; koma Afarisi kunali kwabwino kwa iwo kukana umboni wapoyera koposa kubvomereza kuti iwo amalakwitsa. Ndi kwamphamvu kwambiri kuweluziratu, chilungamo cha chifarisi ndi chosokoneza kwambiri." – ***Ibid.***

**d. Kodi ndimotani mmene ife timachenjezedwera zokhuzana ndi kuipa kwakukhala ndi lingaliro lokhazikitsiratu? Miyambo 18:13.**

"Pali ambiri amene amapanga mawu a iwo okha kudzera pa zimene amva, kupanga lingaliro kuoneka losinthikiratu ndi limene oyankhula amayetsetsa kuti afotokoze. Ena, pakunva kudzera mumzeru zawo zoweluziratu, kapena zimene anakhazikitsiratu, amaimvetsetsa nkhaniyo monga mmene afunira kuti ikhalire monga mmene ingakwanilitsidwire bwino kuzolinga zawo." – ***Testimonies to the Church, vol. 5, p. 695.***

## 4. KUKUMANA NDI CHIOPSEZO

**Lachinayi , Meyi 28**

a. **Kodi ndimotani mmene Afarisi anayetserera kuopseza makolo amunthu amene anabadwa wakhunguNanga ndimotani mmene iwo anayankhira? Yohane 9:20, 21. Chifukwa chiyani iwo anapeleka yankho lolambalala? Yohane 9:22, 23.**

---

---

"Afarisi anatsala ndi chiyembekezo chimodzi chokha, ndipo chinali choti aopseze makolo amunthuyo, ndimaonekedwe ooneka achidwi choona iwo anafunsa `ndipo apenya bwanji tsopano'? Makolowa pochita mantha kuti aziika okha pachiopsezo; popedza chinalengezetsedwa kuti wina aliyense amene angabvomeleze Yesu kuti ndi Khristu akuyenera `kuletsedwa mu Sunagoge' kuti , akuyenera kuchotsedwa kuchoka musunagoge.munthawi imeneyi palibe mwana amene angadulidwe kapena wakufa kulilidwa kubanja lolakwali. Chigamulochi chimatengedwa kukhala tsoka lalikulu; ndipo ngati chingalephere kubweletsa kulapa, chilango chokulirapo chimatsatila. Ntchito yaikulu imene inachitidwa kwa mwana wawo inabweretsa kukhuzika kwakukulu kwa makolowa, komabe iwo anayankha kuti, 'tidziwa kuti uyu ndi mwana wathu, ndikuti anabadwa osaona; koma sitiziwa umo apenya tsopano; kapena sitimziwa amene anamutsegulira maso ake;mufunse iye.' Mukutelo iwo anatsamutsa udindo wonse kuchokera pa iwo okha kupita kwa mwana wawo; pakuti iwo sanayelekedze kuti abvomereze kuti achitire umboni Khristu.***"- The Desire of Ages, 471, 473.***

b. **Pamene tadzungulilidwa ndi chiopsezo, kodi ndi chiyani chomwe tikuyenera kuchisunga mmalingaliro? Masalmo 118:6.**

---

---

"Imani nji ndipo musayelekeze kuchita chinachilichonse choipa nkwabwino kuchulidwa opusa. Musalore kuti kunyoza, kuopseza, kapena mawu opeputsa, kuti akupangitseni inu kuvuladza chikumbumtima chanu ingakhale pang'ono." – ***Fundumentals of Christian Education, p. 93.***

"Khalidwe loona lachikhristu likuyenera kuonetseredwa kudzera mukukhala oima njii mucholinga, kutsimikizika kosasinthika, limene silingaumbidwe kapena kugonjesedwa ndi dziko lapansi kapena jehena. Iye amene Sali wakhungu kuzokopa za ulemu wa dziko lapansi, osunthika ndi ziopsezo, komanso ogwedezeka ndi zokopa azakhala, mosayembekezera kwa iye mwini, ogonjesedwa ndi misampha ya satana." ***-Testimonies for the Church, vol. 4, pp. 543, 544.***

"Ife tizalandira kutsutsa kwakukulu kwambiri kuchokera kwa ma Adventist amene amatsutsa lamulo la Mulungu. Koma monga omanga linga la yelusalemu, Ife sitikuyenera kupatutsidwa kapena kuchingilidwa kuchoka kuntchito yathu kudzera muzoneneza, kudzera mwa amithenga ofuna kukambirana kapena kulimbana, kapena kudzera mu mawu aziopsezo, zolembera za bodza, ingakhale zida zilizonse zimene satana angazigwiritse ntchito."***-Ibid., vol. 3, p. 574.***

## 5. MBIRI IBWELEZEDWA — Lachisanu, Meyi 29

**a. Fotokozani chochitika chimene akumane nacho anthu a Mulungu osunga malamulo - Nanga kodi ndi motani mmene ife tikuyenera kuyankhira kuchochitikachi? Chibvumbulutso12:17; Machitidwe 4:18-20.**

---

---

"Pamene mkangano ukufalikira kupita mmadera atsopano ndipamenenso malingaliro aanthu aitanitsidwe kulamulo lamulungu lopondelezedwa, Satana walutsa. Mphanvu zimene zikuyendera limodzi ndi uthenga zizangowakwiyitsa kwambiri basi iwo amene akuutsutsa uthengawu. M'busa azaika mphanvu zonse zopotsa za umunthu kuti achingire kuunika kuopa kuti kungathe kuwalira pa gulu lake lankhosa. Mwanjira iliyonse imene ili pamaso pawo iwo azayesesa kupondereza kukambirana kwina kuli konse kwa mafunso ofunikira amenewa. Mpingo uzapempha thandizo ku zanja lamphanvu laboma, ndipo ntchito imeneyi, ansembe ndi otsutsa azagwirizana pamodzi. Pamene mgwirizano wolimbikitsa kukhazikitsidwa kwa Sunday ungazakhale wamphanvu ndi wokhazikika, lamulo lizaikidwa lolimbana ndi osunga malamulo. Iwo azaopsezedwa ndi zindaputsa komanso kusekeledwa mundende, ndipo ena azapatsidwa maudindo olemekezeka, ndimphoto ndi maulemu osiyanasiyana, monga zokopa kuti iwo asiye chikhulupiriro chawo, koma yankho lawo lokhazikika ndiloti…` Tionetseni ife kuchokera mmalembo a Mulungu cholakwa chathu'- Pempho lomwelo limene analipempha Martin Luther atakumana ndi zochitika zofanana. Iwo amene azaitanitsidwe kukaima mmabwalo amilandu azachitila umboni mwamphanvu choonadi, ndipo ena amene azawanve iwo azatsogoleredwa kutenga mbali yawo kuti azisunga malamulo onse a Mulungu. Motero kuunika kuzabweretsedwa pamaso pazikwizikwi amene mwanjira ina sakanaziwa kenakalikonse kokhuza choonadi chimenechi." – *The Desire of Ages, p. 607.*

**b. Pokumana ndi kutsutsidwa, kodi ndi chiyani chimene ife nthawi zonse tikuyenera kuchiika mmalingaliro? Yohane 9:39; Machitidwe 4:33; Masalmo 10:28.**

---

"(Ophunzira) sanathe kukakamizidwa kapena kuopsezedwa ndi ziopsezo" ***– The Acts of Apostles, p. 48.***

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu ndi chimodzi, Meyi 30

1. Kodi ndi motani mmene atsogoleri achiyuda amaweluzira odwala ndi otsautsika?
2. Kodi ndi chiyani chimene moonadi chinachilitsa munthu wakhungu?
3. Kodi ndi chifukwa chiyani azinzake amunthu wakhungu anasokonezeka?
4. Kodi ndi chochitika chanji chimene mnyamata wachichepere anakumana nacho atatha kuchilitsidwa?
5. Kodi ndi motani mmene ine ndingapewere kugwera mumsampha omwewo umene anagwera makolo ake?




**ZOPELEKA ZA SABATA LOYAMBA**

**SABATA, JUNI 7, 2025**



## ZAMACHALICHI AWIRI MU TAMIL NADU, INDIA

Maumboni azokumbakumba amaonetsera kuti ingakhale kuyambira muzaka za mma 2600 B.C,Chitukuko cha mmizinda cha gulu la Indus chinazakhala mudela limene lelo limachedwa kuti India. Chipembezo chachikulu chachikoka kumeneku chakhala chili chi Hindu(79.8%), Chosatila ndi chisilamu (14.2%),Chikhristu (2.3%),Sikchism(1.7%) ,ndi zina. Ngakhale pali mbili zina zakulumikizana ndi a SDA Reform Movement zilipo kuyambila mu 1920 ndi 1950, ndimu 1987 mmene kumpoto kwa India kunakhala ndi oimilirako oyambilira obvomelezeka pansonkhanu wakulu wa General Conference wa SDARM.

Mzinda wakummwera kwa India- Tamil Nadu- umatengedwa kukhala nkhokwe yamphanvu ya zokonzakonza komanso ulimi. Ntchito ya Ambuye inakhazikisidwa kumeneku kwa zaka zambiri, Koma kutumikira chiwelengelo chachikulu cha anthu choposa 72 milion mzinda umenewu, pakusoweka kukhala ndi mautumiki amphanvu.

Molingana ndi chiwelengelo cha anthu chaku india chamu 2001, mudzi wa Pattiveeranpatti uli ndi chiwelengelo chokwana 7,744. Chiwelengelo chaanthu ophunzira ndi 83%, chachikulu kwambiri kuposa chaanthu adziko lonse la India. Chinthu chachikulu chimene chimabweletsa ndalama mmanyumba ambiri ndi ulimi wa khofii, otsatilapo wanthochi, wamaolenji, wa cardamom, wasabola, ndi ma spice ena. Mudzi waukulu ndi pallapatti ndi okhala ndi chiwelengelo cha anthu okwana 13,701.

Kuyambira mu 1998, ntchito yosatopetsa yaolalikira uthenga wochokera ku Periyaklam yathandiza kukuza chiwelengelo cha ziwalo zampingo makamaka mmadela awiri amenewa. Zobechela zosiyanasiyana zapangitsa kukhala chovuta kwambiri kupiliza kukhala nyumba zobweleka, Chotelo panthawi ino, abale ammudzi mwa Pattiveeranpatti ndi Pallapatti akufunika malo awoawo opembezera.

Mzimu wachinenelo mwapadela umanena za India monga malo amene "Zikwizikwi za anthu sizinamvepo kwambiri za Mulungu ngakhale za chikondi chake chomwe chinabvumbulutsidwa mwa Khristu. Ndiufulu wawu kulandira chiziwitso chimenechi. Iwo ali ndichoyeneleza chofanana ndi chathu muchifundo cha mpulumutsi." –
***Education p 263***

Chotelo mwaulemu tikupempha abale ndi alongo athu kudziko lonse lapansi kuti mupeleke thandizo lanu lolowa mmanja kuti timange nyumba zakuunika za ambuye kuti ziziwala midzi imeneyi. "Ndi ntcchito yakuimilira malamulo aMulungu ndikumanga malo abwinja amene anapangidwa mulamulo lamulungu, tikuyenera ife kusakaniza chifundo kwa mtundu waanthu obvutika. Ife tikuyenera kuonetsera chikondi chachikulu kwa Mulungu; Tikuyenera kukweza chikumbutso chathu."-***Welfare Ministry,p 32***. Tikukuthokozani inu, ndipo Ambuye athe kudalitsa mphatso ndi opereka!

Abale ndi alongo anu ochokela ku Pattiveeranpatti ndi Pallapatti.

SABATA, JUNI 7, 2025 **PHUNZIRO 10**

# KUKUMANA NDI KHUNGU LAUZIMU

**VESI LOLOWEZA: "Chifukwa chake ndinena kwa inu, Machimo onse, ndi zonena zonse zamwano, zidzakhululukidwa kwa anthu; koma chamwano chapamzimu woyera sichizakhululukidwa. Ndipo amene ali yense anganenere mwana wa munthu zoipa, adzakhululukidwa; koma amene aliyense anganenere Mzimu woyera zoipa sadzakhululukidwa nthawi ino kapena irinkudzayo." (Mateyu 12:31, 32).**

**Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, vol. 2, pp. 489-497.**

**"Si Mulungu amene amapangitsa khungu maso a anthu kapena kuumitsa mitima yawo. Iye amawatumizira iwo kuunika kuti akonze zolakwa zawo, ndikuwatsogolera iwo kunjira yotetezeka; ndikudzera mukukana kuunika kumeneku kuti maso amachititsidwa khungu ndi mitima imaumitsidwa."-** ***The Desire of Ages, p. 322.***

## 1. KUFUNSANA KOYAMBIRANSO — Loyamba, Juni 1

**a. Atamuitanisa kwanthawi yachiwiri mnyamata wachichepele amene kuona kwake kunabwezeretsedwa ndi Khristu, kodi ndi chiyani chimene Afarisi anayesera kumukakamiza iye kuti achite? Yohane 9:24.**

---

---

"Afarisi anaona kuti iwo akufalitsa ntchito imene yachitidwa ndi Yesu. Iwo sangathe kukana chozizwacho. Munthu wakhungu anazazidwa ndi chimwemwe ndi chiyamiko iye anaona zinthu zodabwitsa zamchilengedwe, ndipo anazazidwa ndichisangalalo pakuona kukongola kwa dziko ndi thambo. Iye mwaufulu amafotokoza zomwe zinachitika kwa iye, ndipo kawirinso anayetsetsa kuti amukhazike iye chete, Poonena kuti `lemekedza Mulungu tidziwa kuti munthuyu ali wochimwa.' Kutanthauza kuti, usamanenenso izi kawiri kuti munthu uyu anakupatsa iwe kuona; ndi Mulungu amene anachichita ichi." – ***The Desire of Ages, p. 473.***

**b. Kodi ndi chozikanira chanji chokhazikika chimene mnyamata wachichepere anachiyankhula? Yohane 9:25.**

---

---

---

**a. Kodi ndi chiyani chimene Afarisi kawirinso anafunsa mnyamata wachichepere amene kuona kwake kunabwezeretsedwa-nanga ndi cholinga chanji chimene iwo anali nacho? Yohane 9:26.**

---

---

"(Afarisi) anafunsanso kawiri, `anakuchitira iwe chiyani? Anakusegulira iwe maso bwanji?' Ndimawu ambiri iwo anayesetsa kuti amutsokonedze iye, kotelo kuti iye azizilingalira yekha kuti wasokonezeka mmutu. Satana ndi Angelo ake oipa anali kumbali ya Afarisi, ndipo polumikizitsa mphanvu zawo ndi ukachenjele wawo ndimalingaliro amunthu ndi cholinga choti apotodze ndikufufuta chikoka cha khristu. Iwo anasokoneza kukhuzika kumene kumakula mmitima ya Ambiri." – ***The Desire of Ages, p. 473.***

**b. Kodi ndimotani mmene mnyamata wachichepereyu anawayankhira iwo- nanga kodi ndindani amene anaima kumbali yake kuti azimulimbikitsa iye? Yohane 9:27.**

---

---

"Angelo a Mulungu analinso pamalopa kuti azimulimbikitsa munthu amene kuona kwake kunabwezeretsedwa. "Afarisi sanazindikile kuti iwo akuchita ndi wina woposa munthu wosaphunzira amene anabadwa wakhungu; Iwo samamuziwa iye amene anali naye mukulimbana. Kuunika kwa umulungu kunawalira mumtima wamunthu wakhungu. Pamene achinyengo amenewa amayetsera kumupanga iye kuti asakhulupirire, Mulungu anamuthandiza iye kuti aonetsere, kudzera mumayankho ake amphanvu komanso achindunji, kuti iye sangathe kupotozedwa." – ***Ibid ., pp. 473,474.***

**c. Kodi ndi motani mmene ife tikusimikiziridwa za thandizo longa lomweli lero? Luka 12:11, 12.**

---

---

"Tsopano, ndimabaibulo anu mukufunika kupita pamaso pa Mulungu, atseguleni iwo pamaso pa Mulungu ndikupemphera kwa Mulungu. Mukufunika inu kuti kuzindikila kwanu kutsistimutsidwe; mukufunika inu kudziwa kuti mukuziwa mfundo zenizeni za choonadi, ndipo kenako pamene mwakumana ndi okutsutsani inu simuzakumana nawo mumphanvu za inu nokha angelo a Mulungu azaima pambali panu kuti akuthandizeni inu kukuyankha funso lililonse limene lizafunsidwe kwa inu. Komanso pa nthawi yomweyomweyo Satana azaima pambali pa okutsutsani inu kuti awalimbikitse iwo kuti alankhule zinthu zovuta kwa inu kuzipilira, ndicholinga choti akukwiitseni inu kuti mulankhule mosayenera; koma lolani inu kuti kulankhula kwanu kukhale koti Satana sangathe kutengelapo mwayi pa mawu anu." – ***The Review and Herald, May 3, 1887.***

## 3. KULIMBA MTIMA PAMASO PA KHUNGU LADALA — Lachinayi, Juni 3

**a. Atalephera kunamidza mnyamata wachichepele amene anachiritsidwa, kodi ndi motani mmene Afarisi anamupeputsira iye-nanga ndimotani mmene umbuli wotele wakhala ukuonetseredwa mumbiri? Yohane 9:28, 29; 1 Akolinto 1:18, 19, 26-28.**

“Ku mpingo wake kumibadwo ulionse Mulungu amakhala ndi choonadi chapadera ndi ntchito yapadera. Choonadi chimene chimabitsika kwa amzeru ndi ozindikira adziko lapansi chimabvumbulutsidwa kwa ozichepetsa ndi okhala ngati ana. Chimaitanitsa kudzipereka nsembe wekha. Chili ndi nkhondo zoti zimenyedwe ndi zipambano zoti zipambanidwe. Poonekera chili ndi ochiimirira ochepa mwa anthu aakulu akulu adziko lapansi ndimupingo oyendera limodzi ndi dziko lapansi, iwo amatsutsidwa ndi kupeputsidwa …

“Atsogoleri akulu azipembezo amaganiza mum’badwo uno zoyamikira ndi kumanga zikumbutso za iwo amene anadzala mbewu ya choonadi mmibadwo yapita. Kodi ambiri samatembenuka kuchokera kuntchito imeneyi kuti azipondereza pansi mphukira zophuka kuchokera kumbewu yomweyi lero? Kufuula kwa kalekale kumabwerezedwa, `Tiziwa ife kuti Mulungu analankhul ndi Mose; koma s kumene za munthu uyu (Khristu mwa mtumiki amene iye wamutuma) sitiziwa kumene achokera.’ Yohane 9:29. Monga mmibadwo yoyambilira, choonadi chapadera chanthawi ino chimapedzeka, osati ndi akuluakulu achipembezo, koma ndi amayi ndi abambo amene sali ophunzira kwambiri ndi amzeru kwambiri kuti akhulupilire mawu a Mulungu.”- ***Christ’s Objects Lesson, pp. 78, 79.***

**b. Kodi ndichisanzo chanji chimene ife tingachiphunzire kuchokera kuumboni owona mtima wamnyamata wachichepere, pamodzi ndi okhulupirira oona ena akhristu? Yohane 9:30-33; Machitidwe 4:19, 20.**

“Mwaulemu wonse, muuzimu wachisomo, ndimuchikondi cha Mulungu tikuyenera kuwalodzera anthu kuchoona choti Ambuye Mulungu ndi mulengi wakumwamba ndi dziko lapansi ndikuti tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Ambuye.

“Mudzina la Ambuye tikuyenera ife kupita chitsogolo, kutambasula mbendera yake, kuimilira mawu ake. Pamene olamulira atilamula ife kuti tisachite ntchito imeneyi, pamene iwo atiletsa ife kuti tilalikire malamulo a Mulungu ndichikhulupiliro cha Yesu, pamenepo chidzakhala chofunikira kwa ife kuti tilankhule monga anachitira ophunzira…`weludzani ngati mkwabwino pamaso pa Mulungu kumvera inu kapena Mulungu. Pakuti sitingathe ife kuleka kulankhula zimene tinaziona ndi kuzimva.’ Machitidwe 4:19, 20.” – ***Testimonies for the Church, Vol. 6, p. 395.***

**a. Popedza Afarisi okwiya samafuna kubvomereza umboni, kodi ndi chiyani chimene iwo anachita ndi mnyamata wachichepere amene amachitira umboni za kuchilitsidwa kwake? Yohane 9:34**.

---

---

"Munthuyu anakumana ndi omufunsa mafunso pamalo awo. Mfundo zimene iye amayankhula zinali zosayankhika. Afalisi anadabwitsika, ndipo anakhala duu- opanda mawu pamaso pa mawu ake osimikizika komanso achindunji. Kwamphindi zochepa panali bata. Kenako Ansembe ndi Arabi amkwiyo anakonza mikanjo yawo moisonkhanisa ngati mwina akuopa kudetsedwa kochokera kukukhuzana ndi iye; anasasa fumbi lakumapadzi awo, ndikuyankhula zonyoza zambirimbiri kwa iye `Wabadwa iwe konse mzoipa, ndipo iwe utiphuzitse ife kodi?'Ndipo iwo anamchosa mkachisi." – ***The Desire of Ages, p. 474.***

**b. Mosiyana, kodi ndimotani mmene Yesu anachitira ndi mnyamata wachichepele? Yohane 9:35-38.**

---

"Munthuyu anazigwetsa yekha pamapadzi ampulumutsi kumupembeza. Osati kuona kwake kwachibadwa kokha kunabwezeretsedwa, koma maso akuzindikira kwake anasegulidwa Khristu anaonetsedwa kumoyo wake, ndipo iye anamulandira iye ngati wotumidwa ndi Mulungu." – ***The Desire of Ages, p. 475***.

**c. Fotokozani kusiyana kwakukulu pakati pa kuchosa maina anthu opanduka ouma mtima kusiyanitsa ndi akhungu ouma mtima okana Khristu kuchotsa kwawo miyoyo imene imakonda kumvera Mulungu? 1mafumu 9:6-9; Mateyu 12: 31, 32; Masalmo 11:3.**

---

---

"(Wycliffe anaona,) palibe munthu amene moonadi angachotsedwe dzina mumpingo pokhapokha iye atayamba kaye kuzibweletsera pa iye yekha kutsutsa kwa Mulungu." ***– Great Controversy, p. 84.***

"Kutsusidwa ndi gawo la onse amene Mulungu amawagwiritsa ntchito yolalikira choonadi makamaka chokhuzana ndi nthawi yawo. Kunali choonadi chalero mmasiku a Luther- choonadi chofunikira mwapadera munthawi imeneyo; pali choonadi chalero kumpingo lero… iwo amene akulalikira choonadi chanthawi ino sakuyenera kumayembekezera kulandilidwa ndikukondera kwakukulu kupotsera okonzanso oyambilira. Kulimbana kwakukulu pakati pa choonadi ndi boza, pakati pa Khristu ndi Satana, kuzikulirakulira mwamphanvu mpakana kumapeto a mbiri adziko lino lapansi."- ***Ibid., pp. 143,144.***

## 5. KUDALITSIKA KUSIYANITSA NDI KUWELUDZIDWA NDI KUUNIKA — Lachisanu, Juni 5

**a. Kodi ndi chiyani chimene Yesu ananena zokhuzana ndi zotsatira za ntchito yake? Yohane 9:39.**

---

"Gulu la Afarisi linasonkhana pafupi, ndipo kuonekera kwawo kunabweletsa kumalingaliro a Yesu kusiyana koonekera kwa nthawi zonse kuzotsatira za mawu ndi ntchito yake… Khristu anabwera kuzatsegula maso aakhungu, kuzapereka kuunika kwa iwo amene ali mumdima, iye anazilengezetsa yekha kuti ndikuunika kwa dziko lapansi, ndipo chodzizwa chimene changochitidwa kumene chinali umboni waukulu wa utumiki wake. Anthu amene anamuona mpulumutsi pakudza kwake koyamba anakondeledwa ndikuonekera kodzadza kwakupedzeka kwa Umulungu kupotsera kumene dziko linakhala nako mmbuyo mmosemu. Chiziwitso cha Mulungu chinabvumbulutsidwa mwabwino kwambiri. Koma mukubvumbulutsa kotele komweku, chiweludzo chinapita pa anthu. Khalidwe lawo linayesedwa, chimalidzilo chawo chinatsimikizidwa." – ***The Desire of Ages, p. 475.***

**b. Kodi ndimotani mmene Afarisi anayankhira kumawu a Yesu? Yohane 9:40. Pamene iye amayankhula kwa iwo, kodi ndimotani mmene Yesu anaonetsera kulakwa kwawo za khungu la iwo eni? Yohane 9:41.**

---

"Kuoneseledwa kwa mphanvu za Umulungu kumene kunapeleka kwa Munthu wakhungu kuona kwachibadwa komanso kwa uzimu kunawasiya Afarisi mumdima waukulube….Ngati Mulungu sakanachipanga icho kukhala chotheka kwa inu kuti muone choonadi, kusazindikira kwanu sikukanakhala nawo chimo. `koma sopano munena, tipenya.'inu mumazikhulupirira mwanokha kukhala oona, ndikumakana njira yokhayo imene inu mungathe kulandira kuona. Kwa onse amene adzindikira chosowa chawo, Khristu amabwera ndi thandizo lenileni. koma Afarisi samavomeleza chosowa chilichonse; iwo

anakana kuti abwere kwa Khristu, ndipo chotelo iwo anasiidwa mukhungu – limene ndi iwo okha anali olakwa. Yesu anati, `Chimo lanu likhala."- Ibid.

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu ndi chimodzi, Juni 6

1. Ndi za chiyani zimene Afarisi anayesesa kuti amupange munthu amene anali wakhungu kale kuti akhulupilire?
2. Kodi ndindani amene amawagwiritsa ntchito Afarisi osakhulupilira?
3. Kodi ndi ndani amene anathandiza mnyamata wachichepele kupeleka mayankho achindunji komanso okhuza?
4. Kodi ndichiyani chimene chinachitika pamene iye molimba mtima, mwapoyera anachitila umboni Khristu?
5. Fotokozani mtundu woopsetsetsa wakhungu, nanga chifukwa chiyani?

SABATA, JUNI 14, 2025

PHUNZIRO 11

# YESU, MBUSA WABWINO

**Vesi Loloweza: "Ine ndine m'busa wabwino; m'busa wabwino ataya moyo wake chifukwa chankhosa" (Yohane 10:11).**

**Zowelenga zoonjezera: The Desire of Ages, pp. 476-484.**

**"Khristu ndi khomo komanso ndi mbusa. Iye amalowa mkati kudzera mwa Iye yekha. Ndikudzera munsembe yozipereka yekha kuti Iye anakhala mbusa wankhosa."-The Desire of Ages, p. 478.**

## 1. OKUBA NDI MBUSA

**Loyamba, Juni 8**

**a. Kodi ndi motani mmene Yesu anasiyanisira pakati pa okuba ndi mbusa, Nanga ndi phunziro lanji lauzimu limene Iye amalionetsera? Yohane 10:1, 2.**

"Khristu anagwiritsa ntchito mauneneri awa [onena zautumiki waubutsa wamesiya, monga mmene analembera mu Yesaya 40:9-11; Masalimo 23:1, Ezekieli 34:23,16,25,28] kwa iye yekha, ndipo iye anaonetsera kutsiyana kwa khalidwe lake laiye mwini ndila atsogoleri a Israeli. Afarisi anali atangothamangitsa kumene munthu mmodzi kuchokera mukhola, chifukwa choti iye anasimikiza mtima kuchitira umboni zamphanvu za Khristu. Iwo anadula moyo umene mbusa oona amaukokera kwa iye yekha muchimenechi iwo azionetsera okha kukhala osadziwa ntchito imene inaperekedwa kwa iwo, ndikukhala osayenera kuchidaliro chawo monga abusa agulu lankhosa. Yesu tsopano akuika pamaso pawo kusiyana pakati pa iwo ndi mbusa wabwino, ndipo iye akuzionesera iye mwini monga woweta weniweni wa gulu lankhosa." – ***The Desire of Ages, p. 477.***

"Khristu amatikonda ife chifukwa ndiife osowa thandizo ndi odalira." ***– Selmons and Talks, Vol. 1, p. 248.***

**b. Kodi ndiubale wanji umene ulipo pakati pa nkhosa ndi mbusa wawo? Yohane 10:3, 4. Kodi ndi chiyani chimene nkhosa zimachita pamaso pa mlendo? Yohane 10:5.**

**a. Kodi ndi motani mmene Yesu anabvumbulutsira kusiyana kwa iye mwini ndi Afarisi? Yohane 10:7-10.**

---

"Khristu ndi khomo lolowela mukhola la Mulungu. Kupyolera pakhomo limeneli ana ake onse, kuyambira munthawi yoyambilira, akhala akupedza polowela. Mwa Yesu, monga zinaonetseredwa muzoimilira, monga zinaphimbilidwa muzizindikiro, monga zinaonetseredwa mumabvumbulutso aaneneri, monga zinaikidwa poyera mumaphunziriro amene anaperekedwa kwa ophunzira ake, ndi muzozizwitsa zimene zinachitidwa kwa ana aanthu, iwo anaona `mwanawankhosa wa Mulungu, amene achosa chimo lake ladziko lapansi' (Yohane1:29), ndipo kudzera mwa iye iwo abweletsedwa mkati mwa khola lachisomo chake. Ambiri akhala akubwera kuzaphuzitsa ziphuzitso zina zachikhulupiriro cha dziko lapansi; miyambo ndimadongosolo akhala akukonzedwa amene kudzera mwa iwo anthu amayembekezera kulandira kulungamitsidwa ndi mtendere ndi Mulungu, ndipo mukutero kupedza khomo lolowela kukhola lake. Koma khomo lokha ndi Khristu, ndipo onse amene aika zinazake kuti zitenge malo a khristu, onse amene akhala akuyesera kulowa mukhola kudzera munjira ina, ndi okuba ndi ambanda.

"Afarisi sanalowe kudzera pakhomo. Iwo akwela kulowa mukhola kudzera munjira ina osati ya Khristu, ndipo iwo samakwanilisa ntchito ya mbusa oona. Ansembe ndi atsogoleri, Alembi ndi Afarisi, anaononga msipu wamoyo, ndikudetsa akatsupe amadzi amoyo. Mokhulupirika mawu aumboni akufotokoza za abusa aboza amenewa kuti ..`Zofooka simunazilimbitsa; yodwala simunaichilitsa, yothyoka simunailukira chika, yopitikisidwa simunaibweza…koma munazilamulira mwamphanvu ndi moopsa.' Ezekieli 34:4." – ***The Desire of Ages, pp. 477, 478.***

**b. Kodi ndimotani mmene mbusa woona amasiyanirana ndi olembedwa ntchito? Yohane 10:11-13.**

---

---

"Akufunika, osati anthu chabe oti angathe kulalikira, koma iwo amene ali ndi chiziwitso chamachitachita achinsinsi cha umulungu, amene angathe kuchitapo kanthu kuzosowa za pompopompo za anthu-iwo amene akumvetsetsa kufunikira kwa udindo wawo monga akapolo aKhristu, ndipo amene mokondwera azasenze mtanda umene iye anawaphuzitsa iwo kuti ausenze.

"Ndichofunikira kwambiri kuti mbusa azilumikizana kwambiri ndi anthu ake, ndipo mukutelo azikhala ozolowelana ndi magawo osiyanasiyana akhalidwe lachibadwa laumunthu. Iye azitha kumasinkhasinkha zimene zikuonekela pa mitima yaanthu, Kotelo kuti iye athe kukonza maphunziro ake kukugwirizana ndi mzeru za omumvetsera ake. Iye mukutelo azaphunzira chikondi chachikulu chimene alinacho iwo okha amene amaphunzira mwachidwi khalidwe lachibadwa ndi zosowa zaanthu." – ***Gospel Workers, p. 191.***

## 3. MBUSA WENIWENI WABWINO

**Lachitatu , Juni 10**

**a. Kodi ndi makhalidwe ena anji ambusa wabwino amene Yesu anawaonetsera? Yohane 10:14, 15.**

---

---

"Monga mmene mbusa wakudziko lapansi amaziwila nkhosa zake, chotelonso ndimmene mbusa wa umulungu amadziwila gulu lake la nkhosa limene lamwazikana padziko lonse lapansi.`Ndipo inu nkhosa zapabusa panga, ndinu anthu, ndiine Mulungu wanu, ati Ambuye Yehova.' Yesu akuti, Ndakuchula dzina lako, iwe uli wanga.'ndakulembera iwe pazikhato za manja anga.' Ezekieli 34:31; Yesaya 43:1; 49:16.

"Yesu amatiziwa ife payekhapayekha, ndipo amakhuzika ndi zofooka zathu. Amatiziwa ife tonse ndi dzina lathu. Iye amadziwa nyumba imene ife timakhala, dzina la wina aliyense amene ali mnyumbamo. Iye nthawi zina anakhala akupeleka mapu kwa akapolo ake kuti apite kunjira yakutiyakuti mumzinda wakutiwakuti, kuti akapeze imodzi mwa nkhosa zake.

"Moyo winaulionse umaziwika modzaza kwa Khritsu monga ngati ndiokhawo umene mpulumutsi anaufera. Ziphinjo za wina aliyense zimakhuza mtima wake. Kulira kopempha thandizo kumafikira mmakutu ake. Iye anabwela kuzakokera anthu onse kwa iye yekha. Iye akuwapempha iwo kuti, `ndisatireni ine' ndipo mzimu wake umayendayenda pamitima yawo kuti uwakoke iwo kuti abwere kwa iye. Ambiri amakana kuti akokedwe. Yesu amawaziwa otelewo. Iye amaziwanso iwo amene mwachimwemwe amanva kuitana kwake, Ndipo ndiokonzeka kudza pansi pa chisamaliro chaubusa wake. Iye akuti `Nkhosa zanga zimanva mawu anga, ndipo ine ndimaziziwa izo, ndipo zimandisatira ine.' Iye amasamalira wina aliyense monga ngati kulibenso munthu wina kudziko lapansi." – ***The Desire of Ages, pp. 479, 480.***

**b. Kodi ndi nkhosa zina zotani zimene mwapadera Yesu amaonetsera kukhuzika? Yohane 10:16.**

---

---

"Yesu amalingalira za miyoyo yonse imene ili padziko lapansi imene yasocheletsedwa ndi abusa abodza. Iwo amene iye amafunitsitsa kuti awasonkhanitse monga nkhosa zapabusa pake abalalikana pakati pa mimbulu, ndipo iye akuti `Nkhosa zina ndili nazo, zimene siziri za khola ili; izinso ndiyenera kuzitenga, ndipo zizanva mawu anga; ndipo zidzakhala gulu limodzi, mbusa mmodzi.' Yohane 10:16." – ***Ibid., p. 483.***

"Mulungu ali ndi ngale mumipingo yonse, ndipo sichili kwa ife kumapanga mawu onyoza zamipingo imene ili kudziko lapansi, koma mozichepetsa ndi mwa chikondi, phuzitsani kwa onse choonadi monga chilili mwa Yesu. Lolani anthu kuti aone chifundo ndikuzipereka, lolani iwo aone khalidwe lofanana ndi la Khristu, ndipo iwo azakokeredwa kuchoonadi." ***– The SDA Bible Commentary [E.G. White comments], vol. 4, p. 1184.***

**a. Kodi ndimphanvu yanji yaumulungu imene Khristu analengeza kuti alinayo? Yohane 10:17, 18.**

"'Chifukwa cha ichi Atate andikonda chifukwa nditaya moyo wanga kuti ndikautengeso.' Ndiko kuti, Atate wanga anakukondani kwambiri inu, kuti iye amandikondanso ine kwambiri chifukwa choti ndinapereka moyo wanga kuti ndikupulumutseni inu. Pakukhala mlowammalo ndi chikole chanu, kudzera mukupereka moyo wanga ndikutenga zothodwetsa zanu, zolakwa zanu, ine ndimakondedwa kwambiri ndi Atate wanga.

"'Ndili nayo mphanvu yakuutaya, ndi mphanvu ndiri nayo yakuutenganso; lamulo ili ndinalandila kwa Atate wanga.' Pamene anali monga chiwalo cha banja lamunthu iye anali woti akhoza kufa, monga Mulungu iye anali kasupe wamoyo wadziko lapansi. Iye akanatha kugonjetsa mphanvu za imfa, ndikukana kudza pansi paulamuliro wake; koma mwakufuna mwini iye anasiya pansi moyo wake, kotelo kuti iye akathe kubweletsa moyo ndiumuyaya poonekela. Iye anasenza nchimo ladziko lapansi, kupilira themberero lake, kupereka moyo wake monga nsembe, kuti anthu asazathe kufa kwamuyaya.`Zoonadi iye ananyamula zowawa zathu, ndikusenza zisoni zathu; ….Iye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu, natunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu; chilango chotitengela ife mtendere chinamgwera iye; ndipo ndi mikwingwirima yake ife tachilisidwa.Tonse tasochela ngati nkhosa; tonse tayenda yense mnjira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa iye mphulupulu ya ife tonse.'Yesaya 53:4-6." – ***The Desire of Ages, pp. 483,484.***

**b. Kodi ndi chiyani chimene chimasogolera anthu kuti atsatire Khristu? Yohane 10:27; 1 Yohane 4:10, 19.**

"Simantha oopa chilango, kapena chiyembekezo cha mphoto ya muyaya, zimene zimatsogolera ophunzira a Khristu kuti azimutsatira Iye. Iwo amaona chikondi choposa champulumutsi, chimene chinaonetsedwa mkuyendayenda kwake konse kwa mudziko lapansi, Kuchokera muchodyera cha ng'ombe mu Betelehemu mpaka pa mtanda wakavale, ndipo maonekedwe ake amakopa, ndipo amafewetsa ndikugonjetsa moyo. Chikondi chimadzuka mmutima wa oyang'ana zotelezi. Iwo amanva mawu ake, ndipo iwo amamutsatira Iye." – ***Ibid., p. 480***.

"Ife tikulingalira zamoyo wake padziko lapansi, nsembe yake kwa ife, ntchito yake kumwamba monga otiimilira wathu, ndi nyumba za chifumu zimene iye akukonzera onse amene amamukonda iye, ndipo ife tingathe kufuula basi kuti,Oo kutalika ndi kuya kwa chikondi cha Khristu!" – ***The Acts of Apotsles, p. 334.***

## 5. CHITSIMIKIZO CHA CHIPULUMUTSO

**Lachisanu, Juni 12**

**a. Kodi ndi chitsimikizo chanji chimene Yesu akupereka kunkhosa zake? Yohane 10:28, 29.**

___

___

"Ngakhale tsopano Iye anakwela kumwamba kupita pamaso pa Mulungu, ndikumagawana nawo mpando wachifumu wachilengedwe chonse, Yesu sanataye khalidwe lake lachikondi. Lero mtima womwewo wachifundo, wonvera chisoni ndiosegukira kumabvuto onse a anthu. Lero dzanja limene linakhomedwa latambasulidwa kuti lidalitse modzadza anthu ake amene ali mudziko lapansi 'ndipo sitizaonongeka kunthawi yonse ndipo palibe munthu azazikwatula mzanja langa.' Moyo umene wazipereka okha kwa Khristu ndiwamtengo wapatali kwambiri pamaso pake kupotsera dziko lonse lapansi. Mpulumutsi akanatha kudutsa mumasautso onse akavale kuti moyo umodzi umenewu ukathe kupulumutsidwa muufumu wake. Iye sazataya ingakhale mmodzi waiwo amene iye anawafela. Pokhapokha omutsatila ake asankha kuti amusiye iye, apo ayi Iye azawagwira iwo zolimba. "-The Desire of Ages, pp. 480-483.

**b. Kodi ndi pachiyani pamene chitetezo chathu chauzimu ndichitsimikizo chathu chachipulumutso chagonela? Aroma 8:31-39.**

___

___

"Mmabwalo akumwamba, Khristu akuchondelera za Mpingo wake- kuchonderera za iwo amene iye anapereka mtengo wachiombolo wa mwadzi wake. Zakazaka, mibadwomibadwo, sizingachepetse konse kuthekera kwa nsembe yake yotetezera ngakhale imfa kapena moyo, kutalika kapena kuya, sizingathe kutisiyanitsa ife kuchoka kuchikondi cha Mulungu chimene chili mwa Khristu Yesu; osati chifukwa choti ife tinamamugwira iye zolimba, koma chifukwa choti iye amatigwira ife zolimba kwambiri. Ngati chipulumutso chathu chimadalira mukuyetsetsa kwa ife eni, sitikanatha ife kupulumutsidwa; Koma icho chikudalira mwa iye amene ali kuseli kwa malonjezo onse. Kumugwira kwathu iye kukhoza kuoneka kofooka, koma chikondi chake ndi chonga cha m'bale wamkulu; pokha pamene ifeyo tikupitiliza mgwirizano wathu ndiiye, palibe wina aliyense amene angatikwatule ife kuchoka mmanja mwake." – ***The Acts of Apostles, pp. 552,553.***

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

**Lachisanu ndi chimodzi, Juni 13**

1. Fotokozani kusiyana kwa machitidwe pakati pa mbusa ndi wokuba?
2. Ndikudzera muchizindikiro china chanji chimene Yesu akuzifotokoza yekha?
3. Kodi ndi motani mmene amachitila abusa oona ndi nkhosa zawo?
4. Kodi ndi chifukwa chiyani nkhosa zimasatira mbusa osati mlendo?
5. Fotokozani mmene ife tingakhalire otsimikizika zachipulumutso?

# YESU NDI LAZALO

**VESI LOLOWEZA: "Imfa ya okondedwa ake nja mtengo wake pamaso pa Yehova" (Masalmo 116:15). Zowelenga zoonjezera: The Ministry of Healing, pp. 219-228.**

**Owerenga zoonjezera: The ministry of healing, pp. 219 – 224**

**"Mwa khristu muli moyo, weniweni, osabwerekedwa, osachokera kwina … Umulungu wa Khristu ndi chitsimikizo cha okhulupirira cha moyo wamuyaya." – The Desire of Ages, p. 530.**

## 1. BANJA LA KU BETANIYA

**Loyamba, Juni 15**

**a. Kodi ndi ophunzira anji amene Yesu anali nawo mu mzinda wa Betaniya? Yohane 11:5.**

______________________________________________

______________________________________________

"Mtima wa Khristu unamangililika ndi chingwe champhavu cha chikondi ndi banja la ku Betaniya ndipo kwa mmodzi wa iwo ntchito yake yodabwitsa kwa mbiri inachitidwa.

"Ku nyumba kwa Lazalo, kawirikawiri Yesu amapezako mpumulo. Mpulumutsi analibe nyumba yakeyake Iye amadalira chisamaliro cha abwenzi ndi ophunzira ake, ndipo kawirikawiri akatopa, akakhala ndi ludzu chiyanjano cha umunthu, amakondwera kuthawira kunyumba ya bata imeneyi, kutali ndi kukayikira ndi nsanje ya Afarisi amkwiyo. Kumeneku Iye anapedza kulandilidwa koona, ubwenzi woyera ndi wangwiro. Kumeneku Iye amatha kuyankhula mwa ufulu, podziwa kuti mawu ake akhoza kumvetsetsedwa ndi kuyamikilidwa." – ***The Desire of Ages, p. 524.***

**b. Kodi ndi pa khomo pamtundu wanji pamene Mulungu amapezeka ndi madalitso ake apadera? Miyambo 3:33(mbali yomaliza).**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

"Mpulumutsi wathu amayamikira banja labata ndi omvetsera achidwi. Iye amafuna chikondi, chisamaliro ndi chifundo cha umunthu. Iwo amene alandira langizo la kumwamba limeneiye amakhala nthawi zonse wokonzeka kupereka amakhala odalitsidwa kwakukulu." – ***Ibid.***

**a. Kodi ndi chiyani chimene alongo ake a Lazalo anachita pamene mlongo wawo anadwalika kwambirinanga ndi yankho lanji limene iwo analilandira? Yohane 11:1-4.**

---

---

"Lazaro anadwala mwazizizi, ndipo alongo ake anatumiza uthenga kwa mpulumutsi, nanena, ambuye onani amene mumkonda adwala.' Iwo anaona kuipitsitsa kwa nthenda imene inagwira mlongo wawo, koma amadziwa kuti Khristu anazionetsera yekha kutha kuchilitsa nthenda iliyonse. Iwo amakhulupirira kuti iye awamvera iwo chisoni mukusausika kwawo. Chotelo iwo sanapemphe kupezeka kwake kwa pompopompo, koma anangomutumizira uthenga wachidaliro woti, 'Iye amene inu mumkonda adwala.' Iwo anaganiza kuti iye akhoza kuyankha mwachangu kuuthenga wawo, ndi kubwela kudzakhala nawo mwamsanga pompopompo akangofika ku Betaniya.

"Mwa chidwi iwo anadikirira mawu ochokera kwa Yesu. Nthawi zonse pamene moyo unalipo mwa mlongo wawo, Iwo amapemphera ndi kuyang'anira koma mnthenga anabwerera opanda Iye. Koma anangobweretsa uthenga oti `kudwala kumene sikuli kwa imfa,' ndipo iwo anakakamira kuchiyembekezo choti Lazalo akhala ndi moyo. Mwachikondi iwo amayesera kuyankhula mawu a chiyembekezo ndi chilimbikitso kwa odwala wodwalikayu." – ***The Desire of Ages, pp. 525,526.***

**b. Fotokozani mawu ndi machitidwe a khristu patangopita masiku ochepa. Yohane 11:5-8.**

---

---

---

"kwa masiku awiri Khristu amaoneka ngati wachotsa uthenga uja mu malingaliro ake; popedza iye sanayankhule za Lazalo. Ophunzira analingalira za Yohane m'batizi, wokonza njira ya Yesu. Iwo amadabwitsika kuti ndi chifukwa chiyani Yesu, ndi mphanvu za kuchita zozizwa yodabwitsa analolera kuti Yohane abvutike mundende, ndi kufa imfa yankhaza. Pokhala nazo mphanvu zotere, kodi ndi chifukwa chiyani Khristu sanapulumutse moyo wa Yohane? Funso limeneli kawirikawiri limafunsidwa ndi Afarisi amene amalipereka ilo ngati msunso wosayankhika wosusa kuzinena kwa Khristu koti ndi mwana wa Mulungu. Mpulumutsi anachenjeza ophunzira ake za mayesero, kuluza zinthu, ndi zisautso.

Kodi iye azawasiya iwo mmayesero? Ena amakhala ndi mafunso ngatidi iwo alakwitsa utumiki wake. Onse anasausika mumtima kwakukulu…

"Ophunzira anafunsa chifukwa chiyani ngati Yesu amapita ku Yudeya, iye wadikira matsiku awiri. Koma nkhawa za kwa khristu ndi za kwa iwo eni zinali zambiri mmitima yawo. Iwo samaonanso china chilichonse koma choopsa muulendo umene iye amafuna kuuyenda." – ***Ibid., pp. 526, 527.***

## 3. CHOKHUMUDWITSA CHISANDULIKA CHIYEMBEKEZO — Lachitatu, Juni 17

**a. Kodi ndi uthenga wanji wopanda nthawi umene ife tingaugwiritsise kuchokera ku mmene Khristu anachitira ndi zotsatira zosokonezeka za zinthu zimene zinazungulira kudwala kwa Lazalo? Yohane 11:9, 10.**

---

---

---

"Iwo amene anakhalapo ogwira ntchito limodzi ndi Khristu, koma amakana amithenga ndi uthenga wawo, azagwa ndi kutaya kulimbika kwawo. Iwo azayenda mumdima osadziwa pamene agwera, oterewa ndi okonzeka kunyengedwa ndi zinyengo za mmasiku otsiriza. Malingaliro awo azazidwa ndi zinthu zazing'onozing'ono, ndipo iwo amaluza mwayi wodalitsika wa kuvala goli ndi Khristu, ndi kukhala ogwira ntchito limodzi ndi Mulungu."- ***Fundamentals of Christian Education, p. 471.***

**b. Kodi ndi bvumbulutso lanji lodabwitsa limene Yesu analipereka kwa ophunzira ake komabe kodi ndi motani mmene iwo anatanthauzira mawu ake? Yohane 11:11, 12.**

---

---

---

"'Izi anati, ndipo zitatha izi ananena nawo, Lazalo bwenzi lathu ali m'tulo, koma ndimuka kukamuukitsa Iye ku tulo take.' 'Bwenzi lathu ali mtulo,' kodi ndi mawu okhuza bwanji! Ozaza bwanji ndi chisoni! Ndi lingaliro la chiopsyezo chomwe Mbuye wawo amati akakumane nacho akapita ku Yerusalemu, ophunzira anaiwalira za banja losausika la ku Betaniya. Koma sizinali choncho kwa Khristu. Ophunzira anamva kuzuzulika. Iwo anakhumudwitsika chifukwa Khristu sanayankhe mwachangu ku uthenga. Iwo anayesedwa kuti azilingalira kuti Iye analibe chikondi chachikulu kwa Lazaro ndi alongo ake chimene iwi amaganiza kuti ali nacho,apo ayi Iye akanatha kubwerera mwachangu ndi mthenga. Koma mawu oti, 'bwenzi lathu Lazaro ali mtulo,' Unazusa malingaliro oyenera mu mitima yawo. I anakhulupirira kuti Khristu sanaiwalire abwenzi ake osausika." – ***The Desire of Ages, p. 527.***

**c. Fotokozani chimene mawu a Khristu amatanthauza kwenikweni? Yohane 11:13, 14.**

---

---

---

"Khristu amaonetsera imfa ngati kugona tulo kwa ana ake okhulupirira. Moyo wawo wabisidwa mwa Khristu kwa Mulungu, ndipo kufikira lipenga lomaliza lizalire iwo amene anafa azagona mwa iye." – ***Ibid.***

## 4. KUDIKILA, KUDIKILA, KUDIKILA

**Lachinayi, Juni 18**

**a. Kodi ndichifukwa chiyani Yesu sanapite kuBetaniya ngakhale ataziwa kuti Lazalo wamwalira? Yohane 11:15.**

---

"Ophunzira anadabwa pamawu a Khristu pamene iye anati, 'Lazalo wamwalira. Ndipo ndikondwera ….Kuti kunalibe ine komweko.' Kodi mpulumutsi kudzera muchisankho cha Iye mwini anapewa khomo la abwenzi ake osausika? Moonekera Mariya ndi Malita ndi Lazalo amene anali pafupi kufa anasiidwa okha. Koma iwo sanali okha. Khristu amaona zochitika zonse, Ndipo atamwalira Lazalo, azilongo okhuzikawo analimbikitsidwa kudzera muchifundo chake. Yesu anachitila umboni nkhawa ya mitima yawo yosweka, pamene mlongo wawo amalimbana ndi mdani wake wamkulu, imfa. Iye amanva muntima kusautsika kwinakulikonse, pamene iye anati kwa ophunzira ake, 'Lazalo wamwalira.' koma Khristu sanali ndiokondedwa okhawa ku Betaniya kuti azilingalira za iwo okha; Iye ali ndi lingaliro lakuphunzitsa ophunzira ake. Iwo akuyenera kudzakhala omuimilirako iye kudziko lapansi, kotelo kuti mdalitso wa Atate ukathe kuwafikira onse. Chifukwa cha iwo iye analorera Lazalo kuti afe. Ngati iye anakamuchilitsa iye kuchokera kunthenda yake kuti akhale wathanzi, chozizwitsa chimene ndiumboni wamphanvu kwambiri wakhalidwe lake la umulungu, sichikanachitidwa." – ***The Desire of Ages, p. 528.***

**b. Kodi ndi chiyani chimene ife tikuyenera kuzindikira kudzera mu njira imene mchilitsi wamkulu analorela Lazalo bwenzi lake, kuti adwale kwambili ndikufadi? 1 Akolinto 15:17-19; Masalimo 18:28.**

---

---

"Ntchito ya Khristu siinaimile poonetsera mphanvu zake pamatenda. Iye anapanga ntchito iliyonse yakuchilitsa kukhala chochitika chakudzalira mumtima mfundo za Umulungu zachikondi ndi kuzipeleka kwake." – ***Counsels on Health, p. 249.***

"Ngati Khristu anakakhala mchipinda chimene Lazalo amadwalira, Lazalo sakanafa; pakuti Satana sakanakhala ndi mphanvu pa iye. Imfa sikanaika mivi yake pa Lazalo pamaso pa opereka moyo. Chotelo Khristu sanapiteko kumeneko iye analorera kuti mdani achite mphanvu zake, kotelo kuti iye akathe kumuthamangitsa iye, mdani ogonjetsedwa. Iye analorela Lazalo adutse kupyola mumphanvu zaimfa; ndipo alongo osautsika anaona mlongo wawo akuikidwa mmanda. Khritsu anadziwa kuti pamene iwo akuyang'ana pankhope yokufa yamlongo wawo chikhulupiliro chawo mwa mombolo wawo chiyesedwa kwakukulu. Koma iye anaziwa kuti chifukwa cha mikwingwirima imene iwo tsopano akudutsamo tsopano chikhulupiliro chawo chizawala ndi mphanvu zazikulu. Iye analolera nkhawa yamtundu wina ulionse imene iwo anadutsamo. Iye amawakonda iwo osati mochepelako chifukwa chake iye anachedwa; koma iye amadziwa kuti chifukwa cha iwo, chifukwa cha Lazalo, chifukwa cha iye mwini, ndi chifukwa cha ophunzira ake, chipambano chizapezedwa." – ***The Desire of Ages, p. 528.***

## 5. SITI NTHAWI ZONSE MONGA IFE TIKUYEMBEKEZERA — Lachisanu, Juni 19

**a.** Kodi ndi chiyani chimene nthawi zonse tikuyenera kumachilingalira zokhuzana ndi imfa ya akapolo okhulupirika a Mulungu, posatengela mmene yachitikira? Masalmo 116:15. Pelekani chisanzo.

---

---

---

"Sichinapelekedwe kwa Elisa kuti asatile Mbuye wake mugaleta wamoto. Pa iye Ambuye analorera kuti pabwele nthenda yokhalitsa. Munthawi yaitali yakufooka ndi kusautsika kwa umunthu chikhulupiriro chake chinagwira zolimba pamalonjezo a Mulungu. Ndipo iye nthawi zonse amaona pozungulira pake amithenga akumwamba achitonthozo ndi mtendere…. Chikhulupiriro chinakwhima kufikira muchidaliro chokhazikika mwa Mulungu wathu, ndipo pamene imfa inamuitana iye anali wokonzeka kupumula kuchoka kuntchito yake." ***– Prophets and Kings, pp. 263, 264.***

**a. Kodi ndizochitika zanji zimene zinachitika kuBetaniya asanafike Yesu-Nanga ndi ndani ena amene analikonso pamene iye anabwera? Yohane11:17-19.**

---

---

---

"Mukuchedwa kupita kwa Lazalo, Khristu anali ndi cholinga chachifundo pa iwo amene sanamlandile iye. Iye anachedwa, kuti kudzera mukuukitsa Lazalo kuchokela kuimfa iye akathe kupeleka kwa anthu ake ouma mtima, osakhulupilira umboni wina kuti iye moonadi 'ndikuuka, ndimoyo.' Iye samafuna kutaya chiyembekezo chonse pa anthu, osauka, nkhosa zosochera zanyumba ya Israeli. Mtima wake umasweka chifukwa cha kusakhulupirira kwawo. Muzifundo zake iye analingalira zakuwapatsa iwo umboni waukulu woti iye ndiobwezera moyo, iye amene ndiyekha amene angathe kubweletsa moyo poonekera. Uwu ukhala umboni woti ansembe sangathe kuutanthauzira mwa bodza. Ichi ndi chifukwa cha kuchedwa kwake kupita ku Betaniya. Chozizwa ichi choposa zozwizwitsa zonse, kuukitsa kwa Lazalo, kunaika chizindikiro cha Mulungu kuntchito yake chakuzinena kwake kokhala ndi umulungu."- The Desire of Ages, p. 529.

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu ndi chimodzi, Juni 20

1. Kodi ndi ndani amene anali abanja la Lazalo?
2. Kodi ndichifukwa chiyani Yesu pompo sanayankhe pempho la abwenzi ake?
3. Kodi ophuzira analingalira chiyani kukhalidwe la Khristu?
4. Kodi ndimotani mmene imfa ikuyenera kutengeledwa ndi okhulupirira mwa Khristu?
5. Ndichifukwa cha cholinga chanji kuti Khristu analorela Lazalo kuti afe?

SABATA, JUNI 28, 2025

PHUNZIRO 13

# KUUKA NDI MOYO

**Vesi Loloweza: “Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo: wokhulupirira ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo” (Yohane11:25).**

**Zowelenga zoonjezera: Selected Messages, bk. 1, pp. 296-300.**

**“Kwa okhulupirira imfa ndi nkhani yaing’ono chabe. Yesu Khristu akunena za iyo ngati yakanthawi kochepa chabe ….kwa Mkhristu, imfa ndi tulo, kamphindi ka bata ndi mdima. Moyo unabisidwa mwa Khristu kwa Mulungu.” – The Desire of Ages, p. 787.**

## 1. YESU MU BETANIYA

**Loyamba, Juni 22**

**a. Atamva kuti Yesu akubwera ku Betaniya, kodi ndi chiyani chimene Malita anachita nanga ndikukhuzika kwanji kumene iye anakufotokoza? Yohane 11:20-22.**

---

“Pakati pa abwenzi amene amalira panalinso achibale abanjali, ena mwa iwo anali ndi maudindo apamwamba kwambiri mu Yerusalemu. Pakati pa amenewa panali ena mwa adani kwambiri a Khristu. Khristu anaziwa zolinga zawo, ndipo chotelo iye sanazionetsere yekha mwachangu. Uthenga unaperekedwa kwa Malita mwakachetechete kotelo kuti ena muchipindamu sanamve…

“Malita anafulumira kuti akakumane ndi Khristu, mtima uli wosausika ndi malingaliro otsutsanatsusana. Pa maonekedwe apankhope pake iye anawelenga chifundo ndi chikondi chimene nthawi zonse chakhala chili pamenepo. Chidaliro chake mwa Iye sichinaonongeke, koma iye amalingalira za mchimwene wake wokondedwa kwambiri, amene Yesuso amamukonda. Ndinkhawa imene imakula mumtima mwake chifukwa Khristu sanabwele mmbuyomu, komabe ndi chiyembekezo choti ingakhale tsopano iye angathe kuchita chinachake choti awatonthoze iwo, iye anati ‘Ambuye, mukadakhala kuno mlongo wanga sakadafa. Kawiri ndi kawiri, pakati pa phokoso limene limapangidwa ndi olira, alongowa anakhala akubweleza mawu amenewa.

“Ndi chisoni chaumunthu ndi umulungu Yesu anayang’ana pankhope pake pachisoni ndi podzazidwa ndi nkhawa. Malita analibe khumbo lakulankhula zambuyo; zonse zimafotokozedwa kudzera mmawu okhuza kwambiri oti, ‘Ambuye, mukadakhala kuno mlongo wanga sakadafa.’ Koma poyang’ana pankhope paja yachikondi, iye anaonjezera kunena kuti, ‘ndiziwa kuti ngakhale tsopano, zinthu zilizonse mukapempha Mulungu, azakupatsani inu.’ ” – ***The Desire of Ages, pp. 529, 530.***

## 2. LONJEZO LAPOMPOMPO LACHIYEMBEKEZO — Lachiwiri, Juni 23

**a. Ndizachiyani zimene Yesu anamusimikizira Malita? Yohane 11:23. Kodi ndi chiyani chimene iye anachizindikira kudzera muchimenechi? Yohane 11:24.**

"Yesu analimbikitsa chikhulupiriro chake, ponena kuti, 'Mlongo wako azauka.' Yankho lake silinaperekedwe ndi cholinga choti libweletse chiyembekezo chakusintha mwachangu. Iye anatengela malingaliro a Malita kupyola kubwezeletsedwa kwapanopo kwa mlongo wake, ndikuwakhazikitsa iwo pa mzukiro pa kuuka kwa anthu olungama. Ichi anachita Iye kotelo kuti iye akathe kuona kukuukitsidwa kwa Lazalo lonjezo lakuuka kwa olungama onse amene anafa, ndi chitsimikizo choti kuzakwanilitsidwa kudzera mumphanvu za Mpulumutsi. Malita anayankha kuti, 'ndikuziwa kuti adzauka mkuuka tsiku lomalidza.'" – ***The Desire of Ages, p. 530.***

**b. Ndipamawu anji amene Yesu anabvomeledza chikhulupiliro cha Malita? Yohane 11:25; 1 Yohane 5:12.**

"Pofunitsitsabe kuti apeleke chitsogozo choona kuchikhulupiriro chake, Yesu ananena kuti, 'ine ndine kuuka ndi moyo.' Mwa Khristu muli moyo, weniweni, osabwelekedwa, osachokera kwina. 'Iye amene ali ndi mwana ali nawo moyo.' 1Yohane 5:12. Umulungu wa Khristu ndichitsimikizo chaokhulupirira cha moyo wosatha." – ***Ibid.***

**c. Kodi ndi lonjezo lanji limene lili madziko achiyembekezo chathu kupyola manda, Nanga kodi ndimotani mmene chikhulupiliro cha Malita chikugwirizana ndi chozizwa cha Khristu? Yohane 5:26; 11:26, 27.**

"Apa Khristu akuyang'ana chitsogolo kunthawi yakubwera kwake kwachiwiri. Pamenepo wolungama wokufa azaukitsidwa osavunda, ndipo olungama amoyo azasinthidwa kupita kumwamba popanda kuona imfa. Chozizwa chimene Khristu anali pafupi kuti achichite, mukuzutsa Lazalo kuchokera kwaakufa, kuzaimilira kuukitsidwa kwa olungama onse okufa. Kudzera mmawu ake ndi munchito zake iye anazilengezetsa iye yekha kuti ndi mwini wake wakuuka kwa kufa. Iye amene mwini wake posachedwa anali kuti afa pamtanda anayima ndi makiyi aimfa ogonjetsa wamanda, ndikusimikizira za kuyenera ndi mphanvu zake zakupereka moyo wosatha." – ***Ibid.***

## 3. YESU ALIRA

**Lachitatu, Juni 24**

**a. Fotokozani machitachita ndi mawu a Mariya ogwidwa ndi chisoni. Yohane 11:28-32.**

**b. Pamene Yesu anaona Mariya ndi Ayuda ena akulira, kodi ndi chiyani chimene Yesu anachita-ndipo chifukwa chiyani? Yohane 11:33-35.**

"'Pamenepo Yesu pakumuona iye akulira, ndi Ayuda akumperekeza iye akulira, anazuma muuzimu, nabvutika mwini.' Iye anawelenga mitima ya anthu onse amene anasonkhana. Iye anaona kuti kwa ambiri, chimene chimaonetseredwa ngati chisoni chinali kunamizira chabe. Iye anaziwa kuti anthu ena pagulupa, amene tsopano akuonetsera chisoni cha chinyengo, posachedwapa akhala akukonza madongosolo akupha, osati ochita chozizwa chachikulu yekha basi, komanso aiye amene atadzusidwe kuchokera kuimfa. Khristu akanatha kubvula kuchokera kwa iwo mikanjo yawo yachisoni chabodza. Koma iye anabweza mkwiyo wake wachilungamo. Mawu amene mwachilungamo chonse akanatha kuwanena, iye sanawanene, chifukwa cha okondedwa amene anagwada pamapadzi ake mwachisoni, amene moonadi anakhulupilira mwa Iye.

"`Mwamuika iye kuti?' Iye anafunsa, 'ananena ndi iye, Ambuye tiyeni mukaone.' Limodzi iwo anayenda kupita kumanda. Chinali chochitika cholilitsa. Lazalo anali okondedwa kwambiri, ndipo adzilongo ake anamulirira iye ndimitima yotsweka, Pamenenso iwo amene anali abwenzi ake anasakanidza misodzi yawo ndi ya alongo ake achisoni. Poona kutsautsika uku kwa umunthu, ndichoona choti abwenzi otsautsikawa akhoza kulirira wokufa wawo pamene mpulumutsi wadziko lapansi akuima pomwepo- `Yesu analira.' Ngakhale iye anali mwana wa Mulungu, komabe iye anatenga khalidwe la umunthu pa

Iye, ndipo iye anakhuzika ndi chisoni cha umunthu. Mtima wake wachifundo, wachisoni nthawi zonse umazutsidwa ku chisoni kudzera mu kuvutika. Iye amalira limodzi ndiiwo amene akulira, ndikukondwa ndiiwo amene akukondwa." – ***The Desire of Ages, p. 533.***

**c. Kodi ndi motani mmene nthawi imeneyi mumoyo wa Khristu ingakhalire chisanzo kwa ife? Aroma 12:15.**

"Chisanzo chodabwitsa cha Khristu, chifundo chosafanizilika chimene pamodzi nacho iye amalowela muzokunva mumtima za ena, kulira ndiiwo amene akulira, kukondwa ndiiwo amene akukondwa zikuyenera kukhala ndi chikoka chakuya pakhalidwe la onse amene amamutsatila iye moonadi. Kudzera mumawu ndi ntchito zachifundo iye azayetsetsa kupanga njira yophweka yamapadzi otopa." – ***The Ministry of Healing, pp. 157,158.***

## 4. MGWIRIZANO PAKATIKA MULUNGU NDI UMUNTHU — Lachinayi, Juni 25

**a. Kodi ndikulamula kwanji kumene Yesu anakupereka kwa iwo amene anamuzungulira iye? Yohane 11:39(mbali yoyamba).Kodi ndi motani mmene Malita anayankhira ndipo ndi chiyani chimene Yesu anayankhula kwa iye? Yohane 11:39 (mbali yomaliza).**

---

---

"Pamene Ambuye alipafupi kuti achite ntchito inayake, Satana amayenda pa wina wake kuti atsutse. 'chotsani mwala,' Khristu anatelo. Monga mmene mungathele, konzani njira ya ntchito yanga. Koma khalidwe la chibadwa lamatama ndi lozionetsera la Malita linazikweza lokha. Iye sanafune kuti thupi lobvundalo libweletsedwe kuti lionedwe. Mtima waumunthu ndi ochedwa kuzindikira mawu aKhristu, ndipo chikhulupiliro cha Malita sichinamvetsetse tanthauzo lenileni la lonjezo lake.

"Khristu anamudzuzula Malita, koma mawu ake anayankhulidwa modekha kwambiri. 'Sindidati kwa iwe, ngati ukhulupirira uzaona ufumu wa Mulungu?' Kodi ndi chifukwa chiyani ukuyenera kukaikira zokhuzana ndi mphanvu zanga? Kodi chifukwa chiyani ukulingalira motsutsana ndi zofuna zanga? Ndanena mawu anga. Ngati iwe uzakhulupirira, udzaona ulemerero wa Mulungu. Zosatheka mwa chilengedwe sizingathe kuletsa ntchito ya opanda malire. Kukaikira ndi kusakhulupirira sikuzichepetsa. Kukhulupirira mwa ndendende mumawu a Khristu ndiko kudzichepetsa koona, kuzipereka wekha koona.

"'Chotsani mwala.' Khristu akanatha kulamulira mwala kuti uchoke, ndipo iwo ukanatha kumvera mawu ake. Iye akanatha kulamulira angelo amene anali pafupi pambali pake kuti achite chimenechi. Pakulamula kwake, manja osaoneka akanatha kuchotsa mwala. Koma iwo umayenera kuchotsedwa ndi manja aumunthu. Mukutelo Khristu amaonetsera kuti umunthu ukuyenera kugwirizana ndi umulungu. Chimene mphanvu za umunthu zingathe kuchita mphanvu za umulungu sizimaitanitsidwa kuchichita.Mulungu samanyozera thandizo la Munthu. Iye amamulimbikitsa iye, kugwira ntchito limodzi ndi iye, pamene iye akugwiritsa ntchito mphanvu ndi kuthekera zimene iye anapatsidwa." –The Desire of Ages, p. 535.

**b. Kodi ndimawu anji a Khristu amene modekha akudzudzula kusakhulupirira kwathu lero? Yohane 11:40.**

---

"Ambiri alibe chikhulupiriro cha moyo. Ichi ndi chifukwa chake iwo samaona zambiri zamphanvu ya Mulungu. Kufooka kwawo ndichotsatira cha kusakhulupirira kwawo…Iwo amakonza madongosolo ndikuwachita, koma amapemphera pang'ono, ndipo ali ndi chidaliro chochepa chenicheni mwa Mulungu. Iwo amaganiza kuti ali ndi chikhulupiriro,koma ndikuzizimuka chabe kwa kanthawi. Polephera kuzindikira chosowa chawo, kapena khumbo la Mulungu lakupereka, iwo samapilira mukuika zopempha zawo pamaso pa Mulungu." – ***Christ's Object Lessons, pp. 145,146.***

## 5. YESU AUKITSA LAZALO — Lachisanu, Juni 26

**a. Kodi ndi pemphero lanji limene Yesu analipereka pambali pa manda? Yohane 11:41, 42.**

---

"Kulamula kunamveredwa. Mwala wachosedwa. Chinachilichonse chikuchitidwa pambalambanda komanso ndi cholinga. Onse apatsidwa mwayi kuti awone kuti palibe chinyengo chilichonse chimene chikuchitidwa. Thupi la Lazalo ilo lagona potelopo mmanda amwala, lozizila ndi lachete muimfa. Kufuula kwa olira kwalekeka. Odabwisika ndi oyembekezera, gulu lonse linaima mozungulira manda, kuyembekezera kuti aone chimene chingasatire…

"Apa khristu akunena Mulungu monga Atate wake, ndipo ndichidaliro chozaza akunena kuti iye ndi mwana wa Mulungu." – ***The Desire of Ages, p. 535, 536.***

**b. Ndimawu anji amene Yesu anazutsira Lazalo? Yohane 11:43.Kodi ndichiyani chimene chinachitika pompopompo? Yohane 11:44**

---

"Mawu akhristu,omveka bwino ndi opyoza, analowa mukhutu laokufa. Pamene iye amalankhula, Umulungu unawala kudzera mumunthu. Pankhope pake, pamene panawalisidwa ndi ulemerero wa Mulungu, anthu anaona chisimikizo cha mphanvu zake. Diso linalililonse linayang'anitsitsa pakhomo lamphanga lamanda. Khutu linalililonse linachela kuti linvesele liwu lina lililonse. Ndichidwi chachikulu komanso chopweteka onse anadikilira yetsero la umulungu la Khristu, umboni umene ungasimikizire kuzinena kwake koti ndi mwana wa Mulungu, kapena woti ufufute chiyembekezo kwa muyaya.

"Panamveka ngati kukuyenda munthu mumanda achete, ndipo iye amene anali wakufa anaima pakhomo lamanda… Umunthu ukuyenela kugwilila ntchito umunthu. Lazalo wamasulidwa zomangila, ndipo waima pamaso pa gulu limene linasonkhanalo, osati ngati munthu ochilitsidwa kumatenda, okhala ndi thupi lofooka, oonekela nthiti, koma monga munthu wathanzi lachikhalire, munthu wamphanvu zake olemekezeka. Maso ake anawala ndi nzeru ndi chikondi kwa mpulumutsi wake. Iye anazigwetsa mwini yekha mukupembeza pamapazi a Yesu." – ***Ibid., p. 536.***

## 6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu ndi chimodzi, Juni 26

1. Fotokozani chidaliro chimene azilongo ake a Lazalo anali nacho mwa Yesu?
2. Kodi ndi chiyani chimene Yesu anachilonjeza kwa Malita, kwa Mariya ndi kwa okhulupirira wina aliyense?
3. Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu analira?
4. Kodi ndi motani mmene umunthu unagwirira ntchito limodzi ndi umulungu muchozizwa chimenechi?
5. Fotokozani machitidwe a Lazalo Yesu ataitana?

# Chopereka cha Sabata Loyamba




## Sabata Epulo 5

**Kumanganso kwa chalichi ku** Prokhorovka, Russia

Khalani mbali ya nchito imene ikukula mu driko lokulisa padriko lonse lapansi.
(Onani p. 4).



## Sabata Meyi 3

Mathumiki akudriko lapansi

Kuli malo atsopano ambiri ofunika kupitako,chomcho tiyeni titandizire kumaliritsa kwa nchito ya Mulungu!
(Onani p. 24).




## Sabata Juni 7

Mipingo iwiri ku Tamil Nadu, India
South India ili ndi kusowa kwa kukulu kwa athanga waltwimo; tsopano ndi nthawi wathu kutandizira kumutha zimbo (Onani p. 46)